

Machitidwe a Mulungu Wathu Wofatsa

Kuwunika Kwaulemerero kwa Tsiku
Latsopano pa Khalidwe la Mulungu

Jay A. Schulberg



Machitidwe a Mulungu

Wathu Wofatsa

Kuwunika Kwaulemerero kwa Tsiku

Latsopano pa Khalidwe la Mulungu

Mlandu wa Mulungu Wopanda Chiwawa:

Kafukufuku Wotsutsa Maganizo Olakwika Ponena

za Mulungu ndikupatsanso

Maganizo Olimbikitsa

Jay A. Schulberg

Kukopera © 2017 Jay A. Schulberg

Mau wonse a mwini wake ndi otetezedwa. Palibe gawo lililonse la bukuli lomwe lingagwiritsidwe ntchito kapena kusindikizidwanso mwa njira iliyonse, zojambulajambula, zamagetsi, kapena zamakina kuphatikiza kukopera, kujambula, kapena kugwiritsa ntchito mwa njira iliyonse yosungira zinthu popanda chilolezo cholembe kwa wolembe kupatula ngati mawu womwe atchulidwa mwachidule zolembe zowunikira komanso zobweleza.

Wosindikiza ndi



Tatewachikondi.com

June 2019

M'ndandanda Wazopezekamo

| | |
|--|-----|
| Kodi Munayamba Mwadzifunsapo? | 7 |
| Mutu 1. Kodi Ziridi Zofunika? | 9 |
| Mutu 2. Chitsanzo Chathu Changwiro..... | 11 |
| Mutu 3. Gwero Lathu La Moyo | 13 |
| Mutu 4. Kupangidwa M'chifanizo Chake..... | 15 |
| Mutu 5. Wonyenga Wamkulu | 17 |
| Mutu 6. Kodi Tchimo Ndi Chiyani? | 19 |
| Mutu 7. Nchifukwa Chiyani Pali Mdierekezi? | 22 |
| Mutu 8. Njoka Yowononga | 29 |
| Mutu 9. Kugwidwa Kwa Yobu..... | 32 |
| Mutu 10. Chifukwa Chake Timawerenga Baibulo Molakwika..... | 38 |
| Mutu 11. Chifukwa Chake Sitimamumvetsa Mulungu..... | 40 |
| Mutu 12. Momwe Mulungu Amawonongera | 45 |
| Mutu 13. Kodi Ukali Wa Mulungu N'chiyani? | 47 |
| Mutu 14. Momwe Mulungu Amamenyera Nkhondo | 59 |
| Mutu 15. Sodomu Ndi Gomora..... | 62 |
| Mutu 16. Nanga Bwanji Chigumula?..... | 65 |
| Mutu 17. Umboni wa Mtanda | 71 |
| Mutu 18. Mulungu Sali Wankhanza | 73 |
| Mutu 19. Mlengi wathu ndi Wotisamalira | 82 |
| Mutu 20. Titha Bwanji Kukhala Ndi Moyo Wamuyaya?..... | 88 |
| Mutu 21. Tiyenera Kuopa Chiweruzo? | 95 |
| Mutu 22. Kodi Chiweruziro cha Mulungu Chimawoneka Motani? | 104 |
| Mutu 23. Mulungu Ndi Wodzichepetsa | 109 |
| Mutu 24. Mulungu Ndi Wantchito, Osati Mbuye Wa Kapolo | 112 |
| Mutu 25. Mulungu Amakukondani Mosasamala..... | 115 |
| Mutu 26. Ufumu wa Mulungu | 117 |
| Mutu 27. Mulungu Amatipatsa Ufulu Weniweni..... | 122 |
| Kuphatikizira | 126 |

Mawu Oyambirira

Kodi Munayamba Mwadzifunsapo?

M'chilankhulo chachilamulo, tsoka lomwe limachitika chifukwa cha mphamvu zachilengedwe zosaletsetseka limatchedwa kuti zochitika za Mulungu. Mawuwa nthawi zambiri amaphatikizidwa ndi ndondomeko za ma inshuwaransi. Kodi tinalitenga kuti lingaliro lakuti Mulungu amachititsa zoipa zonse zimachitika m'dziko lathu? Kodi amangosankha mwadala liti kapena m'malo komwe zinthu monga mphepo zamkuntho, zivomerezi, mikuntho, kusefukira kwa madzi, ndi matsoka ena achilengedwe akachitika? Kodi Mulungu amachita china chilichonse kuti izi zichitike? Kodi amagwiritsa ntchito chilengedwe kuti akwaniritse zomwe amafuna? Ndipo nchifukwa ninji sachita zambiri kuti athetse mavuto padziko lapansi? Pomaliza, kodi ndi Mulungu amene anachititsa zachiwawa tikawerenga m'Baibulo? Kodi nayenso anayamba kuchita zachiwawa?

Baibulo limayankha mafunso amenewa, koma tiyenera kuyang'ana pansu kuti tipeze mayankho ake. Tiyeneranso kukhala ofunitsitsa kumva zomwe Mulungu akunena za iye komanso momwe amagwirira ntchito ngakhale zitakhala zovuta zomwe timakhulupirira za Iye. Bukuli liziwunika za khalidwe la Mulungu monga zawululidwa m'Baibulo – zochitika zake ndipo, koposa zonse, zomwe sizili. Ambiri amakhulupirira kuti Mulungu amatikonda tikalola malamulo ake koma amakwiya ndi zolakwa ndikulanga iwo amene amatsutsana ndi malamulo ake. Cholinga cha phunziroli ndikuwonetsa kuchokera m'Baibulo kuti Mulungu sanachitepo zowononga koma monga Mlengi, Wosamalira, ndi Mpulumutsi.

Koma nzeru yocokera kumwamba iyamba kukhala
yoyera, nikhalanso yamtendere, yaulere, yomvera
bwino, yodzala cifundo ndi zipatso zabwino,
yopanda tsankhu, yosadzikometsera pamaso.

— Yakobo 3:17

Kodi Ziridi Zofunika?

Chifukwa chiyani kuli kofunika kudziwa momwe Mulungu alili? Kodi pali kanthu pa zomwe timaganiza za Mulungu? Kodi zilibe kanthu ngati timaganizira za Iye konse? Mayankho a mafunso awa ali pachiyambi cha chilichonse chomwe tiyenera kudziwa. Zomwe timakhulupirira za Mulungu ndi chikhalidwe chake zimatsimikizira momwe timakhalira – ndipo chikhalidwe chathu nchofunika kwambiri kuposa chuma chonse chomwe dzikoli lingapereke.

Yesu anati, “Ine ndi Atate ndife amodzi” (Yohane 10:30). Mulungu Atate ndi Mwana wa Mulungu ali amodzi mu cholinga – amodzi mwamakhalidwe. Ubale wawo ndi umodzi mwamugwirizano. Wolemba buku la Ahebri akulengeza kuti Yesu kwa Mulungu Atate ndiye, “kuwala kwa ulemero wake, ndi chifanizo cha umunthu wake” (Ahebri 1:3). Ulemerero wa Mulungu umaposa chabe kukongola kwake; ndi khalidwe lake. Pamene Mose adafunsa kuti amuwonetse ulemerero wake, Mulungu adadutsa pamaso pa Mose ndikulengeza za chikhalidwe chake:

AMBUYE, AMBUYE Mulungu, wachifundo, wachisomo, woleza mtima, wodzaza ndi ubwino ndi choonadi, amene akusungira chifundo zikwizikwi, akukhululukira kusaweruzika ndi zolakwa ndi tchimo. (Eksodo 34:6-7)

Kudziwa Mulungu monga momwe alili kumatigwirizanitsa ndi Iye. Chidziwitsochi chimachiritsa komanso chimapatsa moyo. Invani zomwe Yesu adanena popemphera kwa Atate wake: “Ndipo moyo wosatha ndi uwu, kuti akadziwe Inu Mulungu wowona yekha, ndi Yesu Kristu, amene mudamutuma” (Yohane 17:3). Yesu adawonetsa m’mawu ake ndi m’moyo wake momwe Mulungu Atate alili. Iye anati, “Indetu, indetu, ndinena kwa inu, sakhoza Mwana kuchita kanthu pa yekha, koma chimene awona Atate achichita;

pakuti zinthu zonse zimene azichita, zomwezo Mwananso amazichita” (Yohane 5:19).

Tikadziwa kuti Mulungu ndi wachikondi komanso wachifundo nthawi zonse tidzakopeka naye mwa chikondi ndi chidaliro. Tatsimikizikidwa kuti Mulungu amatikonda komanso amatifunira zabwino nthawi zonse, chifukwa njira zake sizisintha. Mulungu akuti mu Malaki 3:6, “Pakuti Ine ndine Yehova, sindisintha.” Iye sasintha monga ife tilili. Titha kukhala okoma mtima, achikondi, komanso oganiza bwino bola ngati atichitira mwachilungamo komanso mwaulemu, koma tikakumana ndi omwe amatipweteka, timakhala okwiya ndipo timafuna kubwezera. Mulungu samayankha mokwiya kapena mwa kubwezera choipa.

Mawu a Mulungu amatsimikizira kuti Yesu sasintha ngakhalenso Atate: “Yesu Kristu ali yemweyo dzulo ndi lero, ndi ku nthawi zonse” (Ahebri 13:8). “Mphatso iliyonse yabwino, ndi chininkho chilichonse changwiwo zichokera kumwamba, zotsika kwa Atate wa mauniko, amene alibe chisanduliko, kapena mthunzi wa kusintha” (Yakobo 1:17). Mawu awa akutitsimikiziranso kuti Mulungu wathu wofatsa alibe mbali yankhanza.

Ndipo Mawu anasandulikathupi, nakhala pakati pathu, (ndipo ife tinawona ulemerero wake, ulemerero wonga wa wobadwa yekha wa Atate) wodzala ndi chisomo ndi chowonadi.

— Yohane 1:14

Chitsanzo Chathu Changwiro

Mu mtima wa Ulaliki wa pa Phiri, Yesu amatipatsa chitsanzo chabwino cha m'mene tingakhaliye m'dziko lankhazali:

Munamva kuti kunalembedwa, Uzikondana ndi mnansi wako, ndi kumuda mdani wako; koma Ine ndinena kwa inu, Kondanani nao adani anu, ndi kupempherera iwo akuzunza inu; kotero kuti mukakhale ana a Atate wanu wa Kumwamba; cifukwa Iye amakwezera dzuwa lace pa oipa ndi pa abwino, namabvumbitsira mvula pa olungama ndi pa osalungama. Cifukwa kuti ngati muwakonda akukondana ndi inu mphoto yanji muli nayo? kodi angakhale amisonkho sacita comweco? Ndipo ngati mulankhula abale anu okha okha, mucitanji coposa ena? Kodi angakhale anthu akunja sacita comweco? Cifukwa cace inu mukhale angwiwo, monga Atate wanu wa Kumwamba ali wangwiwo. (Mateyo 5:43-48)

Kodi ndimeyi ikutiphunzitsa chiyani za Mulungu? Yesu akuti, “Kondanani nawo adani anu,” ndipo akutsatira ndikuti, “Kuti mukakhale ana a Atate wanu wa kumwamba,” ndipo akumaliza ndi, “Chifukwa chake inu mukhale angwiwo, monga Atate wanu wa Kumwamba ali wangwiwo.” Yesu akutiphunzitsa kuti tichitire adani athu monga momwe Atate wathu wa Kumwamba amachitira ndi adani ake. Afuna kuti timvetsetse kuti mfundo zapanwamba zomwe amatipatsa patsogolo pake mu Ulaliki wa pa Phiri zimatheka pokhapokha tikazona kuti zikuchokera kwa Mulungu mwini. Mu moyo wa Yesu, timapeza machitidwa athu abwino amomwe tingachitire ndi adani athu. Sanabwezere konse iwo amene anamulakwira. Kuchokera pa kuperekedwa kwake ndi kumangidwa mpaka pa kupachikidwa kwake, pomwe adapempha kuti omwe amuzunzawo akhululukidwe – “Atate, akhululukireni iwo; chifukwa

sadziwa chimene iwo akuchita” (Luka 23:34) – Iye adangowonetsa chikondi chokha.

Pamene Yesu sanalandiridwe mu mudzi wa Samariya, ophunzira ake Yakobo ndi Yohane adaganiza kuti mudziwo uwonongedwe ndi moto: “Ambuye, kodi mufuna kuti ife tilamule moto utsike kumwamba ndi kuwanyeketsa iwo, monga Eliya anachitira? Koma iye anatembenuka, nawadzudzula, nati, Simudziwa mzimu wa inu. Pakuti Mwana wa munthu sanadza kudzawononga miyoyo ya anthu, koma kudzapulumutsa iwo” (Luka 9:54-56).

Njira yabwino kwambiri yodziwira Mulungu ndi wotani ndi pophunzira za moyo wa Yesu. Sanaphe aliyense kapena kumuwopeza kuti atero. Yesu sanakhumudwitse aliyense. Sanaweruze aliyense. Pamene Filipino, m’ malo mwa ophunzira, adamufunsa Yesu kuti awawonetsere Atate, adayankha:

Ndakhala ndi inu nthawi yayitali, komabe simunadziwe ine, Filipino? Iye amene wandiona Ine wawona Atate; ndi motani unena kodi, Mutiwonetsere Atate? Sukhulupirira kodi? Ndili mwa Atate, ndi Atate ali mwa Ine? Mawu womwe ndimalankhula kwa inu sindilankhula kwa Ine ndekha: koma Atate omwe akhala mwa Ine, Iye amachita ntchitozo. (Yohane 14:9-10)

Pamene tikuphunzira zomwe zingatsutse ophunzira za umulungu, tiyeni titsimikizike kusunga mawu a Yesu ndi chitsanzo chake changwiro patsogolo pa malingaliro athu.

Gwero Lathu La Moyo

Pokhala ndi maziko oyamba otsimikizira chowonadi chakuti Mulungu ali wachikondi mosalekeza, tiunika zochita za Mulungu mu Baibulo zomwe zimawoneka ngati zosemphana ndi mfundo zophunzitsidwa ndi Yesu. Mu buku la Yesaya, timazindikira mozama za njira ndi malingaliro a Mulungu:

Pakuti maganizo anga sali maganizo anu, ngakhale njira zanu siziri njira zanga , ati Yehova. Pakuti monga kumwamba kuli kutari ndi dziko lapansi, momwemo njira zanga ziri zazitari kupambana njira zanu, ndi maganizo anga kupambana maganizo anu. (Yesaya 55:8-9)

Njira ndi malingaliro a Mulungu ndi wokwera kwambiri mu cholinga ndi chikhalidwe kuposa njira zathu ndi malingaliro athu. Chowonadi chotsimikizika chonena za Mulungu nchovuta kwa ife kumvetsetsa. Potsimikiza kudzilungamitsa tokha, timaganiza kuti Mulungu ali ngati ife. Timakwiya, ndiye timaganiza kuti Mulungu ayenera kukhala wokwiya ngati ife. Timasonkhezereka kubwezera ngati wina watilakwira, choncho timaganiza kuti Mulungu ayenera kukhala ndi mtima womwewo wobwezera pomwe walakwiridwa. Mulungu akutiuzana mosiyana:

Izi unazicita iwe, ndipo ndinakhala cete Ine; Unayesa kuti ndifanana nawe: Ndidzakudzudzula, ndi kucilongosola pamaso pako. (Masalmo 50:21)

Mulungu atalenga dziko lathu lapansi, sanafuna kuti lizingochitika lokha. Kuti Mulungu asakhuzike ndi dziko lathu lino silingakhale kokha zotsutsana ndi cholinga chake, zitha kutanthauza kuti moyo sungapitirire pa dziko lathuli – “Pakuti mwa Iye tikhala ndi moyo ndi kuyendayenda, ndi kupeza mkhalidwe wathu”

(Macitidwe 17:28). Mulungu amatisamalira mu mpweya uliwonse womwe timapuma.

Mulungu ndiye Gwero ndi Wosamalira za moyo zonse. Komabe, pali chinthu chimodzi chomwe chingatirekanitse ife ndi Iye – tchimo. Koma kodi tchimo ndi chiyani? Nthawi zambiri timaganiza tchimo ngati zinthu zoyipa zomwe timachita kapena kuphwanya malamulo a Mulungu. Lingaliro ndi lakuti tchimo limatha kuwerengedwa, pomwe ena a ife tili ndi ochulukirapo pomwe ena alibe angakhale pang’ono kapena ochepa. Mu Baibulo, timaphunzira zinthu zoyipa zomwe timachita ndi zizindikiro za matenda omwe tidatengera kuchokera kwa makolo athu oyamba. Matendawa akukhulupirira bodza loti Mulungu amasamala zofuna zake. Bodza ili la Satana lidasiyidwira mtundu wa anthu mu munda wa Edeni, ndipo lasokoneza chinthunzi chatu cha Mulungu kuyambira nthawi imeneyo.

Pamene Mulungu adalenga Adamu ndi Hava ndi kuwayika mu munda, adapatsidwa lamulo limodzi – ndi chimodzi chokha:

Ndipo Yehova Mulungu anamuuza munthuyo, nati, Mitengo yonse ya m’munda udyeko; koma mtengo wakudziwitsa zabwino ndi zoipa, usadye umenewo; cifukwa tsiku lomwe udzadya umenewo udzafa ndithu. (Genesis 2:16-17)

Ndikosavuta kumvetsetsa chifukwa chomwe Mulungu adaika “mtengo wa moyo” (Genesis 2:9) m’munda, koma ndizovuta kwa ife kumvetsetsa chifukwa chake adaika “mtengo wodziwitsa chabwino ndi choipa mumkhalidwe wangwiro. Poyamba, titha kuwona kupezeka kwa mtengowo, ndi chenjezo loti asadye chipatsocho, ngati choitanira tsoka.

Kupangidwa M'chifanizo Chake

Mu Genesis timapeza cholowa chathu: “Ndipo anati Mulungu, Tipange munthu m’cifanizo cathu, monga mwa cikhalidwe cathu: Kotero Mulungu adalenga munthu m’chifanizo chake, m’chifanizo cha Mulungu adamulenga iye; adalenga iwo mwamuna ndi mkazi” (Genesis 1:26-27). Kodi kumatanthauza chiyani kupangidwa m’chifanizo cha Mulungu, ndipo kodi chifanizo cha Mulungu nchiyani? Tidzapeza tanthauzo la Mulungu tikapeza tanthauzo lofotokoza kuti Mulungu ndi dani. Kutanthauzira kolondola kumapezeka mu 1 Yohane 4:8: “Mulungu ndiye chikondi” Onani kuti vesili sikuti limangonena kuti “Mulungu ndi wa chikondi,” ngati kuti chikondi ndi chimodzi mwa zinthu zake zambiri, koma limangonena mwachidule kuti, “Mulungu ndiye chikondi.” China chilichonse chomwe tingadziwe chokhuza Mulungu chiyenera kukhala chogwirizana ndi tanthauzo ili. Chifukwa chake, monga momwe Mulungu alili wangwiro, titha kunena kuti chikondi cha Mulungu chiyeneranso kukhala changwiro, chopanda kuzikonda. Kuphatikiza apo, chikondi chake chiyenera kukhala chosasinthika popeza sasintha.

Ngati tinapangidwa m’chifanizo cha Mulungu, ndiye kuti tiyenera kulengedwa ndi Mulungu kuti tikondane. Tsopano chikondi, kukhala chikondi sichingakakamizike kapena mwa njira iliyonse kukakamizidwa. Chitha kupatsidwa mwaulere ngati chisankho. Izi zimamveka mosavuta ngati tingaganizire munthu wa njala ya chikondi wokhala ndi mfuti yodzaza zipolopolo ndikukera basi ndikupempha chikondi kwa apaulendo powawopseza kuti awapha. Kodi njirayi ingabweretse chikondi?

Tiyerekeze kuti titayesa njira yocheperako yopezera chikondi popanga loboti yomwe idakonzedwa kuti iziti “Ndimakukondani” pamene tayandikira. Kodi izi zingabweretse ubale wokhutitsa

komanso watanthauzo wokondana? Kodi njira izi, zomwe zalephera kupeza chikondi, zingagwire ntchito kwa Mulungu?

Tiyeni tibwerere ku munda wa Edeni ndi mtengo wovuta woletsedwa. Mulungu akanapanda kupanga mtengo, kodi zikanatheka kuti anthu azikondana monga momwe Mulungu amakondera? Kuti chikondi, chikhale chikondi, chimafuna kuti chiziperekedwa momasuka, tiyeneranso kukhala ndi ufulu wosakonda. Chikondi nthawi zonse chimakhala chisankho; chikondi sichingathe kulumulidwa kapena kukakamizidwa.

Mulungu akadakhala kuti adalenga makolo athu oyamba ndikuwayika mu mundamo popanda kuwapatsa njira yowonekera yomwe akanasankha kusamkonda ndi kumukhulupirira, sizikanatheka kuti iwo azikonda monga Mulungu mwiniyo amakondera. Monga momwe Mulungu ali Kasupe wa moyo, alinso Gwero lathu la chikondi chenicheni – moyo ndi chikondi ndizogwirizana nzosasiyanitsidwa. Kulengedwa m'chifanizo cha Mulungu kumapereka mwayi kwa aliyense wa ife kukhala bwenzi la chikondi la Mlengi wathu.

Mulungu sanaike mtengo wodziwitsa chabwino ndi choipa ndi lamulo loletsa kudya nthambi zake ngati mayeso omumverera Iye, koma monga chitsimikizo chakuti amayamikira ufulu wathu wosankha kotero kuti anali wofunitsitsa kukhala pachiwopsezo kuti titha kusankha kumusiya Iye. Tikamvetsetsa chifukwa chake Mulungu adaika mtengo woletsedwa m'mundamo, sitidzamunena kuti ndi wolamulira mwankhanza. Panali m'modzi, komabe, yemwe anali wokonzeka kuneneza Mulungu za chinthu chomwecho.

Wonyenga Wamkulu

Ndipo njoka inali yakucenjera yoposa zamoyo zonse za m'thengo zimene anazipanga Yehova Mulungu. Ndipo inati kwa mkaziyo, Ea! Kodi anati Mulungu, Usadye mitengo yonse ya m'mundamu? Mkaziyo ndipo anati kwa njoka, Zipatso za mitengo ya m'mundamu tidye. Koma zipatso za mtengo umene uli m'kati mwa munda, Mulungu anati, Musadye umenewo, musakhudze umenewo, mungadzafe. Njokayo ndipo inati kwa mkaziyo, Kufa simudzafai; cifukwa adziwa Mulungu kuti tsiku limene mukadya umenewo, adzatseguka maso anu, ndipo mudzakhala ngati Mulungu, wakudziwa zabwino ndi zoipa.

— Genesis 3:1-5

Choyamba, tiyeni tione kuti njoka yoyankhulayi ndi ndani. Kodi njoka iyi ndani? “Ndipo cinaponyedwa pansi cinjoka cacikuru, njoka yokalambayo, iye wochedwa mdierekezi ndi Satana, wonyenga wa dziko lonse; cinaponyedwa pansi kudziko, ndi angelo ace anaponyedwa naye pamodzi” (Cibvumbulutso 12:9). Hava sanali kungoyankhula ndi njoka yochenjera, koma ndi Satana – wonyenga wamkuluyo.

Njokayo mwa kunamidzira mosabisa inatsutsa Mulungu mwa kunamiza Adamu ndi Hava kuti akuwabisira kanthu kena kabwino. Kuphatikiza apo, ngati atangodya chipatsocho, maso awo adzatseguka, ndipo adzakhala ngati “milungu, yodziwa zabwino ndi zoipa.” Mkazi wasankha ndani kuti akhulupirire, Mulungu kapena Satana?

Ndipo pamene anaona mkaziyo kuti mtengo unali wabwino kudya, ndi kuti unali wokoma m'maso, mtengo wolakalakika wakupatsa nzeru, anatenga

zipatso zace, nadya, napatsanso mwamuna wace amene ali naye, nadya iyenso. Ndipo anatseguka maso ao a onse awiri, nadziwa kuti anali amarisece: ndipo adasoka masamba amkuyu, nadzipangira matewera. Ndipo anamva mau a Yehova Mulungu alikuyendayenda m'munda nthawi ya madzulo: ndipo anabisala Adamu ndi mkazi wace pamaso pa Yehova Mulungu pakati pa mitengo ya m'munda. Ndipo Yehova Mulungu anaitana mwamunayo nati kwa iye, Uli kuti? (Genesis 3:6-9)

Pamene Adamu ndi Hava adadya za mtengo woletsedwa maso awo anatseguka (adayamba kudzindikira), ndipo adafuna kubisala kwa Mulungu. Mulungu adayankha kuti chiyani? Anabwera kudzawafuna. Mawu ake oyamba anali, “Uli kuti?” Adafunafuna kuyanjanitsidwa kwa ana ake omwe tsopano anali achilendo atasokonekera.

Pakuti Mwana wa munthu anadza kufunafuna ndi kupulumutsa cotayikaco.

— Yesu (Luka 19:10)

Kodi Tchimo Ndi Chiyani?

Tsopano, tibwerere ku funso: kodi tchimo ndi chiyani? Kuti tipeze tanthauzo lolondola, ndikofunikira kuti tidzindikire zomwe zidasokonekera “pa mtengo wodziwitsa zabwino ndi zoipa.” Mu Genesis 3:6, mayiyo adawona zithu zitatu zofunika pamtengo:

1. “Mtengo unali wabwino kudya.” Pamwamba izi zikuwoneka ngati zowona, zikanapanda kuti mtengowo udaletsedwa ngati chakudya. Vuto silinali chipatso chomwecho koma kuti mayiyu anali kuchiyang’ana ngati chabwino.

2. Mtengowo “unali wokongola m’maso mwake.” Chilichonse chimene Mulungu adalenga m’mundamo chinali changwirowo, chifukwa chake mtengowo “ungakhale wokongola m’maso.” Mkaziyo anawona chimodzi chowonjezera chokhumbirika cha mtengowo.

3. “Mtengo wolakalakika wopatsa nzeru.” Zoonadi? Kodi mtengo uwu unali ndi zinsinsi zina? Kodi njokayo yinali yolondola? Kodi kungakhale kofunika kudziwa zabwino ndi zoipa? Ndipo kodi kudziwa zabwino ndi zoipa kumatanthauzanji? Kodi ndikungopeza chidziwitso?

Vesili likumaliza ndi kuti “adatenga zipatso zake, nadya, napatsa mwamuna wake pamodzi naye, nadya iye.” Izi nthawi zambiri zimamveka kuti ndi tchimo la munthu, koma tchimo ndi chiyani? Nchiyani chomwe chinabwera poyamba – kudya chipatso kapena kukhulupirira bodza la njoka ponena za Mulungu?

Vuto lalikulu linali pamene Hava anakukhulupirira bodza la njoka loti Mulungu anali kuwabisira kanthu kena kabwino. Tchimo silimangokhala zochitika zokha ngati kuti tchimo ndi chinthu chowerengeka. Tchimo, pachimake, ndilo vuto la malingaliro lomwe limawona Mulungu ngati munthu wongodzikonda ndipo wosamudalira.

Tchimo tingaliyerekezere ndi matenda. Mu matenda pali zomwe zimayambitsa matenda monga tizirombo, chakudya chosagayika bwino, kapena kuchepa kwa chitetezo cha mthupi. Zoyambitsa zazikuluzikuluzi zimabweretsa chizindikiro chimodzi kapena zingapo: kutentha thupi, mseru, kupweteka, chizungulire, ulesi, ndi zina zambiri. Ndi tchimo, choyambitsa chachikulu ndi kukhulupirira bodza lonena za Mulungu, ndipo chotsatira chake, kudzipatula tokha kwa Iye amene chikondi chake chimakhala kwa ena. Mchimo athu akunja (zizindikiro) ndi zotsatira zokhulupirira kuti Mulungu ndi wozikonda (zomwe zimayambitsa matenda). Yesu pokambirana ndi alembi ndi Afarisi, adagwiritsa fanizo ili la tchimo ngati matenda omwe amafunika kuchiritsidwa:

Ndipo alembi ndi Afarisi, pakuona kuti alinkudya nao wocimwa ndi amisonkho, ananena ndi ophunzira ace, Uyu akudya ndi kumwa nao amisonkho ndi ocimwa. Ndipo pamene Yesu anamva ici, ananena nao, Akulimba safuna sing'anga, koma odwala ndiwo; sindinadza kudzaitana olungama, koma ocimwa kuti alape. (Marko 2:16-17)

Tchimo ndi lowopsa chifukwa limatirekanitsa ife ndi Mulungu, Gwero la moyo wonse. Pakulekana kumene kumachitika, si Mulungu amene akumalekanitsa ndi ife – nthawi zonse timadzapatula tokha kwa Iye. Adamu ndi Hava anayamba kuopa Mulungu kuposa Satana – amene anayenera kumuopa. Atadya chipatso, Baibulo limati, “Adamu ndi mkazi wake anabisala pa maso pa Yehova Mulungu pakati pa mitengo ya m'munda” (Genesis 3:8). Takhala tikubisalira Mulungu wathu wofatsa kuyambira tsiku lomwelo. Tiyenera kudziwa kuti Mulungu atachenjeza Adamu ndi Hava kuti asadye za mtengo woletsedwa, sananene kuti, “Tsiku lomwe udzadya, ndidzakupha,” Iye anati, “Tsiku lomwe udzadya umenewo udzafa ndinthu.” Mwamuna ndi mkazi wake atadya za mtengowo, kufa kunayamba tsiku lomwero pamene anadzapatula ku Gwero la moyo wao. Iri ndi (kukhulupirira bodza loti Mulungu ndiwodzikonda komanso wosadalirika) lowopsa kwambiri, osati

Mulungu: “Mphoto yake ya uchimo ndi imfa” (Aroma 6:23). Mulungu sachita bizinesi ya machismo, ndipo salipira mphoto za uchimo.

Zikuwonekeranso kuti Adamu ndi Hava atadya chipatso cha mtengo woletsedwa, adalandira zambiri kuposa chidziwitso cha m'mutu cha chabwino ndi choipa. Mosadzindikira adadzipereka okha ndi mbadwa zawo kuti adziwe zabwino ndi zoipa. Iwo sakanangodziwa za zoipa zokha; iwo angaganize izo, iwo angakhale moyo wa izo, iwo angakhale akapolo a izo; ndipo zotsatira adziwa ululu, kuvutika, mantha, ndi imfa. Anthu sanali okha akuvutika ndi zotulukapo zosapeweka pamene uchimo unalowa m'dziko lathu. Chilengedwe chonse chidakhuzidwa ndi kusagwirizana pakati pa chilengedwe ndi Mlengi zomwe zidayambidwa ndi tchimo la Adamu ndi Hava: “Pakuti tidziwa kuti colengedwa conse cibiula, ndi kugwidwa m'zowawa pamodzi kufikira tsopano” (Aroma 8:22). Dziko lapansi linakhala malo owopsa kwa anthu komanso nyama. Chiyambire chigumula cha m'masiku a Nowa, dziko lapansi lakhala likukumana ndi nyengo za chiwawa, zivomerezi, mapiri ophulika moto, ndi zinthu zina zowononga za chilengedwe. Mphamvu za chiwawa zoonekera m'chilengedwe sizichokera kwa Mulungu; zimakhalapo chifukwa choti tayika Mulungu patali ndi ife.

Nchifukwa Chiyani Pali Mdierekezi?

Kunenedwa kwapangidwa kale za winawake weniweni wauzimu amene anaziyika yekha motsutsana ndi Mulungu. Iye amatchulidwa mu Baibulo kuti Satana, Mdierekezi, Njoka, Ng'ona, ndi Lusifala ndi maina ena angapo. Poyerekeza zaka mazana awiri zapitazo, anthu ochepa kwambiri ku mayiko akumadzulo masiku ano amakhulupirira Satana weniweni. M'chikhalidwe chathu chamakono, Satana nthawi zambiri amatsitsidwa kuzikhulupiriro komanso umbuli. Ndi ganizo ili m'malingaliro awa, komanso poyankha funsoli, kuti tiwunike nkhani ya mu Baibulo yonena za Satana (mdani).

Satana amadziwika mu Baibulo kuti ndi m'ngelo wakugwa. Mawu oti kugwa amatanthauza kuti Satana poyambirira anli m'ngelo wopanda tchimo amene anasankha kupandukira Mlengi wake. Chifukwa chake adapandukira Mulungu ndicha chinsinsi, poganizira chilengedwe changwiro kumwamba. Mwachiwonekere, anali ndi udindo wolemekezeka komanso wotsogolera pakati pa angelo. Nthawi yina, mbeu yonyada idamera ndikukula ndi kupangitsa kusakhutira ndi udindo wake kumwamba. Izi pamapeto pake zidafika pakupandukira Mulungu. Si Satana yekha adapandukira. Anatha kuthandizidwa ndi angelo ena ambiri, ngakhale kuti angelo ambiri ochuluka adasankha kukhalabe okhulupirika kwa Mulungu. Nkhondo yomwe idabwera chifukwa cha kupanduka kwa Satana ndi omutsatira sinali yokhuza zida za nkhondo monga zida za nkhondo za dziko lapansi. Mulungu adapambana pa nkhondo yakumwambayi pogwiritsa chikondi chotsutsana ndi kudzikonda, chowonadi chotsutsana ndi chinyengo, kuwonekera kutsutsana ndi chinsinsi, kuganiza bwino kutsutsana ndi zopanda pake, kuleza mtima kutsutsana ndi kutsimidwa, ndi kudalira kutsutsana ndi kukayikira. M'pomveka kukhulupirira kuti njira zomwe Satana adagwiritsira ntchito kwa Hava mu munda wa Edeni

zopangitsa kuti apatukane ndi Mulungu ndi zomwezo anachita kuti akhale ndi omutsatira ake kumwamba. Mpaka nthawi imeneyo, funso lonena za chilungamo cha Mulungu linali lisanabweretsedwe pa maso pa angelo kumwamba. Iwo analibe njira yodziwira motsimikiza kotheratu ngati zonena za Satana motsutsana ndi Mulungu zinali zowona, kapena ayi. Pa chifukwa ichi Satana wapatsidwa mwayi woti awonetse ulamuliro wake.

Titha kufunsa kuti bwanji Mulungu sanawononge mdani wake poyambirira kwa kupanduka. Kodi izi sizikanalepheretsa kuchuluka kwa opandukawo? Ayi, izi zikanatsimikizira kwa angelo kuti zomwe Satana ananena motsutsana ndi Mulungu zinali zenizeni. Mulungu akadamuwononga Satana, zomwe zikanapangitsa ufulu kukhala chinthu chopanda pake chopanda phindu. Pali china chake kupatula izi. Kukhala osasitha pakuphunzira kwathu kwa Baibulo, kulemerera kwa maumboni kumatsimikizira kuti Mulungu sawononga – tchimo limatero. Kenako Satana adzawonongedwa. Kuwonongeka kumeneku sikuchokera kwa Mulungu, koma ndi tchimo la Satana lomwe:

Nandidzeranso mau a Yehova, akuti, Wobadwa ndi munthu iwe, kweza nyimbo ya maliro yolirira mfumu ya Turo, niziti kwa iye, Atero Ambuye Yehova, Wakomera muyeso ndi cizindikiro, wodzala ndi nzeru wokongola wangwiro. Unali m’Edene, munda wa Mulungu, mwala uli wonse wa mtengo wace unali copfunda cako, sardiyo, topazi, diamondi, berulo, sohamu, ndi yaspi, safiro, nofeki, bareketi, ndi golidi; malingaka ako ndi akazi ako anakutumikira tsiku lolengedwa iwe zinakonzeke ratu. Unali kerubi wodzodzedwa wakuphimba, ndipo ndinakuika unali pa phiri lopatulika la Mulungu, anayendayenda pakati pa miyala yamoto. Unali wangwiro m’njira zako cilengedwere iwe, mpaka cinapezeka mwa iwe cosalungama. Mwa kuculuka kwa malonda ako anakudzadza m’kati mwako ndi ciwawa, ndipo unacimwa; cifukwa cace

ndinakukankha kukucotsa pa phiri la Mulungu; ndipo ndinakuononga, kerubi wakuphimba iwe, kukucotsa pakati pa miyala yamoto. Unadzikuza mtima cifukwa ca kukongola kwako, waipsa nzeru zako; cifukwa ca kuwala kwako ndakugwetsa pansu, ndakuika pamaso pa mafumu, kuti akupenye. Mwa phulupulu zako zocuruka ndi malonda ako osalungama waipsa malo ako opatulika; cifukwa cace ndaturutsa moto m’kati mwako wakunyeketsa iwe; ndipo ndakusandutsa mapulusa panthaka pamaso pa onse akuona. Onse akudziwa iwe mwa mitundu ya anthu adzadabwa nawe; wasanduka coopsa, ndipo sudzakhalanso konse. (Ezekieli 28:11-19)

Mfumu yaku Turo ikuyimira Satana moyenera mu nkhani yake. Satana analengedwa wangwiro, wopanda kunyada kapena kudzikonda. Kugwa kwake kuchokera ku ugwiro kunali chifukwa cha iye mwini, ndipo analibe chowiringula pa zomwe adachita. Adadzitukumula chifukwa cha kukongola kwake. “Moto” womwe udzawononge Satana sudzabwera kuchokera kwina; udzachokera mkati mwa Satana iye mwini. Moto uwu ndi kudzikonda kwake. Ndiwo moto wodziyambitsa wokha womwe udzamudye. Satana sadzakhalapo – “iye sadzakhalaponso.”

Wagwadi kucokera kumwamba, iwe nthanda, mwana wa mbanda kucha! Wagwetsedwa pansu, iwe wolefula amitundu! Ndipo iwe unati mumtima mwako, Ndidzakwera kumwamba, ndidzakweza mpando wanga wacifumu pamwamba pa nyenyezi za Mulungu; ndidzakhala pamwamba pa phiri la khamu, m’malekezere a kumpoto; ndidzakwera pamwamba pa mitambo, ndidzafanana ndi Wam’mwambamwamba. (Yesaya 14:12-14)

Lusifala (dzina loyambirira la Satana) adagwa chifukwa amafuna kudzikweza. Yesu adaphunzitsa otsatira ake, “Ndipo amene ali yense akadzikuza yekha adzacepetsedwa; koma amene adzicepetsa mwini yekha adzakulitsidwa” (Mateyu 23:12). Lusifala

adadzichititsa manyazi yekha. Mawu ake “Ndidzakhala ngati Wam’mwambamwamba” akuwonetsa zowona kuti amangokhumba udindo wa Mulungu. Analibe chidwi chowonetsa makhalidwe a Mulungu (njira yokhayo yomwe cholengedwa chingafanane ndi Mulungu).

Pofufuza nkhaniyi, ziyenera kudziwika kuti malingaliro onenedwa okhuza Mulungu ndi a Lusifala ndipo sakulongosola molondola zolinga za Mulungu. Lusifala, chifukwa chofuna kwambiri kudzikweza, adayamba kulingalira kuti Mulungu ali ndi cholinga chodzikonda chonchi.

Ndipo munali nkhondo m’mwamba. Mikayeli ndi angelo ace akucita nkhondo ndi cinjoka; cinjokanso ndi angelo ace cinacita nkhondo; ndipo sicalakika, ndipo sanapezekanso malo ao m’mwamba. Ndipo cinaponyedwa pansi cinjoka cacikuru, njoka yokalambayo. Iye wochedwa mdierekezi ndi Satana, wonyenga wa dziko lonse; cinaponyedwa pansi kudziko, ndi angelo ace anaponyedwa naye pamodzi. (Cibvumbulutso 12:7-9).

Ndimeyi ikunena za nkhondo yakumwamba pomwe Satana adayamba ntchito yake ya chinyengo. Ntchito yake sinangokhala pakakona kakang’ono kokha ka dziko lathu lapansi; wanyenga ‘dziko lonse lapansi.’”

Ndipo anati kwa iwo, Ndiona Satana alinkugwa ngati mphezi wocokera kumwamba. (Luka 10:18)

Yesu akulankhula apa zakufulumira kwa kugwa kwa Satana kuchoka pakukhulupirika kufikira ku kuwukira.

Pakuti takhala ife coonetsedwa ku dziko lapansi, ndi kwa angelo, ndi kwa anthu. (1 Akorinto 4:9)

Mwa iwo amene anakulalikirani Uthenga Wabwino mwa Mzimu Woyera, wotumidwa kuchokera

Kumwamba; zinthu izi angelo alakalaka kusuzumiramo.
(1 Petro 1:12)

Satana atapanduka kumwamba, anatenga angelo angapo, angelo okhulupirika otsalawo sanamvetsetse zomwe zimachitika komanso chifukwa chake. Uthenga wabwino ndi wawo, monganso kwa ife, ndipo ali ndi chidwi chachikulu ndi kuyetsetsa kusadzikonda kwa Mulungu pa dziko lino lapansi kuti apulumutse anthu ku chiwonongeko chawo. “Uthenga wabwino wosatha” (Cibvumbulutso 14:6) ndikutsimikizira kuti chilengedwe chidzakhala kwamuyaya popanda kukayika kulikonse pakukhulupirika kwa Mulungu: “Mulingaliranj cotsutsana ndi Yehova? Iye adzatha psiti; nsautso siidzauka kawiri” (Nahumu 1:9).

Pamenepo Yesu anatengedwa ndi Mzimu kumka kucipululu kukayesedwa ndi mdierekezi. Ndipo pamene Iye analibe kudya masiku makumi anai usana ndi usiku, pambuyo pake anamva njala. Ndipo woyesayo anafika nanena kwa Iye, Ngati muli Mwana wa Mulungu, tauzani kuti miyala iyi isanduke mikate, Koma Iye anayankha nati, Kwalembedwa, Munthu sadzakhala ndi moyo ndi mkate wokha, koma ndi mau onse akuturuka m’kamwa mwa Mulungu. Pamenepo mdierekezi anamuka naye ku mzinda woyera; namuika Iye pamwamba pa cimbudzi ca Kacisi, nanena naye, Ngati muli Mwana wa Mulungu, mudzigwetse nokha pansi: pakuti kwalembedwa, kuti, Adzauza angelo ace za iwe, Ndipo pa manja ao adzakunyamula iwe, Ungagunde konse phazi lako pamwala. Yesu ananena naye, Ndiponso kwalembedwa, Usamuyese Ambuye Mulungu wako. Pomwenso mdierekezi anamuka naye ku phiri lalitali, namuonetsa maiko onse a dziko lapansi, ndi ulemerero wao; nati kwa Iye, Zonse ndikupatsani Inu, ngati mudzagwa pansi ndi kundigwadira ine. Pomwepo Yesu ananena kwa iye, Coka Satana, pakuti kwalembedwa, Ambuye Mulungu wako udzamgwadira, Ndipo Iye yekha yekha

udzamlambira. Pomwepo mdierekezi anamsiya Iye, ndipo onani, angelo anadza, kumtumikira Iye. (Mateyu 4:1-11)

Satana anadza kwa Yesu ngati woyesa; cholinga chake chowoneka kuti achotse chikhulupiriro ndiponso kudalira kwa Yesu pa Atate wake. Satana anachita bwino pogwiritsa njira yomweyi kwa Hava mu munda wa Edeni. Satana anali atatsimikiza mtima kulepheretsa cholinga cha Yesu chobwera pa dziko lino lapansi kudzapulumutsa anthu poyesa Yesu kuti agwiritse ntchito mphamvu zake za uzimu kuti adzipindulire. Wonyengayo anali wofunitsitsa kuti amulepheretse Yesu kuchita bwino pantchito yake yowulula kusadzikonda kwa Mulungu – zomwe zingawonetse Satana kuti ndi wabodza.

Mu yesero limodzi mdierekezi adampatsa Yesu “maufumu a dziko lapansi” ngati Yesu akadangomugwadira ndi kumulambira. Nzochititsa chidwi kuti Yesu sanatsutse zoti Satana ali ndi ulamuliro pa “maufumu a dziko lapansi.” Pomwe Mulungu adalenga anthu koyamba, adapatsa anthu ulamuliro “pa dziko lonse lapansi” (Genesis 1:26), Koma Adamu ndi Hava atakhulupirira bodza la Satana lonena za Mlengi wawo, adaperekanso mphamvuzo kwa Satana. Timawona chinyengo, kuponderezana, kukakamizana, ndi kusalinganika mu “ufumu wa dziko lonse lapansi.” Mu ufumu wa Mulungu palibe mphamvu yogwiritsidwa ntchito nthawi iliyonse kapena munthawi iliyonse. Palibe kufanana pakati pa ufumu wake ndi maufumu apa dziko lapansi, omwe amadalira kulamulira ndi malamulo osati malamulo a chikondi.

Sindidzalankhulanso zambiri ndi inu, pakuti mkuru wa dziko lapansi adza; ndipo alibe kanthu mwa Ine. (Yahane 14:30)

Yesu akutsimikiza kuti ndi Satana yemwe ali “Karonga wa dziko lapansi.” Tikakana zakuti Satana aliko komanso kuti ali ndi mphamvu pa dziko lapansi pano, mosadziwa timayika Mulungu mlandu kuti tikumana ndi mavuto.

Khalani odzisungira, dikirani, mdani wanu mdierekezi, monga mkango wobuma, ayendayenda ndi kufunafuna wina akamlikwire. (1 Petro 5:8)

Tabvalani zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoze kucirimika pokana macenjerero a mdierekezi. Cifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukulu, ndi maulamuliro, ndi akucita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a coipa m'zakumwamba. (Aefeso 6:11-12)

Tikazindikira kuti tonsefe ndife ozunzidwa ndi chinyengo chonena za Mulungu chomwe chinayambika pa mtundu wa anthu, sitidzayang'ana pa anthu ena ngati adani athu, koma monga ozunzidwa anzathu pachinyengo chachikulu ichi.

Ndipo linali nayo Mfumu yakulilamulira, mngelo wa phompho; dzina lace m'Cihebri Abadoni, ndi m'Cihelene ali nalo dzina Apoliyoni. (Cibvumbulutso 9:11)

“Mngelo wa phompho” amanthauza Satana, Apollyon, dzina lomweadapatsidwa pano, limanthauza wowononga m'Chigiriki. Satana ndiye wowononga. Kodi tingakhale ndi chifukwa chomveka choperekera udindo womwewu kwa Mulungu wathu wofatsa?

Siikudza mbala, koma kuti ikabe, ndi kupha, ndi kuwononga, Ndadza Ine kuti akhale ndi moyo, ndi kukhala nao wocuruka.

— Yesu (Yohane 10:10)

Njoka Yowononga

Milili yomwe Mulungu anatumiza motsutsa Aigupto ikuwoneka ngati zina mwa machitidwe a Mulungu wowononga mwadala. Pamwamba zikuwoneka ngati palibe njira ina iliyonse yotanthauzira izi mu Baibulo. Kumbukirani, komabe, vesi lomwe tidawerenga kale ili: “Pakuti maganizo anga Sali maganizo anu, ngakhale njira zanu siziri njira zanga, ati Yehova” (Yesaya 55:8).

Mose adasankhidwa ndi Mulungu kuti atsogolere ana a Israyeli kuchokera ku ukapolo ku Aiguputo kupita ku ufulu. Amayenera kupita kwa Farao kukachenjeza za matsoka omwe atsala pang’ono kuchitika mdziko lake. Mulungu atakumana ndi Mose mchipululu, adamupatsa phunziro lomwe Mose ndi Aroni adzawonetsera pa maso pa Farao lomwe liziwonetsa wolamulirayo ndendende momwe Mulungu adzakhalire pa zovuta zazikulu zikubwerazi:

Ndipo Yehova ananena naye, Ico nciani m’dzanja lako? Nati, Ndodo. Ndipo ananena Iye, Iponye pansi. Naiponya pansi, ndipo inasanduka njoka; ndipo anaithawa. Koma Yehova anati kwa Mose, Tambasula dzanja lako, nuigwire kumcira; ndipo anatambasula dzanja lace, naigwira, nikhalanso ndodo m’dzanja lace. (Eksodo 4:2-4)

Pamenepo mkwiyo wa Yehova unamyakira Mose, ndipo anati, Nanga Aroni Mlevi mbale wako sialipo kodi? Ndidziwa kuti kulankhula alankhula. Ndipo iye adzukulankhulira iwe kwa anthu: ndipo kudzatero, kuti iye adzakhala kwa iwe ngati m’kamwa, ndi iwe udzakhala kwa iwe ngati Mulungu. Ndipo ukaigwire m’dzanja lako ndodo iyi, imene ukacite nayo zizindikilo. (Eksodo 4:14, 16-17)

Mose anayenera kupita kwa Farao monga nthumwi ya Mulungu. Cholinga cha Mulungu mu chiwonetserochi chinali choti

sichingokhala kuwonetsera chabe mphamvu; chinali chodziwitsa wownonga weniweni ndani. Pamene Mose, monga woimira Mulungu, adagwira ndodo m'dzanja mwake zimaimira mphamvu za chilengedwe zomwe zili m'dzanja la Mulungu. Palibe vuto lomwe likanabwera ku Aiguputo bola ngati dzanja loteteza la Mulungu likuletsa mphamvu zowononga za chilengedwe. Mose ataponya pansi ndodoyo, idasanduka njoka, chizindikiro choipa ndi chiwonongeko. Izi zikuimira mphamvu za chilengedwe zomwe zachoka m'dzanja la Mulungu ndipo zili m'dzanja la Satana – wowononga.

Zaka mazana ambiri nthawi ya Mose asanafike komanso Yosefe (yemwe adagulitsidwa mu ukapolo ndi able ake) adamasulira maloto ovuta a Farao panali dongosolo labwino kwambiri kwa ana a Israyeli. Farao adakweza Yosefe kukhala malo olemeketeka ndi ulemu pomasulira maloto a ulosi komanso kuwoneratu kwake pakukonzekeretsa mtunduwo ku njala ya zaka zisanu ndi ziwiri. Aigupto anaonetsa kuyamikira Yosefe ndi Mulungu amene anali kumulambira. Mulungu adatha kudalitsa mtunduwo molemera. Zaka zambiri Yosefe atamwalira, Aigupto adayiwala za iye ndi Mulungu wake ndipo adapanga akapolo a ana a Israyeli omwe adachita bwino ndi kuchulukirachulukira mdzikolo. Aigupto, mwa machitidwe awo anali kutumiza uthenga kuti sakufuna kukhalapo kwa Mulungu. Anali ndi milungu yawo ndipo sanafune kuvomereza Mulungu wa akapolo awo. Mulungu sanathenso kupitiriza kuchuluka kwa madalitso ndi chitetezo pa nthawi imodzimodziyo kulola Aiguputo ufulu wawo kuzipatula kwa Iye.

Ngati nthawi ina milili itayamba, Farao akadatembenuka kusiya njira yake yotsutsa ndikulola Aisrayeli apite, Mulungu akadalamuliranso mphamvu za chilengedwe, ndipo milili ikadatha. Wolamulira wamakaniyo sanachite izi, ndipo Iguputo anatsala bwinja. Udindo wa Mulungu mu milili ya Aiguputo umawonekera tikalingalira za uthenga wophiphiritsa omwe Mulungu adapereka mu ndodo ndi njoka.

Thandizo lowonjezera lakuchotsera Mulungu pa milandu yakuwonongedwa ndi zinthu za chilengedwe limapezeka mu buku la Mafumu woyamba. Mneneri Eliya pa nthawi yovuta mu utumiki wake anali kubisala ku phanga kwa Mfumukazi Yezabeli, yemwe adawopseza moyo wake. Mulungu adadza kwa mneneri yemwe adathawa:

... Nati kwa iye, Ucitanji pano, Eliya? Ndipo anati, Ine ndinachitira cangu Yehova Mulungu wa makamu; popeza ana a Israyeli anasiya cipangano canu, napasula maguwa anu a nsembe, napha aneneri anu ndi lupanga, ndipo ndatsala ndekha, ndipo afuna moyo wanga kuucotsa. Ndipo Iye anati, Turuka nuime pa phiri lino pamaso pa Yehova. Ndipo taonani, Yehova anapitapo, ndi mphepo yaikuru ndi yamphamvu inang'amba mapiri, niphwanya matanthwe pamaso pa Yehova; koma Yehova sanakhala m'mpheapomo. Itapita mphepoyo kunali cibvomezi; komanso Yehova sanali m'cibvomezimo. Cinaleka cibvomezi panali moto; koma Yehova sanali m'motomo. Utaleka moto panali bata la kamphepo kayaziya. (1 Mafumu 19:9-12)

Mulungu wathu wofatsa amalankhulabe momveka ndi kamvekedwe kakang'ono kayaziya.

Kugwidwa Kwa Yobu

Buku la Yobu limapereka umboni woonekeratu wokhudzidwa ndi Satana pa mazunzo ndi chiwonongeko. Zimatipatsanso chithunzi chakumbuyo kwa nkondo ya uzimu pakati pa Mulungu ndi mphamvu zoyipa. Yobu, “munthu wangwiro ndi woongoka” (Yobu 1:8), adapezeka pakati pa mavuto pa nthawi yovuta kwambiri ya nkondo ya uzimu:

Ndipo panali tsiku lakuti ana a Mulungu anadza kudzionetsa kwa Yehova, nadzanso Satana pakati pao. Nati Yehova kwa Satana, Ufuma kuti? Nayankha Satana kwa Yehova, nati, Kupitapita m’dziko ndi kuyendayenda m’mwemo. Ndipo Yehova anati kwa Satana, Kodi waonerera mtumiki wanga Yobu? Pakuti palibe wina wonga iye m’dzikomo, munthu wangwiro ndi woongoka, wakuopa Mulungu ndi kupewa zoipa. Nayankha Satana, nati kwa Yehova, Kodi Yobu aopa Mulungu pacabe? Kodi simunamcinga iye ndi nyumba yace, ndi zace zonse, pomzinga ponse? Nchito ya manja ace mwaidalitsa, ndi zoweta zace zachuruka m’dziko. Koma mutambasule dzanja lanu ndi kumkhudzira zace zonse, ndipo adzakuchitirani mwano pankhope panu. Nati Yehova kwa Satana, Taona, zonse ali nazo zikhale m’dzanja mwako; pa iye pokha usatambasula dzanja lako. Naturuka Satana pamaso pa Yehova. (Yobu 1:6-12)

Nthawi yomweyo Satana anafuna kuwononga zonse Yobu anali nazo, kuphatikizapo ana ake a amuna ndi a akazi. Mu chiwonongeko chotsatira, Satana anagwiritsa ntchito achifwamba “Sabeans” (vesi 15) ndi “Akasidi” (vesi 17), “moto wa Mulungu kuchokera kumwamba” (vesi 16), ndi “mphepo ya mkuntho kuchokera kuchipululu” (vesi 19).

Ngakhale zikuwonekeratu mu buku la Yobu kuti wowonongayo ndi ndani, owerenga ambiri akadali ndi nkhwana ndi mavuto a Yobu chifukwa amaganiza molakwika kuti Mulungu adalola Satana kuzunza Yobu. Lingaliro ndiloti popeza Mulungu ndi mphamvu zonse, akanayenera kulepheretsa Satana kuukira Yobu. Komabe, mphamvu ya Mulungu sinali nkhwana yofunika; zakhala zikukhala ndipo zakhala zikukhuzana ndi mfundo za Mulungu za kayendetsedwe ka ntchito – kodi Mulungu ndiwosasinthika popatsa ufulu kwa zolengedwa zake za nzeru kapena sichoncho? Ufulu kukhala ufulu, uyenera kukhala wosasinthika; kutanthauza kuti ndi osasinthika ndipo sangakumbukiridwe – mosasamala kanthu momwe zinthu zilili.

Pankhwana ya Yobu, panalinso china, china chimene chinali pa chiwopsezo kupatula mbiri ya Mulungu – dziko lathu. Satana anali ndi malingaliro olanda dziko lathu lapansi (dera lomwe adani amakhala) ngati ufumu wake odziyimira pawokha: “Nati Yehova kwa Satana, Ufuma kuti? Nayankha Satana kwa Yehova, nati, Kupitapita m’dziko ndi kuyendayenda m’mwemo” (Yobu 1:7).

Ngati tingatenge ufulu kuti tiwerenge mosamala kwambiri, Satana kwenikweni anali kunena kwa Mulungu, “Ndakhala ndikuyenda padziko lonse lapansi ndipo zikuwoneka kuti ndiri ndi mgwirizano wonse pa zifukwa zanga; ndikuti ndiri ndi ufulu wolamulira padziko lapansi.” Mu zochitika zonse zotsatira, Mulungu (mwamwayi) adakhala patsogolo pa Satana – adadziwa mtumiki wake wodalirika. Yobu anakhalabe wokhulupirika kwa Mulungu ngakhale anazunzidwa kwachiwiri kwadzawoneni kwambiri mu mbiri ya mu Baibulo. Pamapeto pake, Mulungu adasunga moyo wa Yobu, “ndipo Yehova anacotsa ukapolo wa Yobu, pamene anapempherera mabwenzi ace” (Yobu 42:10), omwe anali pachiwopsezo chachikulu kuposa Yobu – samamudziwa Mulungu.

Buku la Yobu limatipatsa chidziwitso cha nkhwana ya uzimu yomwe ikupitirira lero pakati pa Mulungu ndi mphamvu za mdima. Tikawona m’aganizo mwathu zinthu zina zosamveka bwino

momwe Mulungu amadziwonera bwino kwambiri, tidzayamba kudzindikira kukula kwa vuto lomwe akukumana nalo.

Ife monga anthu anzeru sitiri tokha mdziko lathu lino. Pali zolengedwa zambiri za uzimu zomwe zikugawana malo nafe – Satana ndi gulu lake la nkondo la angelo omwe anagwa. Popeza mikhalidwe yathu yadyera komanso ya ziwanda, dziko lathu lapansi ndiye nsanja lazowombana zingapo zofuna zathu tsiku ndi tsiku. Chomwe chiri chovuta kwambiri kuti timvetse ndi momwe Satana ndi gulu lake la ziwanda angalepheretse kapena kutsutsa Mulungu.

Zimakhala zosasangalatsa kwa ife tikadzindikira kuti Mulungu sakhala ndi ulamuliro pa chilichonse pa dziko lapansi. Komabe, Mulungu safuna kulamulira miyoyo yathu, kapenanso kuti sichikhalidwe chake kutero; adatirenga tikhale anthu anzeru – osati zidole.

Kumayambiriro a buku la Yobu, atatu womwe adatenga nawo gawo lalikulu awonetsedwa: Mulungu, Satana, ndi Yobu. Kumapeto kwa bukuli Satana sakutchulidwa ndi dzina. Chifukwa chiyani sangapezeke pamapeto omaliza a kukumana kwakukulu ndi Mulungu.

Mutu wonse cha makumi anayi ndi chimodzi a Yobu umayang’ana cholengedwa chodabwitsa chomwe Mulungu amatcha “Ng’ona” Kodi Ng’ona ndi chiyani kapena kuti ndi ndani? Kodi mu Baibulo muli mfundo zotithandiza kudziwa chirombo chimenechi? “Tsiku limenelo Yehova ndi lupanga lace lolimba ndi lalikuru ndi lamphamvu adzalanga nangumi njoka yotamanga, ndi nangumi njoka yopindika-pindika; nadzapha cing’ona cimene ciri m’nyanja” (Yesaya 27:1). Kodi “njoka yoboola,” “njoka yopotoka,” ndi “chinjoka chomwe chiri m’nyanja” chikuyimira ndani? “Ndipo cinaponyedwa pansu cinjoka cacikuru, njoka yokalambayo, iye wochedwa mdierekezi ndi Satana, wonyenga wa dziko lonse; cinaponyedwa pansu kudziko, ndi angelo ace anaponyedwa naye pamodzi” (Revelation 12:9). Tiyeni tiwone Yobu mutu makumi anayi ndi chimodzi ndi diso kuti tiwone zikhalidwe za usatana pofotokozera cholengedwa ichi:

Kodi ukhoza kukoka ng'ona ndi mbedza? Kapena kukanikiza kalandira wace ndi cingwe? Kodi ukhoza kumanga m'mphuno ndi mlulu? Kapena kuboola nsagwada wace ndi momba? Kodi idzacurukitsa mau akukupembedza? Kapena idzanena nawe mau ofatsa? Kodi idzapangana ndi iwe, Kuti uitenge ikhale kaopolo wako wacikhalire? Kodi udzasewera nayo ngati mbalame? Kapena udzaimangira anamwali ako kuti aiwete? Kodi opangana malonda adzaitatsa? Adzaigawana eni malonda? Kodi udzadzaza khungu lace ndi nchetho, Kapena mutu wace ndi miomba? Isanjike dzanja lako; Ukakumbukila nkhondoyi, sudzateronso. Taona, ciyembekezo cako ca pa iyo cipita pacabe. Kodi sadzatenga nkhawa munthu pakungoiona? Palibe wolimba mtima kuti adzaiputa. Ndipo ndaniyo adzaima pamaso pa Ine? Ndaniyo anayamba kundipatsa Ine kuti ndimthokoze? Ziri zonse pansu pa thamboponse ndi zanga. Sindikhala cete osachula ziwalo za ng'onayo, Ndi mbiri ya mphamvu yace, ndi makonzedwe ace okoma. Ndani adzasenda cobvala cake cakunja? Adzalowa ndani ku mizere iwiri ya mano ace? Adzatsegula ndani zitseko za pakamwa pace? Mano ace aopsa pozungulira pao. Mamba ace olimba ndiwo kudzitama kwake; Amangika pamodzi ngati okomeredwatu. Alumikizana lina ndi linzace, Mphepo yosalowa pakati pao. Amamatirana lina ndi linzace, Agwirana osagawanikana. Pakuyetsemula ing'anipitsa kuunika, Ndi maso ace akunga zikope za m'mawa. M'kamwa mwace muturuka miuni, Mbaliwali za moto zibukamo. M'mphuno mwace muturuka utsi, Ngati nkhalu yobwadamuka ndi moto wa zinyatsi. Mpweya wace uyatsa makara, Ndi m'kamwa mwace muturuka lawi la moto. Kukhosi kwace kukhala mphamvu, Ndi mantha abvumbuluka patsogolo pace. Nyama yace yopsapsala igwirana lkwima pathupi pace yosagwedezeka. Mtima wace ulimba ngati mwala, Inde ulimba ngati mwala

mphero. Ikanyamuka, amphamvu acita mantha; Cifukwa ca kuopsedwa azimidwa nzeru. Munthu wakuiyamba ndi lupanga, ligoma; Ngakhale nthungo, kapena mubvi, kapena mkondo. Citsulo iciyesa phesi, Ndi mkuwa ngati mtengo woola. Mubvi suithawitsa, Miyala ya pacoponyera iisandutsa ciputu. Zibonga ziyesedwa ciputu, Iseka kuthikuza kwace kwa nthungo. Kumimba kwace ikunga mapule akuthwa, Itasalala kuthope ngaticopunthira. Icititsa nthumbwinthumbwi pozama ngati nkhalu, Isanduliza Nyanja ikunge mafuta. Icititsa mifunde yonyezimira pambuyo pace; Munthu akadati pozama pali ndi imvi. Pa dziko lapansi palibe cina colingana nayo, Colengedwa copanda mantha. Ipenya ciri conse codzikuzi, Ndiyo mfumu ya zodzitama zonse. (Yobu 41)

Mulungu amagwiritsa ntchito mawu ophiphiritsa m'mutu uno kufotokoza za mdani wamphamvu kwambiri komanso opanda chifundo kotero kuti sitingathe kulimbana ndi mdani ameneyu patokha. Mulungu akuchita nkondo yayikulu ndi mdani woopsa kwambiri, komabe ali otsimikiza mtima kutimenyera nkondoyi m'malo mwathu popanda kugwiritsa mphamvu nthawi iliyonse kapena muli monse momwe zingakhalire.

Satana wapangitsa Mulungu kuwonekera monga momwe iye aliri: wokwiya wobwezera, wosakhululuka, wokakamiza, woweruza milandu, komanso wovuta, pomwe nthawi yomweyo, akuwonekera kwa ife ngati “m'ngelo wakuunika” (2 Akorinto 11:14), koma Mulungu amawona bwino zomwe ife singathe kuziwona – monga wonyengayo aliri waluso pamachitidwe ake.

Ndikulongosola kophiphiritsira kwa mdani wa Mulungu, titha kumvetsetsa za nkondo ya tsiku ndi tsiku yomwe Mulungu akumenyera aliyense wa ife. Mulungu amalowererapo kuti achotse ana ake mu njira yovulaza pomwe Satana adzadutsa malire ake mwakufuna kwake kuti alepheretse kapena kuwononga iwo omwe akumvera Mzimu Woyera. Zina mwa zinthuzi zikuwoneka kwa ife,

pomwe zambiri siziri choncho. Chifukwa chake, Mulungu apitirizabe kumuimba mulandu tsiku ndi tsiku chifukwa cha mavuto omwe timawona mdziko lathu. Tikhulupirira kuti zomwe Yobu adakumana nazo zitithandiza kuzindikira kuti Mulungu sangateteze ngozi zonse, masoka aliwonse, matenda aliwonse, kapena imfa iriyonse nthawi yomweyo alemekeza ufulu wa zolengedwa zake zanzeru.

Palinso chinthu china chomwe Mulungu amawona bwino. Ndi yekhayo amene alibe chiyambi – pamene Satana ali. Satana ndi cholengedwa chomwe chidasankha choyipa, ndipo choyipa chimadalira zabwino zokha kuti chikhalepo. Pamene zolengedwa za nzeru m'chilengedwe chonse zimvetsetsa chowonadi ichi, potengera kukhulupirika kwa Mulungu, adzalola Satana, woyambitsa zoyipa, kuti adziwononge yekha; chingakhale chabwino bwanji kuposa icho?

*Usaope, pakuti Ine ndiri pamodzi ndi iwe; usaopsyedwe,
pakuti Ine ndine Mulungu wako; ndidzakulimbitsa; inde,
ndidzakucirikiza ndi dzanja langa lamanja la cilungamo.*

— Yesaya 41:10

Chifukwa Chake Timawerenga Baibulo Molakwika

Baibulo silinalembedwe ngati lembetso kuchokera kwa Mulungu, “koma anthu oyera a Mulungu analankhula, motsogozedwa ndi Mzimu Woyera” (2 Petro 1:21). Baibulo linalembedwa ndi amuna pogwiritsa ntchito mawu awo komanso malingana chikhalidwe, kumene akuchokera, ndi umunthu wa wolembe aliyense.

Chifukwa chiyani nthawi zambiri zimawoneka mu Baibulo kuti Mulungu ndiye wowonga? Kuti tiyankhe funsoli kungakhale kothandiza poyamba kulingalira miyambo ya chipembedzo ya mayiko akale otchulidwa mu Baibulo. Chinthu chimodzi chikuwonekera – anthu achi Israyeli, anthu otchulidwa mu nkhanayi, anali atazunguliridwa ndi mafano. Ngakhale anali kuwachenjeza momveka bwino kuti apewe kupembedza mafano, anali kutengera zochitika za olambira mafano. Kumvetsetsa kwa a Israyeli kunasokonekera chifukwa cha chikhalidwe chofala.

Mulungu adalalaka kudziulula kwa anthu. Komabe, kuwaululira kwathunthu ulemerero wamakhalidwe ake kwa iwo kukadawatengera kutali. Mulungu adadzitsitsa kufikira anthu omwe amafuna kuwafikira, ndipo amafunika kuyankhula chiyankhulo chawo kuti atero. Anali wokonzeka kuti anthu asamumvetse polumikizana ndi anthu achi Israyeli kuti awapulumulutse kuti asadziwononge okha.

Kuphatikiza apo, m’maiko akale otchulidwa mu Baibulo, anthu omwe amatsogozedwa ndi ziwanda amapanga milungu yomwe inali ya chiwawa komanso yosachedwa kupsa mtima. Amakhulupirira kuti mavuto omwe amakumana nawo amayambitsidwa ndi milungu yomkwiyayi. Chotsatira chake, anthu adzaza nazo nsembe kuti atonthoze mkwiyo wawo ndipo adayigwadira pa mapwando awo achipembedzo.

Mu Chipangapo Chakale, Satana satchulidwa kwambiri, ndiye amene ali ndi mlandu wa mavuto ndi imfa mdziko lathu. Zikanakhala kuti Satana ndi amene anayambitsa mavuto amene anthu amakumana nawo, maganizo awo akanakhala kwa iyeyo osati kwa Mulungu. A Israyeli akadaganizira Satana ngati mulungu wina amene anali ndi mphamvu zodabwitsa pa mphamvu za chilengedwe. Izi zikanawatsogolera kuti kupereka nsembe kwa iye, ndipo mwakutero akanapembedza Satana m'malo mwa Mulungu.

Mulungu anafuna kuletsa izi kuti zisachitike polola podziwonetsera ngati gwero osati la zabwino zokha zomwe anthu amalandira komanso zoyipa. Mulungu anali wodera nkhawa anthu ndi zotsatira zake kuti kuululidwa msanga kwa wowonongayo kuwakhudza kwambiri kuposa kukhuzidwa kwa mbiri yake. Ngakhale ndi kudzichepetsa kumeneku kwa Mulungu, anthu adaperekabe ulemu kwa ziwanda kudzera pakupembedza mafano: “Anapereka nsembe kwa ziwanda, osati kwa Mulungu” (Deuteronomo 32:17).

A Israyeli akale sanali wokonzeka kuwululidwa momveka bwino za chikhalidwe cha Mulungu chofatsa ndi chachikondi. Akadamukana Mulungu palimodzi akadabwera kwa iwo kuwonekera monga aliri – chikondi chopanda dyera. Ankafuna mulungu amene adzawamenyera nkhondo komanso kuchitira nkhanza adani awo. A Israyeli ankafuna mulungu wofanana ndi iwo. M'malo momvomereza chowonadi chakuti “Mulungu adalenga munthu mu chifanizo chake” (Genesis 1:27), adatsimikiza mtima kupanga mulungu mu chifanizo chawo. Izi zimatiipatsa ife (ngati mukufuna kutero) kumvetsetsa kwa momwe anthu akhala akugwirizanirana ndi mibadwo yonse mpaka pano.

Chifukwa Chake Sitimamumvetsa Mulungu

Pamene Mulungu anayenda pakati pathu, sanazindikiridwe kapena kulandiridwa ndi achipembedzo:

Ndipo pamene iwo analikuturuka, onani, anabwera naye kwa Iye munthu wosalankhula, wogwidwa nciwanda. Ndipo m'mene cinaturutsidwa ciwandaco, wosalankhulayo analankhula, ndipo makamu a anthu anazizwa, nanena, Kale lonse sicinaoneke comweco mwa Israyeli. Koma Afarisi analinkunena, Aturutsa ziwanda ndi mphamvu zace za mfumu ya ziwanda. Ndipo Yesu anayendayenda m'mizinda yonse ndi midzi, namaphunzitsa m'masunagoge mwao, nalalikira uthenga wabwino wa Ufumuwo, naciritsa nthenda iri yonse ndi zofoka zonse. (Mateyu 9:32-35)

Mawu otsatirawa a Yesaya akugwira ntchito moyenera kwa iwo omwe amatsutsa Yesu kuti akuchita m'gwirizano ndi Satana: “Tsoka kwa iwo amene ayesa zoipa zabwino, ndi zabwino zoipa; amene aika mdima m'malo mwa kuyera, ndi kuyera m'malo mwa mdima; amene aika zowawa m'malo mwa zotsekemera, ndi zotsekemera m'malo mwa zowawa! Tsoka kwa iwo amene adziyesera anzeru ndi ocenjera” (Yesaya 5:20-21).

Anali m'dziko lapansi, ndi dziko linalengedwa ndi Iye, koma silinamzindikira Iye. Anadza kwa zace za Iye yekha, ndipo ace a mwini yekha sanamlandira Iye. (Yohane 1:10-11)

Ndimeyi sikuti ikungonena za mbiri yakale. Mulungu akupitirabe kusazindikirika, kusamvetsedwa, komanso kusadziwika. Sitimamvetsa Mulungu chifukwa chakukonda kwathu kuganiza molakwika kuti Iye ali wodzikonda monga ife:

Koma munthu wa cibadwidwe ca umunthu salandira za Mzimu wa Mulungu: pakuti aziyesa zopusa; ndipo sakhoza kuzizindikira, cifukwa ziyesedwa mwauzimu. (1 Akorinto 2:14)

Mtundu wa anthu uli ndi zokopa za chipembedzo cha kunja. M'malo mwake chomwe tikusowa ndi kusinthanitsa kudzikonda kwathu ndi chikondi cha Mulungu. Lingaliro losiya kudzikonda likuwopseza kwambiri “munthu wachibadwidwe.” Chipembedzo cha kunja chimawoneka ngati chotetezeka kwambiri, koma chitetezo cha mtunduwu ndi chinyengo; chipembedzo cha kunja nthawi zambiri chimagwiritsidwa ntchito kubisalira Mulungu.

Ndipo Afarisi anadza kwa Iye, namuyesa, nanena, Kodi nkololedwa kuti munthu acotse mkazi wake pa cifukwa ciri conse? Ndipo Iye anayankha, nati, siminawerenga kuti Iye amene adalenga anthu paciyambi, anawalenga iwo mwamuna ndi mkazi, nati, Cifukwa ca ici mwamuna adzasiya atate wace ndi amace, nadzaphatikizana ndi mkazi wace, ndipo awiriwo adzakhala thupi limodzi? Coteru kuti salinso awiri koma thupi limodzi. Cifukwa cace ici cimene Mulungu anacimanga pamodzi, munthu asacilekanitse. Iwo anena kwa Iye, Nanga cifukwa ninji Mose analamulira kupatsa kalata wa cilekaniro, ndi kumcotsa? Iye ananena kwa iwo, Cifukwa ca kuuma mtima kwanu, Mose anakulolezani kucotsa akazi anu; koma paciyambi sikunakhala comweco. (Mateyo 19:3-8)

Zambiri za Chipangano Chakale zimawonetsa kuyesetsa kwa Mulungu kuti ayandikire pafupi ndi anthu ouma mtima. Mulungu samamvetsedwa bwino mu mavesi omwe adakwaniritsa zofuna za anthu m'malo mowasiya opanda chiyembekezo. Ndife omwe timasowa chifundo – osati Mulungu. Komabe nthawi zonse timalakwitsa kulumikizana kwa Mulungu ndi anthu opanda chifundo mu Chipangano Chakale. Zotsatira zako, tikutsutsa Mulungu kuti amalekerera ukapolo ndi mitala, amalimbikitsa nkhondo zakugonjetsa, kulamula kuphana komanso kupereka zilango

zazikulu kwa oswa malamulo. Timapanga izi chifukwa sitimvetsetsa kukula kwa vuto lomwe limakhudzana ndi kuuma mtima kwa anthu komwe Mulungu anali kukumana nako polumikizana ndi Israyeli wakale.

Yesu, mu Ulaliki wa pa Phiri, adakweza lamuloli, ndi kuliyika motsatira lamulo la chikondi:

Munamva kuti kunanenedwa, Diso kulipa diso, ndi dzino kulipa dzino: koma ndinena kwa inu, Musakanize munthu woipa; koma amene adzakupanda iwe pa tsaya lakumanja, umtembenuzire linanso. Ndipo kwa iye wofunakupita nawe kumlandu ndi kutenga Malaya ako, umlolezenso copfunda cako. Ndipo amene akakukakamiza kumperekeza njira imodzi, upite naye ziwiri. Kwa iye wopempha iwe umpatse, ndipo kwa iye wofuna kukukongola usampotolokere. (Mteyu 5:38-42)

Mwa mawu awa, Yesu adalongosola chifuniro changwirowo cha Mulungu mosiyana ndi kusintha kwa zofuna za anthu ouma mitima.

Yesu anati kwa iwo, Mulungu akadakhala Atate wanu mukadakonda Ine; pakuti Ine ndinaturuka, ndi kucokera kwa Mulungu; koma Iyeyu anandituma Ine. Simuzindikira malankhulidwe anga cifukwa ninji? Cifukwa simungathe kumva mau anga. Inu muli ocokera mwa atate wanu mdierekezi, ndipo zolalalaka zace za atate wanu mufuna kucita. Iyeyu anali wambanda kuyambira paciyanji, ndipo sanaima m'coonadi, pakuti mwa iye mulibe coonadi. Pamene alankhula bodza, alankhula za mwini wace; pakuti ali wabodza, ndi atate wace wa bodza. Koma Ine, cifukwa ndinena coonadi, simukhulupirira Ine. Ndani mwa inu anditsutsa Ine za cimo? Ngati ndinena coonadi, simundikhulupirira Ine cifukwa ninji? Iye wocokera kwa Mulungu amva zonena za Mulungu; inu simumva cifukwa cakuti simuli a kwa Mulungu. Ayuda anayankha nati kwa Iye, Kodi

sitinenetsa kuti Inu ndinu Msamariya, ndipo muli ndi ciwanda? (Yohane 8:42-48)

Yesu anati kwa atsogoleri achipembedzo, “Inu ndinu a atate wanu mdierekezi.” Atate wawo anali mdierekezi chifukwa adatengera cithunzi cholakwika kwa Satana cha Mulungu ndipo amakana kusintha kulikonse ku chithunzichi.

Ndipo anaika pamwamba pamutu pace liwongo lace lolembedwa: UYU NDI YESU MFUMU YA AYUDA. Pamenepo anapacika pamodzi ndi Iye acifwamba awiri, mmodzi ku dzanja lamanja, ndi wina kulamanzere. Ndipo anthu akupitirirapo anamcitira mwano Iye ndi kupukusa mitu yao, nati, Nanga Iwe wopasula Kachisi, ndi kummanganso masiku atatu, tadzipulumutsa wekha; ngati uli Mwana wa Mulungu, tatsika pamtandapo. Comweconso ansembe akuru, pamodzi ndi alembi ndi akuru anamcitira cipongwe, nati, Anapulumsa ena, sangathe kudzipulumutsa yekha. Ndiye Mfumu ya Ayuda; atsike tsopano pamtandapo, ndipo tidzamukhulupirira Iye. Amakhulupirira Mulungu; Iye ampulumutse tsopano, ngati amfuna; pakuti anati, Ine ndine Mwana wa Mulungu. (Mateyu 27:37-43)

Iwo amene adanyoza Yesu pa mtanda adagwiritsa ntchito njira yomweyo Satana adagwiritsa ntchito mchipululu pomyesa Khristu: “Ngati muli Mwana wa Mulungu” (Mateyu 4:3).

Ndipo palibe munthu atsanulira vinyo watsopano m'matumba akale; cifukwa ngati atero, vinyo watsopanoyo adzaphulitsa matumba, ndipo ameneyo adzatayika, ndi matumba adzaonongeka. Koma kuyenera kutsanulira vinyo watsopano m'matumba atsopano. (Luka 5:37-38)

Yesu, mu fanizoli, akuyerekezera chiphunzitso chake chatsopanocho ndi “vinyo watsopano” wophulitsa “mabotolo akale.” Mwa mawu ndi chitsanzo chake Yesu adalongosola momveka bwino za chikondi cha Mulungu chomwe chinali chosiyana kwambiri ndi chithunzi cholakwika cha Mulungu “vinyo wakale” wophunzitsidwa wan dihunzitsi achipembedzo “mabotolo akale” omwe adakumana nawo. Malingaliro awiri osiyanawa sakanakhoza kusakanizidwa pamodzi. Zirinso chimodzimodzi lero. Chithunzi cha mulungu wachiwawa chiyenera kupita kuti chipatse malo Mulungu wathu wofatsa mu malingaliro athu.

Momwe Mulungu Amawonongera

Chimodzi mwazitsanzo zomveka bwino za momwe Mulungu amawonongera chikupezeka mu buku la 1 Mbiri. Sauli mfumu ya Israyeli anali kunyalanyaza uphungu wa Mulungu, womulankhula kudzera mwa mneneri Samueli, kuti asiye njira yowononga. Sauli anayesera kangapo kupha Davide, mtumiki wake wokhulupirika. Analinso mlandu wopha anembe a Nobu, komanso adakonza uphungu ndi mfiti. Sauli anali atabvulazidwa pa nkondo ndi Afilisiti, ndipo adachita mantha ndi zomwe zingachitike akagwidwa. Motsimidwa, “Sauli anatenga lupanga, naligwera” (1 Mbiri 10:4).

Wonani momwe Baibulo likumalidzira nkhani yowopsayi ya imfa ya Sauli:

Momwemo Sauli anafa, cifukwa cha kulakwa analakwira Yehova, kulakwira mau a Yehova amene sanawasunga; ndiponso cifukwa ca kufunsira wobwebweta, kufunsirako, osafunsira kwa Yehova; cifukwa cace anamupha, napambutsira ufumu kwa Davide mwana wa Jese. (1 Mbiri 10:13-14)

Zikuwonekeratu kuti pa kufa kwa Sauli chinthu chokhacho chomwe tikuwona Mulungu akuchita ndikulola Sauli apite mu njira zake ndi kukumana ndi zotsatirapo za zomwe adachita. Chimene chinapangitsa imfa ya Sauli ndi kudzipha, osati kuphedwa, komabe Baibulo limanena kuti Mulungu adamupha. Mawu omwe agwiritsidwa ntchito pano pofotokoza zomwe Mulungu anachita ndi osiyana ndi tanthauzo lotanthauzira mawu. Ichi sichitsanzo chokha. Mu mutu wotsatira mawu a mu Baibulo monga ukali, mkwiyo, nsanje awunikidwa. Malemba amapereka tanthauzo losiyana ndi momwe amagwiritsidwira ntchito pofotokoza njira za Mulungu ndi malingaliro a Mulungu.

Funani Yehova popezeka lye, itanani lye pamene ali pafupi; woipa asiye njira yace, ndi munthu wosalungama asiye maganizo ace, nabwere kwa Yehova; ndipo Yehova adzamucitira cifundo; ndi kwa Mulungu wathu, pakuti lye adzakhulukira koposa. Pakutimaganizo anga sali maganizo anu, ngakhale njira zanu siziri njira zanga, ati Yehova. Pakuti monga kumwamba kuli kutari ndi dziko lapansi, momwemo njira zanga ziri zazitari kupambana njira zanu, ndi maganizo anga kupambana maganizo anu.

— Yesaya 55:6-9

Kodi Ukali Wa Mulungu N'chiyani?

Funso la ukali wa Mulungu limatidabwitsa ife ambiri pamene timawerenga Chipangano Chakale. Pali zonena zambiri za ukali wa Mulungu ndi mkwiyo, koma ukali wake nchiyani? Kuti tiyankhe funso limeneli, zikhala zounikira kuwona zitsanzo zina za mu Baibulo. Kutchulidwa koyamba za ukali wa Mulungu kunali pamene adalamula Mose kuti atsogolere ana a Israyeli kuchokera ku ukapolo ku Iguputo kupita ku ufulu. Ndi ziti zomwe zidakakamiza Mulungu kuti awonetse ukali wake pa nthawiyo?

Ndipo Mose anati kwa Yehova, Mverani, Ambuye, ine ndine munthu wosowa ponena, kapena dzulo, kapena kale, kapena cilankhulire Inu ndi kapolo wanu, pakuti ndine wa m'kamwa molemera, ndi wa lilime lolemera. Koma Yehova ananena naye, Anampangira munthu m'kamwa ndani? Kapena analenga munthu wosalankhula ndani, kapena wogontha, kapena wamaso, kapena wakhungu? Si ndine Yehova kodi? Ndipo tsopano muka, ndipo Ine ndidzakhala m'kamwa mwako, ndi kukuphunzitsa comwe ukalankhule. Koma anati, Mverani, Ambuye, tumizani pa dzanja la iye amene mudzamtuma. (Eksodo 4:10-13)

Mose anali ndi mantha kupita kukawonekera pa maso Farao yekha ndipo anapempha womulankhulira. Kodi Mulungu adayankha motani?

Pamenepo mkwiyo wa Yehova unamyakira Mose, ndipo anati, Nanga Aroni Mlevi mbale wako sialipo kodi? Ndidziwa kulankhula alankhula. Ndipo, taona, aturuka adzakomana ndiwe; ndipo pakuona iwe adzakondwera m'mtima mwace. (Eksodo 4:14)

Kodi Mulungu adawonetsa bwanji ukali wake? Mwa kupereka zomwe amafuna. Tiyeni tione mavesi ena a Baibulo okhudzana ndi ukali wa Mulungu:

Ndipo anthu osokonezeka ali pakati pao anagwidwa naco cilakolako; ndi ana a Israyeli omwe analiranso, nati, Adzatipatsa nyama ndani? Ndipo Mose anamva anthu alikulira m'mabanja ao, yense pakhomo pa hema wace; ndipo Yehova anapsa mtima ndithu, ndipo kudamuipira Mose. Ndipo kudachokera mphepo kwa Yehova, nidza nazo zinziri zocokera kunyanja, nizitula kucigono, ulendo wa tsiku limodzi dera lino, ndi ulendo wa tsiku limodzi dera lina, pozungulira pa cigono, ndipo zinabisa nthaka ngati muyeso wa mikono iwiri. Ndipo anthu anauka tsiku lonse, ndi usiku wace wonse, ndi mawa lace lonse, nakusa zinzirizo; wokusa pang'ono anakusa zodzaza mahomeri khumi, ndipo anadziyanikira izi pozungulira pa cigono. (Numeri 11:4, 10, 31-32)

Pazochitikazi, tikupezanso ukali wa Mulungu ukutchulidwa. Anachitanji? Anapatsa anthu zomwe amafuna.

Ndipo kunali, pamene Samueli anakalamba, anaika ana ace amuna akhale oweruza a Israyeli. Dzina la mwana wace woyamba ndiye Yoeli, ndi dzina la waciwiri ndiye Abiya; ndiwo oweruza a ku Beereseba. Ndipo ana ace sanatsanza makhalidwe ace, koma anapambukira ku cisiriro, nalandira cokometsera mlandu, naipitsa kuweruza. Pamenepo akuru onse a Israyeli anasonkhana, nadza kwa Samueli ku Rama; nanena naye, Taonani, mwakalamba, ndipo ana anu satsanza makhalidwe anu; tsono, mutilongere mfumu kuti ikatiweruze, monga umo mucitidwa m'mitundu yonse ya anthu. Koma cimenezi sicinakondweretse Samueli, pamene iwo anati, Tipatseni mfumu kuti itiwereze. Ndipo Samueli anapemphera kwa Yehova. Ndipo

Yehova ananena ndi Samueli, Umvere mau onse anthuwo alikulankhula nawe; popeza sindiwe anakukana, koma ndine anandikana, kuti ndisakhale mfumu yao. (1 Samueli 8:1-7)

Mulungu adatumiza uthenga kwa anthu kudzera mwa mneneri wake Samueli kupereka zifukwa zambiri zomwe sizingakhale zabwino kuti iye apereke pempho lawo la mfumu. Kodi anamvera Samueli?

Koma anthu anakana kumvera mawu a Samueli; nati, lai, koma tifuna kukhala nayo mfumu yathu; kuti ifenso tikafanane nao anthu amitundu yonse; kuti mfumu yatthuyo ikatiweruze, ndi kuturuka kutitsogolera, ndi kuponya nafe nkondo zathu. (1 Samueli 8:19-20)

Kodi Mulungu anawayankha bwanji anthuwo? “Ndipo Yehova anati kwa Samueli. Mvera mawu awo, nuwapangire iwo mfumu” (vesi 22). Tidziwa bwanji kuti Mulungu anawapatsa mfumu mwa ukali? Mneneri Hoseya, poyang’ana m’mbuyo pa chochitika ichi cha mbiri, akutipatsa malingaliro a Mulungu pa gawo lomwe adachita povomereza zopempha za anthu:

Israyeli, cikuononga ndi ichi, cakuti utsutsana ndi Ine, cithandizo cako. Iri kuti mfumu yako ikupulumutse m’midzi yako yonse? Ndi oweruza ako amene unanena za iwo, Ndipatseni mfumu ndi akalonga? *Ndinakupatsa mfumu mu mkwiyo wanga*; ndinamcotsanso m’ukali wanga. (Hoseya 13:9-11)

Nkhani zitatu za m’malemba izi zikuwonetsatu kuti ukali wa Mulungu udali wofanana ndi kupatsa a Israyeli zome amafuna pomwe sizinali zabwino kwa iwo kutero. Izi zikuyenera kukhala zokwanira, kuwonetsa ukali wa Mulungu ukhoza kufotokozedwa, kuchokera mu Baibulo ngati china chosiyana ndi tanthauzo lomwe likupezeka mu chothanthauzira mawu. Komabe, pali zina zambiri kuposa izi. Kodi chinachitika ndi chiyani Yesu atakwiya?

Ndipo analowanso m'sunagoge; ndipo munali munthu m'menemo ali ndi dzanja lace lopuwala. Ndipo anamuyang'ana Iye, ngati adzamuciritsa dzuwa la Sabata; kuti ammange mlandu. Ndipo ananena munthu ali ndi dzanja lopuwala, Taimirira pakati. Ndipo ananena kwa iwo, Kodi nkolodwa dzuwa la Sabata kucita zabwino, kapena zoipa? Kupulumutsa moyo kapena kupha? Koma anakhala cete. Ndipo m'mene anawaunguza ndi mkwiyo, ndi kumva cisoni cifukwa ca kuuma kwa mitima yao, ananena kwa munthuyo, Tambasula dzanja lako. Ndipo analitambasula; ndipo linacira dzanja lace. Ndipo Afarisi anaturuka, ndipo pomwepo anamkhalira upo ndi Aherode, wakumuononga Iye. (Marko 3:1-6)

Uku ndiko kumana komwe Yesu adakumana nako ndi Afarisi. Kuletsa kwawo malamulo kunkaletsa machiritso pa tsiku la Sabata. Yesu, powerenga mitima yawo, “adawunguzawunguza ndi ukali.” Kodi Yesu anali ndi ukali wotani? Mtundu omwe umanenedwa kuti “akumva chisoni chifikwa cha kuuma kwa mitima yawo.” Yesu anali ndi chisoni kapena kuti anakhumudwa kwambiri chifukwa chosowa chikondi ndi chisoni chosonyezedwa ndi atsogoleri achipembedzo opanda chifundo amenewa kwa munthu amene anali ndi dzanja lopuwala. Tingapezenso chiyani mu Baibulo za ukali wa Mulungu ndi mkwiyo wake?

Pakuti mkwiyo wa Mulungu wocokera Kumwamba, uonekera pa cisapembedzo conse ndi cosalungama ca anthu, amene akanikiza pansu coonadi m'cosalungama cao. (Aroma 1:8)

Kodi mkwiyo wa Mulungu umaululidwa motani?

Chifukwa cace Mulungu anawapereka iwo m'zilakolako za mitima yao, kuzonyansa. (Aroma 1:24)

Chifukwa ca ici Mulungu anawapereka iwo ku zilakolako za manyazi. (Aroma 1:26)

Ndipo monga iwo anakana kukhala naye Mulungu m'cidziwitso cao, anawapereka Mulungu ku mtima wokanika, kukucita zinthu zosayenera. (Aroma 1:28)

Mkwiyo wa Mulungu umatanthauzidwa pano ngati kuwasiya kapena kuwapereka – m'njira ina, Mulungu akupatsa anthu ufulu wodzirekanitsa ndi Iye yekha. Osati kwenikweni mkwiyo wa chiwonongeko chobwezera chomwe nthawi zambiri timapereka ku nkhani ya Mulungu. Tiyeni tiwone ndime zina za Chipangano Chakale.

Ndipo anthu anauka tsiku lonse, ndi usiku wace wonse, ndi mawa lace lonse, nakusa zodzaza mahomeri khumi; ndipo anadziyanikira izi pozungulira pa cigono. Nyamayi ikali pakati pa mano, asanaitafune, Mulungu apapsa mtima pa anthuwa, ndipo Yehova anawakantha anthu ndi kukantha kwakukuru ndithu. (Numeri 11:32-33)

Tikubwerera kuno ku nkhani ya zinziri zomwe Mulungu adapatsa anthu mokwiya. Panali zotsatira za chilengedwe chifukwa chakususuka kwa anthu: “AMBUYE adakantha anthuwo ndi mliri waukulu.”

Tiyenera kudziwa kuti nyama yatsopano ya zinziri singakhale nthawi yayitali mu chipululu pomwe a Israyeli anali atamanga misasa. Nyamayo yikanawonongeka msanga ndikupangitsa isakhale yoyenera kudya anthu. Poganzira izi, kodi ndi mliri wanji womwe ukadakhala wotsatira? Kupatsidwa tizirombo toyambitsa matenda toyenera komanso makhalidwe woyenera, poyizoni wazakudya ndi vuto lowopsa kwambiri: “Ndipo anatcha malowo Kibrothhattaavak (manda a chilakolako) chifukwa pamenepo adayikirapo anthu omwe adasilira” (vesi 34). Kodi “mkwiyo wa AMBUYE” unali chiyani? Kodi sizikutsatira molondola kuti mkwiyo wa Mulungu sunali kulowererapo muzochitika ndi zoyambitsa?

Pamenepo ndidzawapsera mtima tsiku ilo, ndipo ndidzawataya, ndi kuwabisira nkhope yanga, ndipo adzathedwa, ndi zoipa ndi zobvuta zambiri zidzawafikira; kotero kuti adzati tsiku lija, Sizitifikira kodi zoipa izi popeza Mulungu wathu sakhala pakati pa ife? Koma Ine ndidzabisatu nkhope yanga tsiku lija cifukwa ca zoipa zonse adazicita; popeza anadzitembenukira milungu yina. (Deuteronomo 31:17-18)

Kodi zimatanthauza chiyani Mulungu akabisa nkhope yake? “Kodi zoipa izi sizitigwera chifukwa Mulungu wathu Sali pakati pathu?” Ichi ndiye chilankhulo chomwe chimafotokoza kusalowererapo kwa Mulungu. Chifukwa chiyani adati abisa nkhope yake? “Chifukwa cha zoyipa zonse zomwe adachita, potembenukira kwa milungu ina,” Ndipo zotsatira zake zingakhale zotani? “Adzawonongedwa, zoyipa zambiri ndi zovuta zidzawagwera.” Anthuwo atatembenukira kwa milungu ina, apatuka kwa Mulungu woona, ndipo analephera kuwateteza ku zotsatira zosapeweka.

Ndipo ana a Israyeli anacita coipa pa maso pa Yehova, natumikira Abaala; nasiya Yehova Mulungu wa makolo ao, amene adawaturutsa m’dziko la a Igupto, natsata milungu ina, ya mitundu ya anthu okhala pozungulira pao, naigwadira; nautsa mkwiyo wa Yehova. Ndipo anasiya Yehova, natumikira Baala ndi Asitaroti. Pamenepo mkwiyo wa Yehova unayakira Israyeli, ndipo anawapereka m’manja a ofunkha kuti awafunkhe; nawagulitsa m’dzanja la adani ao akuwazungulira osakhonzanso iwowo kuima pamaso pa adani ao. (Oweruza 2:11-14)

Ndimeyi ikufotokoza zakupitirira kwa anthu kupatuka kwa Ambuye. Apa Mulungu “adawapereka m’manja mwa ofunkha” ndipo “adawagulitsam’manja mwa adani awo.” Uku ndi kungokhalanso poyankha ku mavuto. Chifukwa cha mpatuko wawo, Mulungu sanathe kuletsa adani a Israyeli kuti asalowe m’dziko lawo.

Popeza Yehova adzawakantha Aisrayeli monga bango ligwedezeke ndi madzi, nadzazula Aisrayeli m'dziko lino labwino analipatsa makolo ao, nadzawamwazira ku tsidya lija la Frate, popeza iwo anapanga zifanizo zao zokwiyitsa Yehova. Ndipo adzapereka Aisrayeli cifukwa ca macimo a Yerobiamu anacimwawo, nacimwitsa nao Asrayeli. (1 Mfumu 14:15-16)

Apa ukali wa Mulungu (ndi kukantha) ndi kupereka Israyeli wampatuko.

Ndipo anautsa mtima wace ndi malo amsanje ao, Namcititsa nsanje ndi mafano osema. Pakumva ici Mulungu, anakwiya, Nanyozatu Israyeli; Ndipo anacokera cokhalamo ca ku Silo, Cihemaco adacimanga mwa anthu; Napereka mphamvu yace m'ukapolo, Ndi ulemerero wace m'dzanja la msautsi. Naperekanso anthu ace kwa lupanga; Nakwiya naco colandira cace. (Masalmo 78:58-62)

Apa tanthauzo la mkwiyo limaphatikizapo: kusiya, kupereka m'ukapolo, kupereka.

Potero udayaka mkwiyo wa Yehova pa anthu ace, Nanyansidwa Iye ndi colowa cace. Ndipo anawapereka m'manja a amitundu; Ndipo odana nao anacita ufumu pa iwo. (Masalmo 106:40-41)

Mkwiyo wa Mulungu ukufotokozedwa ngati “kuwapereka m'manja mwa acikunja.”

M'kukwiya kwa kusefukira ndinakubisira nkhope yanga kamphindi; koma ndi kukoma mtima kwa cikhalire ndidzakucitira cifundo, ati Yehova Mombolo wako. (Yesaya 54:8)

M'ndimeyi, “kukwiya pang’ono” kumatanthauzidwa kuti Mulungu amabisa nkhope yake “kwakanthawi,” koma kukoma mtima kwa Mulungu ndi chifundo chake kwa ife ndizosatha.

Ndipo ndidzakucotsani inu pamaso panga, monga ndinacotsa abale anu onse, mbeu zonse za Efraimu. Kodi autsa mkwiyo wanga? ati Yehova; kodi sadziutsira okha manyazi a nkhope zao? Cifukwa cace, ati Ambuye Mulungu, Taonani, mkwiyo wanga ndi ukali wanga udzathiridwa pa malo ano, pa anthu, ndi pa nyama, ndi pa mitengo ya m’unda, ndi pa zipatso zapansi; ndipo udzatentha osazima. (Yeremiya 7:15, 19-20)

Mulungu amafunsa, “Kodi akundikwiyitsa? Kodi sadzichititsa okha kuti asokonezeke nkhope zawo?” Mavuto a anthu adabwera chifukwa chotsatira mafano awo osati monga chirango chokera kwa Mulungu.

Senga tsitsi lako, iwe Yerusalemu, nulitaye, nukweze maliro pa mapiri oti se; pakuti Yehova wakana ndi kusiya mbadwo umene aukwiyira. (Yeremiya 7:29)

Pali mavesi ena mu Baibulo omwe amagwiritsa ntchito mawu ofanana, koma awa omwe tawona akuyenera kukhala okwanira kupereka chifukwa chomveka chakuti mkwiyo wa Mulungu suli chilango kuchokera kwa Iye, Mulungu amatipatsa ufulu womulandira kapena kumukana. Mkwiyi wa Mulungu ndi zotsatira za chilengedwe za zosankha zathu zolakwika, pomwe amakamizidwa kutirola kukhala ndi njira yathuyathu. Udindo wa Mulungu nthawi zonse umangokhala wotchulidwa kuti kusiya, kubisa nkhope yake, kugonja, kulolera, kupereka, ndi matchulidwe ena ofanana.

Polengeza pamaso pa Mose, Mulungu sanatchule mkwiyo kakena ukali monga zina za khalidwe lake: “Ndipo Yehova anapita pamaso pace, naimapo, Yehova, Yehova, Mulungu wachifundo ndi wacisomo, wolekereza, ndi wa ukoma mtima wocuruka, ndi

wacoonadi; wakusungira anthu osawerengeka cifundo, wakukhulukira mphulupulu ndi kulakwa ndi kucimwa; koma wosamasula woparamula; wakulangira ana ndi zizukulu cifukwa ca mphulupulu ya atate ao, kufikira mbadwo wacitatu ndi wacinai” (Eksodo 34:6-7).

Ndipo anthu ananena motsutsana ndi Mulungu, ndi Mose, ndi kuti, Mwatikwezeranji kucitotsa ku Aigupto kuti tifere m’cipululu? Pakuti mkate ndi madzi palibe, ndi mtima wathu walema nao mkate wacabe uwu. Pamenepo Yehova anatumiza njoka zamoto pakati pa anthu, ndipo zinaluma anthu; nafapo anthu ambiri a Israyeli. (Numeri 21:5-6)

Ndimeyi ikutiiza kuti “AMBUYE adatumiza njoka za moto pakati pa anthu poyankha madandaulo awo. Kuchokera ku umboni wa m’malemba womwe tawona mpaka pano, kodi zochita za Mulungu zikadakhala zotani pamene “adatumiza” njokazo? Mogwirizana ndi mavesi ena mu Baibulo omwe taphunzira, Mulungu adakakamizidwa ndi kusamvera kwa anthu kuti awapatse ufulu wosawalowerera kuchokera kuchitetezo chake m’malo mwawo.

Kodi njoka zamoto zinakhalapo bwanji poyamba? “(Ambuye Mulungu wanu) amene anakutsogolerani m’cipululu cacikuru ndi coopsaco, munali njoka zamoto, ndi zinkhanira, mouma madzi; amene anakuturutsirani madzi m’thanthwe lansangalabwi” (Deuteronomo 8:15).

Njoka zamoto zinali pamenepo nthawi zonse ngati imodzi mwangozi zambiri zomwe Mulungu adateteza a Israyeli mozizwitsa kuukali wa m’chipululu. Nkhani iyi yonena kuti Mulungu anatumiza njoka zamoto zitha kukhala zovuta ngati Mulungu atatumiza zimbalangondo zanjala m’malo mwake.

Pali nkhani zambiri mu Baibulo zosonyeza kuti Mulungu anatumiza magulu ankhondo amene anaukira anthu kapena tsoka linalake. Ndikumvetsetsa uku, titha kunena kuti mu nkhani zonse za

m'malemba momwe Mulungu adatumiza kena kake koopsa, zikutanthauza kuti Mulungu sanathe luletsa izi kuti zisachitike popanda kuyambitsa zochitika ndi zotsatira. Sicholinga cha Mulungu, komanso sichikhalidwe chake, kuti adzilamulira zochitika za anthu.

Pamenepo Yehova anacitira dziko lace nsanje, nacitira anthu ace cifundo. Ndipo Yehova anayankhula, nati kwa anthu ace, Taonani, ndidzakutumizirani tirigu, ndi vinyo, ndi mafuta; ndipo mudzakhuta ndi izo; ndipo sindidzakuperekaninso mukhale citonzo mwa amitundu. (Yoweli 2:18-19)

Ndipo mthenga wakulankhula ndi ine anati kwa ine, Pfuula, ndi kuti, Atero Yehova wa makamu: Ndicitira nsanje Yerusamu ndi Ziyoni ndi (Zekariya 1:14)

Pakuti ndicita nsanje pa inu ndi nsanje ya Mulungu; pakuti ndinakupalitsani ubwenzi mwamuna mmodzi, kuti ndikalangize inu ngati namwali woyera mtima kwa Kristu. Koma ndiopa, kuti pena, monga njoka inanyenga Heva ndi kucenjerera kwace, maganizo anu angaipsidwe kusiyana nako kuona mtima ndi kuyera mtima ziri kwa Kristu. (2 Akorinto 11:2-3)

Nsanje ya Mulungu ndi yopanda dyera. Mulungu amachita nsanje chifukwa cha ena, osati chifukwa cha zake.

Ndipo Mkwiyo wa Yehova unayakanso pa Israyeli, nafulumiza Davide pa iwo, nati, Muka, nuwerenge Israyeli ndi Yuda. Ndipo mfumu inanena ndi Yoabu kazembe wakhamu, amene anali naye, Kayendere tsopano mafuko onse a Israyeli, kuyambira ku Dani kufikira ku Beereseba, nuwerenge anthuwo, kuti ndidziwe kucuruka kwao kwa anthu. Ndipo Yoabu ananena ndi mfumu, Yehova Mulungu wanu aonjezere kwa anthu monga ali kuwacurukitsa makumi khumi, ndi

maso a mbuye wanga mfumu acione; koma mbuye wanga mfumu alikukondwera bwanji ndi cinthu ici? Koma mau a mfumu anapambana Yoabu ndi atsogoleri a khamulo anaturuka pamaso pa mfumu kuti akawerenge anthu a Israyeli. (2 Samueli 24:1-4)

Pamene David adawerenga Israyeli anali akuwonetsa kunyada ndi kusakhulupirira Mulungu poyang'ana kuchuluka kwa anthu ndi magulu a nkondo kuti ateteze Israyeli. Izi zidachotsa chitetezo cha Mulungu mopanda chiwawa pa iwo, ndikuwasiya ali pachiwopsezo cha adani awo ndi ziwopsezo zina. Ngakhale wankhondo wolimba mtima Yoabu adaona zoopsa mu pempho la mfumu kuti awerenge Israyeli ndipo anafunsa mfumu.

Mulungu adasonkhezera Davide kumenyana nawo.” Kodi pangakhale vuto kumvetsetsa mawu awa momwe akuwerengedwera? Kodi Mulungu ali kunong'oneza khutu la Davide kuti awerenge Israyeli kuti akhale ndi chifukwa chomveka chowaukira iwo? Tiyeni tiwone vesiri molingana ndi zimene taphunzira pano pa zochitika za Mulungu.

Mulungu satenga mbali pakuwononga, ndipo samayambitsa zoyipa, koma pali wina amatero. Kodi nkutheka, mu chochitika ichi, kuti Mulungu “anafulumiza” Davide kuti awerenge Israyeli mwosamuletsa kutero? Ndipo zingakhale zopitirira muyeso kunena kuti sanali Mulungu akumanong'oneza Davide koma Satana? Kodi tingadziwe bwanji? Titha kuwerenga zomwezi mu buku la Mbiri woyamba: “Pamenepo Satana anaukira Israyeli nasonkhezera Davide awerenge Israyeli” (1 Mbiri 21:1).

Tikhoza kudabwa chifukwa chiyani Baibulo sirimangobwera poyera ndikunena mwatchutchu m'mene zinthu zidachitikira tikamawerenga m'masamba ake; kodi kuphunzira Baibulo sikukanakhala kosavuta? Inde zingatero. Komabe, vuto loyankhulana pakati pa Mulungu ndi anthu silinayambe lakhalapo chifukwa cha kutsamvetsetsa kwa Mulungu, koma chifukwa cha ife. Mulungu, mu nzeru zake, amatipatsa mwayi wosankha kuvomereza kapena kukana choonadi chokhudza Iye. Baibulo linalembedwa ndi

mfundo yofunika imeneyi m'malingaliro. Tikakhala ndi mwayi womvetsetsa kupulumutsa chowonadi chokhudza Mulungu ndikuchikana, kuunika kochuluka kumangotipikitsa patali kuchokera kwa Iye. Kusamvetsetsa kwa Baibulo kumapereka matanthauzidwe otsutsana pa chifukwa chimenechi. Sikuli khalidwe la Mulungu kutikopa, motsutsana ndi chifuniro chathu, kuti timukhulupirire ndi chikondi chake chasasunthika. Pa nthawi imodzimodziyo, Baibulo limapereka umboni wochuluka kwa iwo amene akufunafuna Mulungu wathu wofatsa kuti amupeze Iye.

Ndipo mudzandifuna Ine, ndi kundipeza, pamene mundifuna ndi mtima wanu wonse.

— Yeremiya 29:13

Momwe Mulungu Amamenyera Nkhondo

Mulungu amachita nkhondo yolimbana ndi choipa ndi chowonadi, chikondi, chifundo ndi kukhululuka.

Iye wocita cimo ali wocokera mwa mdierekezi, cifukwa mdierekezi amacimwa kuyambira paciyanbi. Kukacita ici Mwana wa Mulungu: adaonekera, ndiko kuti akaononge nchito za mdierekezi. (1 Yohane 3:8)

Ntchito ya mdierekezi kuyambira pamene anapanduka ndi yoneneza Mulungu komanso kuipitsa Mulungu. Yesu, Mwana wa Mulungu anabwera, anawonga ntchito za mdierekezi posonyeza kuti zonena zake zokhuza Mulungu zinali za bodza.

Simunazindikira malankhulidwe anga cifukwa ninji? Cifukwa simungathe kumva mau anga. Inu muli ocokera mwa atate wanu mdierekezi, ndipo zolalakaka zace za atate wanu mufuna kucita. Iyeyu anali wambanda kuyambira paciyanbi, ndipo sanaima m'coonadi, pakuti mwa iye mulibe coonadi. Pamene alankhula bodza, alankhula za mwini wace; pakuti ali waboddza, ndi atate wace wa bodza. (Yohane 8:43-44)

Yesu akutsimikizira kuti chida chachikulu cha mdierekezi ndikugwiritsa ntchito mabodza. “Ndizosatheka kuti Mulungu aname” (Ahebrei 6:18); amalimbana ndi mabodza a mdierekezi ndi chowonadi.

Tabvalani zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoze kucirimika macenjerero a mdierekezi. Cifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukulu, ndi maulamuliro, ndi akuchita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a coipa m'zakumwamba. Mwa ici mudzitengere zida zonse

za Mulungu, kuti mudzakhoza kuima citsutsire pofika tsiku loipa, ndipo, mutacita zonse, mudzacirimika. Cifukwa cace cirimikani, mutadzimangira m’cuuno mwanu ndi coonadi, mutabvalanso capacifuwa ca cilungamo; ndipo mutadzibveka mapazi anu ndi makonzedwe a Uthenga Wabwino wa mtendere; koposa zonse mutadzitengeranso cikopa ca cikhulupiro, cimene mudzakhoza kuzima naco mibvi yonse yoyaka moto ya woipayo. Mutengenso cisoti ca cipulumutso, ndi lupanga la Mzimu, ndilo Mau a Mulungu. (Aefeso 6:11-17)

Yesu anatiwonetsera ife kugwiritsa ntchito zida za Mulungu: Uthenga Wabwino wa chowonadi chonena za Mulungu (“mu chiuno mwanu mutadzimangirira ndi chowonadi”), kukwaniritsidwa kwake kwa kukhulupirika kwa chipangano (“chapachifuwa cha chilungamo”), uthenga wachiyanjanitso kwa Atate wathu Wakumwamba (“Uthenga Wabwino wantendere”), chitsimikizo chakukhulupirika kwa Mulungu (“chikopa cha chikhulupiro”), ndi lonjezo la moyo wosatha kwa iwo amene anamasulidwa ku ukapolo wa Satana ndi mabodza ake (“chisoti cha chipulumutso”). Timalimbikitsidwanso kutenga chida chomwechi chomwe Yesu adagwiritsa ntchito – Mwu a Mulungu (“lupanga la Uzimu”).

Musabwezere coipa, okonedwa, koma patukani pamkwiyo; pakuti kwalembedwa, Kubwezera kuli kwanga, Ine ndidzabwezera, ati Ambuye. Koma ngati mdani wako akumva njala, umdyetse, ngati akumva ludzu ummwetse; pakuti pakutero udzaunjika Makala a moto pamutu pace. Musagonje kwa coipa, koma ndi cabwino gonjetsani coipa. (Aroma 12:19-21)

Kodi kubwezera kwa Mulungu ndi chiyani? Amagonjetsa choipa mwa kuchita chabwino, ndipo amauza ana ake nawonso atero. Kuchitira adani athu mokoma mtima osati kubwezera kuli ngati kuwunjika “makala a moto” pamutu yawo. Kubwezera mdani ndiko kugonjetsedwa ndi choipa. Komabe, pali njira yogonjetsera

choyipa – “ndi chabwino.” Ndiyo njira ya Mulungu yomenyera nkondo.

Ndipo Yesu ananena, Atate, muwakhulukire iwo, pakuti sadziwa cimene acita. Ndipo anagawana zobvala zace, poyesa maere. (Luka 23:34)

Mawu a Yesu awa ndi otipindulitsa ife. Atate salira kukakamizidwa kuti atikhulukire. Vuto silili kwa Mulungu, koma ndi ife. Timaganiza ngati Mulungu ali ngati ife. Pomwe Yesu adalankhula mawuwa “Atate, akhulukireni; pakuti sadziwa chimene achita,” samangonena za iwo okha amene adapachika pa mtanda, amalankhulanso m’ malo mwathu, Mulungu akufuna kuti tidziwe kuti amamvetsetsa mavuto athu (sitidziwa zomwe tikuchita); amatikondabe mopanda malire ndipo akugwira ntchito mwakhama kuti atipulumutse.

Koma cipatso ca Mzimu ndico cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, cikhulupiriro, cifatso, ciletso; pokana zimenezi palibe lamulo.

— Agalatiya 5:22-23

Sodomu Ndi Gomora

Kuwonongedwa kwa Sodomu ndi Gomora kumaganiziridwa ngati chitsanzo chapadera cha Mulungu wokwiya kugwetsa imfa ndi chiwonongeko pa anthu oipa. Ngati titenga nkhanayi mu Baibulo monga momwe ikuwerengedwera, zomwe zikuwoneka kuti zikuchitika ndi izi: Mizinda iwiri ili m'dera lamalonda a ulimi labwino, ndipo moyo umakhala wosavuta kwa nzikazo. Anthu amakhala nthawi yambiri yosangalala ndipo zochitika zopanda umulungu zimakhala zofala. Mulungu amayang'ana pansi kuchokera kumwamba ndipo adakwiya ndi kuchuluka kwa kuipa kwawo. Amapewa kuchitapo kanthu kwakanthawi, koma m'khalidwe woyipa anaculuka kwambiri mwakuti kuleza mtima kwa Mulungu kumatha. Akutumiza chenjezo kwa Loti wolungamayo ndi banja lake kutuluka mu Sodomu. Kenako, posonyeza mkwiyo modabwitsa, Mulungu akugwetsa moto wa sulufure kuchokera kumwamba. Amuna, akazi, ndi ana adakumana ndi imfa yoopsa. Sodomu ndi Gomora anawonongedwa, ndipo kubwezera kwa Mulungu kwakwaniritsidwa.

Tsopano, tiwone chochitika chomwechi ndikumvetsetsa kuti Mulungu satenga nawo mbali pakuwononga. Yerekezani kuti mu mizinda iwiriya muli anthu odzikonda akusangalala ndi chitukuko komanso zisangalalo: “Taona, mphulupulu ya mng'onowako Sodomu ndi iye, kudzikiza, kucuruka kwa cakudya, ndi kupumula kwa mtambasali, anali nako iye ndi ana ace; ndipo sanalimbitsa dzanja la wosauka ndi wosowa” (Ezekieli 16:49). Anthu sakudziwa kuti pansi pa mizinda yawo (yomwe imamangidwa pa malo osakhazikika mwa chilengedwe) mphamvu ya kuphulika kwa phala la moto kukupanga. Sadziwanso kuti Mulungu wosawonekayo, amene akumukana, ndi Mulungu yomweyo amene, mpaka mu nthawiyo, adawateteza ku masoka. Tsiku lidafika loti avomereze kuti akufuna kukhala osadalira Iye. Kuti asunge ufulu wawo,

anawalola monyinyirika, kuwasiya opanda chitetezo ku mphamvu za chilengedwe zomwe sangathenso kuziramulira. Ziphuphu za pansi zinang'ambika ndikutulutsa thanthwe losungunuka la moto kupita m'mlengalenga mapazi zikwizikwi ndikugwetsa “sulufure ndi moto wochokera kwa AMBUYE kumwamba” (Genesis 19:24), kuwononga Sodomu ndi Gomorrah mu mphindi zochepa.

Zomwe Mulungu adachita powononga mizindayi kudapatsa nzika ufulu weniweni – kuphatikizapo ufulu wosankha zomwe zingabweretse mavuto: “Ndcititsa mboni lero kumwamba ndi dziko lapansi zitsutse inu; ndaika pamaso panu moyo ndi imfa, mdalitso ndi temberero; potero, sankhanimoyo, kuti mukhale ndi moyo, inu ndi mbeu zanu; kukonda Yehova Mulungu wanu, kumvera mau ace, ndi kummamatira Iye, pakuti Iye ndiye moyo wanu, ndi masiku anu ocuruka” (Deuteronomo 30:19-20).

Matenda, ngozi, imfa, nkondo, masoka a chilengedwe, ndi zina zotero zimachitika pa zifukwa zambiri. Nthawi zambiri timakhala ndi mlandu, nthawi zina Satana ndiye amakhala, ndipo nthawi zina mphamvu za chilengedwe zomwe zimachitika pambuyo pa chigumula ndizomwe zimayambitsa. Nthawi zambiri zinthu zina zophatikizira zimakhudzidwa. Chifukwa sitingathe kuwona bwino lomwe chifukwa chake mavuto ena adachitika, timakonda kuimba Mulungu mlandu. Kodi ndi zabwino? Kodi ndi zomveka? Chizolowezi chathu chodzudzula anthu zakhala zikuchitika kwanthawi yayitali. Kodi kupewa udindo kumeneku kunayamba liti ndipo kunayambira kuti? “Ndipo anati mwamunayo, Mkazi amene munandipatsa ine kuti akhale ndi ine, ameneyo anandipatsa ine za mtengo, ndipo ndinadya. Ndipo Yehova Mulungu anati kwa mkaziyo, Ciani cimene wacitaci? Ndipo anati mkaziyo, Njoka inandiyenga ine, ndipo ndinadya” (Genesis 3:12-13).

Yehova, m'mwamba muli cifundo canu; Coonadi canu
cifikira kuthambo. Cilungamo canu cikunga mapiri a
Mulungu; Maweruzo anu akunga cozama cacikuru;
Yehova, musunga munthu ndi nyama. Ha! Cifundo canu,
Mulungu, ncokonedwadi! Ndipo ana a anthu athawira
ku mthunzi wa mapiko anu.

— Masalmo 36:5-7

Nanga Bwanji Chigumula?

Nanga bwanji chigumula cha m' masiku a Noah? Ngati Mulungu sali wowononga, nchiyani chinachitika kuti atibweretsere tsoka lalikulu? Ndi umboni wanji womwe tingaupeze mu Baibulo ndi kwina kulikonse kuti utifotokozere momveka bwino chomwe chinayambitsa chigumula chachikulu padziko lonsechi?

Ndipo anati Yehova, Mzimu wanga sudzakangana ndi anthu nthawi zonse, cifukwa iwonso ndi thupi lanyama: koma masiku ace adzakhala zaka zana limodzi kudza makumi awiri. (Genesis 6:3)

Mulungu mwachiwonekere anali akuyembekezera mtsogolo ku nthawi pamene mtundu wa anthu ukanadzitalikitsa patali ndi Iye mwakuti Iye akakamizidwa kuwalola iwo apite mwa kumasula muchirikizo wake wa mphamvu za chilengedwe. Titha kudabwa chomwe chidamupangitsa kuti kenako asiye. Kodi Mulungu adachita chosankha kuti atero, kapena panali chinthu chinanso chokhudzidwa?

Ingoganizirani kuti muli ndi mnansi yemwe ali ndi mavuto angapo. Amavutika pa nkhani zachuma, ali ndi zovuta zingapo zathanzi, sakhazikika kuyenda mtunda wopitirira pang'ono kuchokera ku nyumba. Kuphatikiza apo, alibe galimoto, zomwe zimapangitsa avutuke kuyenda ndi kutha kupeza zosowa zake.

Tsiku lina, pokambirana naye, munamva zakusowa kwake mayendedwe ndi kumperekeza pagalimoto ku msika ndi malo ena. Kwa miyezi ingapo yotsatira, mumamupatsa mayendedwe mgalimoto yanu kukaonana ndi adokotala, malo ogula mankhwala, komanso kumsika waukulu. Makonzedwe awa akuoneka kuti akuyenda bwino, ndipo ndinu okondwa kumuthandiza.

Ndiye tsiku lina lofunda la chilimwe mnansi wanu yemweyo akubwera pakhomo panu pazomwe zikuwoneka ngati zosokonezeka ndikukufunsani kupita naye ku banki kudutsa tawuni. Mukuwona atanyamula chikwama chapepala, chigoba cha kutetezera, ndi zomwe zikuwona ngati mfuti itakulungidwa mu saka. Inu mungatani? Kodi mungatenge makiyi a galimoto lanu kuthamangira kumuyendetsa kumuperekeza kumene akupita ndi kubwerako?

Tonsefe tiri ndi mizere yomwe sitikufuna kuwoloka. Mizere iyi ikukhuzana ndi nkhani za makhalidwe, zoyenera, komanso malire a umwini. Kodi sizomveka kukhulupirira kuti Mulungu alinso ndi mizere yomwe sadzawoloka – kapena sangatero?

Ndipo anaona Yehova kuti kuipa kwa anthu kunali kwakukuru pa dziko lapansi, ndiponso kuti ndingaliro zonse za maganizo a mitima yao zinali zoipabe zokhazokha. Ndipo dziko lapansi linabvunda pamaso pa Mulungu, dziko lapansi ndipo linadzala ndi ciwawa. Ndipo Mulungu anaona dziko lapansi, ndipo taonani, linabvunda; pakuti anthu onse anabvunditsa njira yao pa dziko lapansi. Ndipo Mulungu anati kwa Nowa, Cimariziro cace ca anthu onse cafika pamaso panga; pakuti dziko lapansi ladzala ndi ciwawa cifukwa ca iwo; taonani, ndidzaononga iwo pamodzi ndi dziko lapansi. (Genesis 6:5, 11-13)

Kodi dziko lathu linali lotani chisanafike chigumula? Mulungu anaululira Nowa, “dziko lapansi linadzala ndi chiwawa chifukwa cha iwo” (vesi 13). Chifukwa cha chiwawa cha anthu, dziko lapansino linali kusunga chiwawa. Mphamvu zodabwitsa za chiwawa zinatsala pang’ono kumasulidwa mu chiwonongeko chomwe chinali kubwera. Gulu la anthu linali litawonongeka: “Ndipo Mulungu anaona dziko lapansi, ndipo taonani, linabvunda; pakuti anthu onse anabvunditsa njira yao pa dziko lapansi.”

Ndi otsatira angati okhulupirika omwe Mulungu anali nawo munthawi yovutayi mu mbiri? Nowa yekha ndi amene amatchulidwa

mu Baibulo. Kodi n’chiyani chinachititsa kuti zinthu ziyende chonchi? Malingaliro a anthu anali “oyipabe.” Kodi Baibulo limafotozanji za zoipa? Pamene Adamu ndi Hava adadya chipatso cha “mtengo wodziwitsa chabwino ndi choipa” (Genesis 2:17; 3:6), kusinthika kwawo malingaliro popena za ubwino wa Mulungu kumatanthauzira bwino lomwe kuti zoipa ndi chiyani. Chithunzi cholakwika cha makolo athu oyamba cha Mulungu wathu wofatsa ndi chomwe dziko lidalandira. Anthu okonda zachiwawa mdziko chigumula chisanachitike amaganiza kuti Mulungu amalekerera zachiwawa zawo. Mulungu adayankha kuti chiyani? “Zinamumvetsa chisoni mu mtima wake” (Genesis 6:6).

Anthu anali atakakhira Mulungu mpaka pamzere womwe sakanatha kuwoloka kuchita nawo zachiwawa Iye mwini. Mulungu anakakamizidwa kumasula kugwira kwake mphamvu zake mu chilengewde. Ntawi ya zaka zana limodzi makumi awiri itatha, ndipo okwerawo ali bwinobwino mu chingalawa, mvula idayamba kugwa, kugwa kwa masiku makumi anayi masana ndi usiku. Kodi nchiyani chinayambitsa chigumula chachikulu chimenechi? Tikupeza zidziwitso zofunikira mu mutu woyamba wa Genesis:

Ndipo anati Mulungu, Pakhale thambo pakati pa madzi, lilekanitse madzi ndi madzi, Ndipo Mulungu anapanga thambo, nalekanitsa madzi anali pansi pa thambolo ndi madzi anali pamwamba pa thambolo; ndipo kunatero. Ndipo Mulungu analicha thambolo Kumwamba. (Genesis 1:6-8)

Thambo ndi chiyani? Thambo limatanthauza chipinda kapena mzikiti. Mzikiti chimatanthauza chophimba pansi chomwe chidayimitsidwa kapena kukhazikika kumwamba kapena m’mlengalenga. Ndimeyi ikupitiriza kufotokoza mzikiti uwu ukulekanitsa madzi, ndi madzi ochulukirapo pamwamba pake.

Chophimba chachikulu cha nthunzi yamadzi yam’mlengalenga chidazungulira dziko lonse lapansi ngati chimbudzi chachikulu chomwe chimapatsa dziko lathu nyengo yozizira komanso kutentha

kuchokera malo ozizira aku mpoto kwenikweni mpaka ku malo ozizira aku mwera kwenikweni. Zotsalira zakale za zomera ndi zinyama za nyengo yotentha zopezeka malo ozizira zomwe zimapereka umboni woti nyengo yotereyi idalipo pa dziko lapansi pano. Baibulo limaperekanso chidziwitso china chofunikira chokhudza nyengo yapadziko lapansi m’masiku akale aja:

Imeneyo ndiyo mibadwo yao ya zakumwamba ndi dziko lapansi, pamene zinalengedwa, tsiku lomwe Yehova Mulungu anapanga dziko lapansi ndi zakumwamba. Ndipo zomera zonse za m’ munda zisanakhale m’ dziko lapansi, ndiponso matherere onse a m’ munda asanamere; cifukwa Yehova Mulungu sanabvumbitsire mvula pa dziko lapansi, ndipo panalibe munthu wakulima nthaka; koma inabwera nkhungu yoturuka pa dziko lapansi, niithiriraponse pamwamba pa nthaka. (Genesis 2:4-6)

Mavesiwa akusonyeza dziko losiyana kwambiri ndi dziko lomwe tikudziwa lero. “AMBUYE Mulungu anali asanabvumbitsire mvula pa dziko lapansi Koma kunakwera nkhungu kuchokera pa dziko lapansi, ndi kuthirira nkhope yonse ya dziko lapansi.” Dziko lapansi linali lonyowa koma mofunda ndi nyengo yabwino kwambiri, osasinthasinthwa mwadzidzidzi kutentha ndi kuzizira. Ndi nyengo yosasinthasinthwa mwadzidzidzi sikungakhale mvula yamabingu, mphepo zamkuntho, mkuntho, matalala, chisanu, ndi mwachiwonekere kunalibe mvula. Ndikothekanso kuti padziko lapansi paliponse panali pa thyathyathya kuposa momwe ziriri masiku ano, popanda mapiri ataliatali kapena zigwembe zakuya zam’nyanja. Kuphatikiza apo, malo ocheperapo a dziko lapansi akanakhala okutidwa ndi madzi.

Kodi nchiyani chomwe chinaimitsa madzi onse m’ malere, ndipo ndi chiyani chimene chiyambitsa chigumula? Tikudziwa kuchokera pakuwona kosavuta kuti kutentha kumapangitsa madzi kukwera. Madzi otentha mu ketulo pa chitofu amatuluka kunja ngati nthunzi. Madzi ambiri pa dziko lapansi amapeka nthunzi ya madzi ambiri pa

tsiku lirironse. Kutentha kwambiri komwe kumaperekedwa, kumathawitsanso nthunzi yambiri ya madziwo. Pafupifupi madzi ochepa amapereka nthunzi kuchokera kunyanja zozizira kwambiri pakatikati pa nyengo yozizira kuyerekeza ndi nyengo yotentha ya chilimwe.

Bwanji ngati kukanakhala mphamvu yowonjezera yotentha chisanachitike chigumula: Kodi sizikanathandizira madzi ambiri m'mlengalenga? Dziko lapansi limapeza mphamvu yotentha kuchokera ku dzuwa lanthu. Popanda dzuwali dziko lathu lapansi likadakhala lozizira kwambiri kutentha kwake koyandikira zero.

Mulungu atalenga dziko lapansi, molodola adayika donosolo la mphamvu yakulentha yomwe yimatha kuyimitsa madzi ambiri m'mlengalenga. Dzuwa likadakhala njira yogwiritsidwa ntchito mu dongosololi. Ndizomvekanso kukhulupirira kuti dzuwa chigumula chisanachitike limatulutsa kutentha kochuluka koposa momwe zikukhalira lero. Ngati izi ndizoona, ndiye kuti ndizomveka kukhulupirira kuti pamene Mulungu adakakamizidwa kumasula kugwirizitsa mphamvu zake pa chilengedwe zinakhunzanso kutentha kwa dzuwa.

Thambo losamalika m'mlengalenga lidasokonekera, ndipo “Caka ca mazana asanu ndi limodzi ca moyo wa Nowa, mwezi waciwiri, tsiku la khumi ndi asanu ndi awiri la mwezi, tsiku lomwelo akasupe onse a madzi akuru anasefuka, ndi mazenera a kumwamba anatseguka. Ndipo mvula inali pa dziko lapansi masiku makumi anai masana ndi usiku” (Genesis 7:11-12). Mvula yoyambirira ya mbiri yakale idayamba kugwa, pamapeto pake madzi ambiri ochuluka adagwa pa dziko lonse lapansi.

Kusakhazikika kwa nthaka kudagwirizana ndi kusakhazikika kwa mlengalenga komwe kunayambitsa kupanikizika kwa madzi a akasupe obisika pansu: “Tsiku lomwero akasupe onse amadzi akuya adapwanyidwa” (Genesis 7:11). “Akasupe” awa mathandizira madzi ambiri osefukira.

Anthu asanu ndi atatu okha omwe anali m'chingalawa anapulumuka chigumula: Nowa ndi banja lake. Mitundu yambiri yazinyama idalinso m'ngalawa yayikuluyi ndi cholinga choculukitsa dziko lansi ndi mtundu uliwonse wa nyama pambuyo pa chigumula.

Zotsalira zakale za chingalawacho zimasungidwa ku malo a dziko losungira za chilengedwe yoperekedwa ku malo omwe ngalawayo inayima ku Mawa kwa dziko la Turkey, pafupi ndi mzinda wawung'ono wa Dogubayit. Kupeza kwapadera kwa akatswiri ofukula zinthu zakale, m'mapiri a Ararati, ndi umboni wotsimikiza kuti nkhani ya mu Baibulo yonena za chigumula chachikulu sithano chabe, koma ndi mbiri yodalirika yatsoka lokhalo la chilengedwe cha dziko lonse lapansi:

*Ndipo madzi anaphweraphwerabe pa dziko lapansi:
pamene anatha masiku zana limodzi kudza makumi atatu
madzi anacepa. Ndipo cingalawacinaima pa mapiri a
Ararati, mwezi wacisanu ndi ciwiri, tsiku lakhumi ndi
asanu ndi awiri la mwezi.*

— Genesis 8:3-4

Umboni wa Mtanda

Pakumvetsetsa kolondola kwa machitidwe a Mulungu mu Chipangano Chakale, tikutsimikizika kuti Iye sawononga – mosasamala momwe zinthu ziriri. Komabe, umboni wotsimikizika kwambiri kuti Mulungu sayandikira wochimwa kuti amuwononge umapezeka mu Chipangano Chatsopano.

Chikhulupiriro chakuti Yesu adatifera pamtanda chiri pafupifupi ponseponse pakati pa ophunzira Baibulo, ngakhale pali malingaliro osiyanasiyana pamomwe imfa ya Yesu yimatipulumutsira. Komabe ambiri amakhulupirira kuti pamene Yesu anafa pamtanda, Iye adakumana ndi zomwe tiyenera kukumana nazo popanda kuzipereka Yekha m'malo mwathu.

Ngati izi ndi zoonza, ndiye kuti tingayembekezere kuti Yesu anafa momwemonso momwe ife timafera mogwirizana ndi zomwe Mulungu “amachita” kuti abweretse imfa. Ngati timakhulupirira kuti Mulungu ndi amene amawononga ochimwa; ndiye tiyembekezeranso kuti Mulungu Atate adayandikira Yesu kuti amuphe. Kodi izi ndi zomwe timapeza? Uthenga wabwino wa Mateyu umafotokoza mwatsatanetsatane za kupachikidwa kwa Khristu. Kodi mawu ati omaliza a Yesu atatsala pang'ono kumwalira? “Mulungu wanga, Mulungu wanga, mwanisiyiranji Ine?” (Mateyu 27:46)

Vesiri likuwulula momwe Yesu anafera. Mulungu Atate analola kuti Mwana Wake akumane ndi zomwe munthu aliyense amene akana chikondi chake adzakumane nazo pamapeto pake – kuzipatula kwa Iye, Wopatsa - Moyo. Mulungu Atate sanaphe Yesu – tchimo lathu lidatero: “Mphotho yake ya ucimo ndi imfa” (Aroma 6:23). Tchimo limatha kupha palokha popanda kuthandizidwa ndi Mulungu. Moyo wonse ndi wochokera kwa Mulungu popanda kuchotserapo. Imfa zonse ndi zotsalira za uchimo popanda

kuchotserapo. Kulingalira kuti Mulungu ndiye gwero la imfa ndizosamveka – popanda kuchotserapo.

Sizingatheke mu buku laling’ono ngati iri kuwunika khani zonse za chiwonongeko ndi mavuto omwe amakanhizira kwa Mulungu. Komabe, mavesi taphunzirawa ndi mfungulo wothandiza kumvetsetsa bwino za udindo wa Mulungu pa imfa ndi masoka omwe ali mu Baibulo. Baibulo limamasulira Baibulo. Lemba likabweza nsalu yotchinga m’mdime ina yake kuti tiwone zomwe Mulungu akuchita, titha kugwiritsa ntchito ilo ngati mfungulo kuti timvetsetse ndime zina zomwe sizikumveka bwino (monga momwe mavesi awiri a mu Baibulo akuwoneka kuti akutsutsana). Kuphatikiza apo, mawu a Mulungu wonena za Iye yekha ndi wofunika kuwalingalira mwapadera, mwachitsanzo: “Ine ndine AMBUYE sindisintha” (Malaki 3:6). Pomaliza, chowonadi chonena za Mulungu, chomwe Yesu anaphunzitsa ndi kuwonetsa, ndi njira yolondola yowerengera Baibulo lonse kuyambira Genesis mpaka Cibvumbulutso.

Kuti Khristu akhale cikhalire mwa cikhulupiriro m’mtima yanu; kuti, ozika mizu ndi otesndereka m’cikondi, mukakhozetu kuzindikira pamodzi ndi oyera mtima onse, kupingasa, ndi utali, ndi kukwera, ndi kuzama nciani; ndi kuzindikira cikondi ca Khristu, cakuposa mazindikiridwe, kuti mukadzazidwe kufikira cidzalo conse ca Mulungu.

— Aefeso 3:17-19

Mulungu Sali Wankhanza

Pali uthenga wabwino kwa aliyense amene anaphunzitsidwa za chiphunzitso cha moto wa gehena woyaka muyaya. Chikhulupirochi sichichirikizidwa ndi kuphunzira kwathunthu kwa Baibulo. Malemba amafotokoza kuti imfa ili ngati kukhala wosadziwa kanthu. Ndi ku gona kwakanthawi komwe kumangokhala mpaka kuwuka. Pambuyo pa nthawi yimeneyo, onse amene adakana kuyanjanitsidwa ndi Mulungu adzakolola, monga zotsatira zake za chirengedwe, kusakhalako kwa muyaya.

Kuti tipeze thandizo la malo ozunzira a moto mu Baibulo titha kuchita izi kutsimikizira mawu omwe ali enieni kapena ophiphiritsa. Mawu oti moto atha kukhala nditanthauzo lenileni kapena lophiphiritsa. Mu buku la Daniel, pamene Nebukadinezara adaponya Sadrake, Meshaki, ndi Abednego mu ng'anjo yoyaka moto, mwachiwonekere unali moto weniweni womwe adakumana nawo. Pamene Yohane M'batizi, yemwe adabatiza ndi madzi, adati Khristu adzabatiza ndi Mzimu Woyera ndi moto, mwachiwonekere sanali kutanthauza moto weniweni, koma anali kugwiritsa ntchito liwu loti moto mophiphiritsa.

“Mulungu wathu ndi moto wonyeketsa,” ndipo “Mulungu ndiye chikondi” (Ahebri 12:29; 1 Yohane 4:16). Kodi mawu awiriwa onena za Mulungu akutsutsana? Kokha ngati tiganiza za moto ngati moto weniweni. Moto ndi mankhwala onyeketsa. Kodi Mulungu ndi mankhwala onyeketsa? Izi ndi zogwirizana ngati timvetsetsa momwe chikondi cha Mulungu chimakhuzira munthu. Chikondi cha Mulungu chimanyeketsa kudzikonda. Kudzikonda ndikotsutsana ndi chikondi chenicheni. Ngati tiri otseguka ku chikondi cha Mulungu, chikondi chomwecho chimabwera mwa ife ndi kunyeketsa dyera lakupha mu mtima yathu. Ichi ndi chochitika chopatsa moyo.

Ngati tikana chikondi cha Mulungu, timamatira kudzikonda kwathu, chikondi chomwecho chimakhala chizunzo chathu.

Tiyetsetsa kuti tisunthire kutali ndi izi ngakhale kuthawa kapena kubisala kwa Mulungu. Izi ndi zomwe zidachitikira Adamu ndi Hava atakhulupirira bodza la njoka lonena za Mulungu. Kumvetsetsa motere, titha kuwona kuti chikondi cha Mulungu ndi moto wonyeketsa.

Fanizo la Yesu la munthu wachuma ndi Lazaro nthawi zina limagwiritsidwa ntchito kuchirikiza chiphunzitso cha malo enieni a chizunzo:

Ndipo panali munthu mwini cuma amabvala cibakuwa ndi nsaru yabafuta, nasekera, nadyerera masiku onse; ndipo wopemphepempha wina, dzina lace Lazaro, adaikidwa pakhomo pace wodzala ndi zironda, ndipo anafuna kukhuta ndi zakugwa pa gome la mwini cumayo; komatu agarunso anadza nanyambita zironda zace. Ndipo kunali kuti wopemphayo adafa, ndi kuti anatengedwa iye ndi angelo kunka ku cifuwa ca Abrahamu; ndipo mwini cumayo adafanso, naikidwa m'manda. Ndipo m'Hade anakweza maso ace, pokhala nao mazunzo, naona Abrahamu patali, ndi Lazaro m'cifuwa mwace. Ndipo anakweza mau nati, Atate Abrahamu, mundicitire cifundo, mutume Lazaro, kuti abviike nsonga ya cala cace m'madzi, naziziritse lilime langa; pakuti ndizunzidwadi m'lawi ili la moto. Koma Abrahamu anati, Mwana, kumbukila kuti unalandira zokoma zako pakukhala m'moyo iwe, momwemonso Lazaro zoipa; ndipo tsopano iye asangalatsidwa pano, koma iwe uzunzidwadi. Ndipo pamwamba pa izi, pakati pa ife ndi inu pakhazikika phompho lalikuru, kotero kuti iwo akufuna kuoloka kucokera kuno kunka kwa inu sangathe, kapena kucokera kwanuko kuyambuka kudza kwa ife, sangathenso. Koma anati, Pamenepo ndikupemphani, Atate, kuti mumtume ku nyumba ya atate wanga; pakuti ndiri nao abale asanu awacitire umboni iwo kuti iwonso angadze ku malo ano a mazunzo. Koma Abrahamu anati, Ali ndi Mose ndi

aneneri; amvere iwo. Koma anati, Iai, Atate Abrahamu, komatu ngati wina akapita kwa iwo wocokera kwa akufa adzasandulika mtima. Koma anati kwa iye, Ngati samvera Mose ndi aneneri, sadzakopeka mtima ngakhale wina akauka kwa akufa. (Luka 16:19-31)

Yesu ananena fanizoli kufotokoza za zotsatira za dyera ndi chisokonezo chimakhala pa munthu. Yesu amalankhula ndi Afarisi omwe amadziyesa olungama, ndipo anafotokoza fanizoli pazolakwika zomwe anthu ambiri amakhulupirira za moyo ukatha moyo pa dziko.

Ayuda adagwirizanitsa chuma ndi madalitso a Mulungu. M'malingaliro awo munthu wosauka, makamaka amene anali ndi vuto linalake, adatembereredwa ndi Mulungu; lingaliro loti munthu amayenera kulandira gawo lake m'moyo chifukwa cha kusowa kwa uzimu kapena tchimo. Wolemera, komabe, adatsimikiziridwa kuti Mulungu amamukonda mwapadera. Malingana ndi kaganiziridwe ka Afarisi, kulemera kwa munthu kapena udindo wake, unali muyeso woti ndi wolungama pamaso pa Mulungu. Yesu adawapatsa fanizoli kuti awulule chinyengo cha lingaliro lopapatiza komanso lankhanza.

Choyamba tiwona nkhani zingapo. Pambuyo pa imfa yake, Lazaro, wopemphapemphayo, akukhala bwinobwino “pachifuwa cha Abrahamu.” Munthu wa chuma nayenso anafa ndikupita ku gehena akuzunzika; atayang'ana kumwamba, anaona Abrahamu ndi Lazaro chapatali. Kukambirana kunatsatira pakati pa munthu wachuma uja ndi “Tate Abrahamu.”

Tsopano tiyeni tiwone bwino nkhaniyi pofunsa mafunso ena moganizira bwino:

- Kodi Abrahamu ndi Lazaro are kuti m'nkhaniyi?
- Ngati Abrahamu ndi Lazaro ali kumwamba kapena ku paradizo, zikutheka bwanji kuti Abrahamu amatha kukambirana ndi munthu wachuma uja ali ku gehena, ndipo zimatheka bwanji kuti munthu wachuma uja amuone?
- Ngati Abrahamu ndi Lazaro ali ku gehena, akutani kumeneko?

- Ngati Abrahamu ndi Lazaro kulibe kumwamba kapena ku gehena, ali kuti?
- Kodi madontho pang'ono amadzi palirime angatsitsimule bwanji munthu kuzunzika ku moto wa gehena?
- Kodi Lazaro akumuona munthu wachuma uja akuzunzika ku gehena ndikumva kuchonderera kwake?
- Kodi Lazaro akutonthozedwa bwanji pachifuwa cha Abrahamu?
- Kodi Lazaro akutonthozedwa ngakhale akudziwa kuti munthu wachuma uja akuvutika kapena chifukwa cha zowawa zake?
- Kodi akulimbikitsidwa Lazaro kuti alimbikitse kuchitira nkhanza munthu wachuma uja chifukwa zinthu tsopano zasintha?
- Kodi phompo ili liyenera kukhala lokulirapo bwanji poletsa kulumikizana pakati pa gehena ndi komwe kunali Abrahamu ndi Lazaro?
- Kodi phompho lalikululi liyenera kukhala lalikululu bwanji kuti lirepheretse kuzindikira kwa omwe kuzunzika ku moto wa gehena ndi iwo omwe ali mbali yabwino ya phompho? Mamita mazana atatu? Makiromita mazana atatu? Kodi chilengedwe chikanakhala chotalikira mokwanira?
- Kodi nkwanzeru kunena kuti chifukwa chakuti Yesu anagwiritsa ntchito liwu lonena za gehena m'fanizo la munthu wachuma ndi Lazaro kuti anali kuchirikiza chiphunzitso cha gehena woyaka moto kwa muyaya.

Kodi sizowoneka zomveka kuti Yesu anabweretsa lingaliro loti malo ozunzirako akuwotchedwa mu fanizoli akuchotsa chiphunzitso choipachi m'malo mochilimbikitsa? Yesu amaphunzitsa kuti sizingatheke kwa iwo adzakhale kwamuyaya kukhala ndi mtendere wangwiro ndi chimwemwe chenicheni ngati kuli gehena weniweni kuli konse mu chilengedwe.

Chiphunzitso chakuti kuli malo ozunzikirako kwamuyaya ndi bodza la Satana lomwe limajambula Mulungu wathu wofatsa, wachifundo, wokhululuka, ndi wachikondi ngati wankhanza

woyipitsitsa mungaganizire ndi kukonza nzeru yotichotsera kwa Atate wathu Wakumwamba. Sipadzakhala konse malo a chizunzo chamuyaya. Baibulo limalankhula m'malo mwake za tsiku likudza pamene mavuto onse adzatha – kwamuyaya:

Ndipo ndinamva mau akuru ochokera ku mpando wacifumu, ndi kunena Taonani, cihema ca Mulungu ciri ndi mwa anthu; ndipo adzakhalisa nao, ndi iwo adzakhala anthu ace, ndi Mulungu yekha adzakhala nao, Mulungu wao; Ndipo adzawapukutira misozi yonse kuicotsa pamaso pao; ndipo sipadzakhalanso imfa; ndipo sipadzakhalanso maliro, kapena kulira, kapena cowawitsa; zoyambazo zapita. (Cibvumbulutso 21:3-4)

Ambiri amakonda kudabwa kuti tidzakhala kwamuyaya motani. Kodi tidzakhala ndi matupi a umunthu monga momwe tilili pano, kapena tidzakhala moyo wopanda matupi? Ndipo. Kodi moyo nchiyani?

Ndipo Yehova Mulungu anaumba munthu ndi dothi lapansi, nauzira mpweya wa moyo m'mphuno mwace; munthuyo nakhala wamoyo. (Genesis 2:7)

Taonani, miyoyo yonse ndi yanga, monga moyo wa atate womwemonso wa mwana, ndiyo yanga; moyo wocimwawo ndiwo udazafa. (Ezekieli 18:4)

Miyoyo yathu imafuna “mpweya wamoyo,” kapena mzimu, wochokera kwa Mulungu. Sitikhala ndi moyo patokha. Aliyense wa ife ndife a moyo. Chikhulupiriro chakuti tiri ndi moyo wapadera wosafa sichichirikizidwa mu Baibulo. Pakubweranso kwachiwiri kwa Khristu matupi athu osakhala angwiro adzasinthidwa “m'kuphethira kwa diso” (1 Akorinto 15:52) kukhala angwiro.

Pakuti mphotho yace ya ucimo ndi imfa. (Aroma 6:23)

Palibe paliponse mu Mawu a Mulungu pomwe imfa imafotokozedwa ngati china chirichonse kupatula imfa. Malemba onse akamveka bwino, amatsimikizira kuti uchimo umabweretsa imfa ndi mawu amodzi okha otsutsana: “Ndipo njoka inati kwa mkaziyo, Kufa simudzafadi” (Genesis 3:4).

Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira Iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha. (Yohane 3:16)

Mawu oti kutayika amatanthauza kudzafika posakhalako. Sizikutanthauza kuti kudzakhalako kumalo kwina kwake kuli mavuto.

Izi anati, ndipo zitatha izi ananena nao, Lazaro bwenzi lathu ali m’tulo; koma ndimuka kukamuukitsa iye tulo tace. Cifukwa cake akuphunzira ace anati kwa Iye, Ambuye, ngati ali m’tulo adzacira. Koma Yesu adanena za imfa yace; koma iwowa anayesa kuti ananena za mpumulo wa tulo. Pamenepo Yesu anati kwa iwo momveka, Lazaro wamwalira. (Yohane 11:11-14)

Yesu anayerekezera imfa ndi tulo chifukwa Mulungu ndi wokhoza kuukitsa munthu amene anamwalira. Yesu akuukitsa Lazaro patapita masiku anayi ali mu manda, Lazaro sanaitanidwe kuchokera kumwamba. Adadzuka ali mosadziwa kanthu – imfa.

Wodala munthu amene akhala naye Mulungu wa Yakobo kuti amthandize, Ciyembekezo cace ciri pa Yehova, Mulungu wace. (Masalmo 146:5)

Pakufa malingaliro ake samapitirira kwina.

Pakuti muimfa m’mosakumbukila Inu: M’mandamo adzakuyamikani ndani? (Masalmo 6:5)

Pakuti amoyo adziwa kuti tidzafa; koma akufa sadziwa kanthu bi, sadzalandira mphotho; pakuti angoiwalika. (Mlaliki 9:5)

Tikafa ntchito zonse zamaganizidwe zimatha panthawiyo, kuphatikizapo kuzindikira kwa kanthawi. Nthawi yakuukitsidwa idzawoneka ikubwera nthawi yomweyo titapuma.

Pakuti Ambuye adzatsika Kumwamba mwini yekha ndi mpfuu, ndi mau a mngelo wamkuru, ndi lipenga la Mulungu; ndipo akufa mwa Ambuye adzayamba kuuka. (1 Atesalonika 4:16)

Kuuka kumeneku kudzachitika pakubweranso kwachiwiri kwa Khristu.

Taonani, ndidza msanga; ndipo mphotho yanga ndiri nayo yakupatsa yense monga mwa ntchito yace. (Cibvumbulutso 22:12)

Sitirandira mphotho yathu yamuyaya mpaka Yesu abwere nthawi yachiwiri.

Limene adzalionetsa m'nyengo za Iye yekha, amene ali Mwini Mphamvu wodala ndi wayekha, ndiye Mfumu ya mafumu ndi Mbuye wa ambuye; amene Iye yekha ali nao moyo wosatha, wakukhala m'kuunika kosakhozeka kufikako; amene munthu sanamuona, kapena sakhoza kumuona; kwa Iye kukhale ulemu ndi mphamvu yosatha. Amen. (1 Timoteo 6:15-16)

Mulungu yekha ndiye wosafa. Ife sitiri.

Taonani, ndikuuzani cinsinsi; sitidzagona tonse, koma tonse tidzasandulika m'kamphindi, m'kutwanima kwa diso, pa lipenga lotsiriza; pakuti lipenga lidzalira, ndipo akufa adzaukitsidwa osabvunda, ndipo ife tidzasandulika. Pakuti cobvunda ici ciyenera kubvala

cisabvundi, ndi caimfa ici kubvala cosafa. Ndipo pamene cobvunda ici cikadzabvala cisabvundi ndi caimfa ici cikadzabvala cosafa, pamenepo padzacitika mau olembedwa, Imfayo yamezedwa m'cigonjetso. (2 Akorinto 15:51-54)

Tiribe moyo wosafa mwa ife eni. Kusakhoza kufa kumatheka pokhapokha mwa kulumikizana ndi Mulungu: “Chakufaci chiyenera kubvala chosafa.” Paulo ananenanso kuti, “Sitidzagona tonse.” Iwo omwe ali moyo, mwa Khristu, pakubweranso kwachiwiri sadzamva imfa.

Mmbulu udzakhala pamodzi ndi mwana wa nkhosa, ndipo nyalugwe adzagona pansi ndi mwana wa mbuzi; ndipo mwana wa ng'ombe ndi mwana wa mkango ndi Coweta conenepa pamodzi; ndipo mwana wang'ono adzazitsogolera. Ndipo ng'ombe yaikazi ndi cirombo zidzadya pamodzi; ndipo mkango udzadya udzu ngati ng'ombe. Ndipo mwana wakuyamwa adzasewera pa una wa mamba, ndi mwana woleka kuyamwa adzaika dzanja lace m'pfunkha la mphiri. Sizidzaipitsa, sizidzasakaza m'phiri langa lonse loyera, cifukwa kuti dziko lapansi lidzadzala ndi odziwa Yehova, monga mdazi adzaza nyanja. (Yesaya 11:6-9)

M'dziko lapansi lopangidwa latsopano chilengedwe chonse cha Mulungu chidzabwezeretsedwa ku ungiwo woyambirira wa Edeni. Nyama sizidzaphana kuti zikhale ndi moyo, ndipo sipazakhala zolengedwa zomwe zimawopseza munthu. Sikudzakhala mantha, kuzunzika, kapena kufa.

Ndipo adzawapukutira misozi yonse kuicotsa pamaso pao;
ndipo sipadzakhalanso imfa; ndipo sipadzakhalanso
maliro, kapena kulira, kapena cowawitsa; zoyambazo
zapita.

— Cibvumbulutso 21:4

Mlengi wathu ndi Wotisamalira

Pachiyambi Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi.

— Genesis 1:1

Nawa maziko a sayansi yonse yoona. Mulungu adalenga dziko lathu lapansi. Mulungu anatipanga ife. Sindife zotsatira za ngozi. Pali cholinga cha umulungu chakukhalapo kwathu. Komabe, dziko lathu lamasiku ano ladzaza ndi malingaliro omwe amatsutsana kotheratu ndi mawu omveka bwino amatsegula Mawu a Mulungu. Kukhulupirira kuti kulibe Mulungu kwayesa kubera sayansi ndi cholinga chofuna kuchotsa Mulungu. Nzeruyi yakhala yovuta pa sayansi kwa zaka zopitirira zana.

Sikuti mu buku laling'onoli tingafufuze zambiri zamaumboni wotsimikizira za sayansi yopanga chilengedwe popeza pali mabuku abwino ambiri pamutuwu. Komabe, masiku ano kuli nkhondo yolimbana ndi kukhalapo kwa Mulungu. Pali olemba ndi olankhula odziwika omwe ali ndi owatsatira ambiri omwe ali pa cholinga chofuna kumuchotsa Mulungu. Nchiyani chikuyendetsa gululi, ndipo nchifukwa ninji anthu ambiri akana kukhulupirira mwa Mulungu?

Anthu ambiri woona mtima akupitirizabe kukhala ndi malingaliro wosagwirizana ponena za Mulungu. Unyinji wakula ndi kumva za chikondi cha Mulungu, kungoti chinthu cha Mulungu cha chikondi chawonetsedwa mogwira mtima ndi chinthunzi chopotoka chomwe chimamuwonetsa Iye kukhala mulungu yemwe amalakwiridwa komanso kupsetsedwa mtima msanga. Kuwonjezera pamenepo chikhulupiriro chakuti Mulungu amabwezera adani ake pochita nawo ndi imfa, kuwononga, ndi chizunzo chosatha; nzosavuta kuwona chifukwa chake anthu ambiri amakananso kukhulupirira mwa Mulungu. Koma mwina iwo omwe adakana

kukhulupirira mwa mulungu pomwe chithunzithunzi chopotokaci ndi chomwe adadziwapo kale ndiye kuti sakukana Mulungu konse. Funso lachiwiri lakukhalako kwa Mulungu limakhalapo chifukwa cha funso loyambirira lonena za chikhalidwe cha Mulungu silinakhazikitsidwe m'malingaliro ali onse.

Ndipo anazona Mulungu zonse zimene adazipanga, ndipo, taonani, zinali zabwino ndithu. (Genesis 1:31)

Vesi ili likumaliza nkhani yakulenga. Mulungu sakadakhocha kuwona chirichonse padziko lapansi ngati “chabwino kwambiri” zikadakhala kuti panali imfa ya cholengedwa chake chirichonse isanathe ntchito yake yolenga. Popeza Mulungu sindiye adayambitsa zowawa ndi imfa, izi zitsutsa njira yokhayo yopulumuka kwa amphamvu kwambiri okhaokha munthu asanagwe pomwe zowawa ndi imfa zinabwera mdziko lathu lapansi koyamba.

Njira ya kupulumuka kwa amphamvu kwambiri okhaokha yomwe timawona padziko lathu lapansi lero ndi kusintha kwa nkhanza ku dziko lomwe liri pa njira yopulumuka pa ngozi kuyambira pamene tchimo linalowa. Pali nkhani ya bwino! Kulekanitsidwa kwa chilengedwe ndi Mlengi komwe kunachitika pakugwa kudzachiritsidwa padziko lapansi lokonzedwanso. Lamulo la chikondi lidzakhala njira ya moyo yoponda mpikisano, yopanda mantha, yopanda mavuto, kapena yopandanso imfa. Cholinga choyambirira cha Mulungu cha dziko lathu lapansi chidzakwaniritsidwa.

Pakuti cilengedwere dziko lapansi zaoneka bwino zosaoneka zace ndizo mphamvu yace yosatha ndi umulungu wace; popeza zazindikirika ndi zinthu zolengedwa, kuti iwo adzakhale opanda mau akuwiringula. (Aroma 1:20)

Tikakhala ndi mwayi wophunzira sayansi, tidzayamikira zozizwa zochuluka ndi kaso la zinthu zowoneka mu chilengedwe. Chidindo cha Mulungu chili paliponse. Tikakana kukhalako kwa

Mulungu, tiyenera kukanso kukhalako kwa zozizwitsa, koma tazunguliridwa ndi zozizwitsa: mtengo waukulu, maluwa wosakhwima, kuyimba kwa mbalame, ukonde wa kangaude, chilengedwe chonse, kumwetulira kwa khanda akazindikira amayi ake, mpweya womwe mukupuma pakadali pano. Izi zonse ndi zozizwitsa zapamwamba kwambiri. Sizingathe kufotokozedwa bwino chifukwa zina zirizonse nzoziwitsa. Moyo wonse nchoziwitsa. Umboni ndi wochulukira kuti Mulungu adatipanga ife ndi china chirichonse chomwe chiri ndi moyo. Kuyang'ana chilengedwe chodabwitsa chotizungulira ndikutsimikiza kuti Mulungu sanachilenge sizomveka.

Pakuti atero Yehova amene analenga kumwamba, Iye ndiye Mulungu amene anaumba dziko lapansi, nalipanga; Iye analikhazikitsa, sanalilenga mwacabe; Iye analiumba akhalemo anthu; Ine ndine Yehova; ndipo palibenso wina. (Yesaya 45:18)

Mulungu anapanga dziko lapansi likhale malo athu okhala osatha.

Paciyambi panali Mau, ndipo Mau anali kwa Mulungu, ndipo Mau ndiye Mulungu. Awa anali paciyambi kwa Mulungu. Zonse zinalengedwa ndi Iye; ndipo kopanda Iye sikunalengedwa kanthu kali konse kolengedwa. Ndipo Mawu anasandulika thupi, nakhazikika pakati pa ife, ndipo tinaona ulemerero wace ulemerero wonga wa wobadwa yekha wa Atate, wodzala ndi cisomo ndi coonadi. (Yohane 1:1-3, 14)

Mlengi wathu adakhala m'modzi wa ife kuti awulule bwino momwe Iye aliri.

Pakuona ine thambo la kumwamba lanu, nchito ya zala zanu, Mwezi ndi nyenyezi, zimene munazikhazika, Munthu ndani kuti mumkumbukila? Ndi mwana wa munthu kuti muceza naye? Pakuti munamcepsa

pang’ono ndi angelo, Munambveka iye korona wa ulemero ndi ulemu. Munamcititsa ufumu pa nchito za manja anu; Munagonjetsa zonse pansu pa mapazi ace. (Masalmo 8:3-6)

Banja la anthu linapangidwa “mochepepa pang’ono ndi angelo.” Komabe, iwo omwe adakhalapo padziko lapansi ndipo adayanjanitsidwa ndi Mulungu adzakakhala atakumana ndi zomwe ngakhale “angelo alakalaka kusuzumiramo” (1 Peter 1:12). Kudziwa kwawo za chikondi chozipereka nsembe cha Mulungu kudzawapatsa malo apadera mu chilengengedwe: “Ndipo ndinaona mzinda woyerawo, Yerusalemu watsopano, ulikutsika Kumwamba kwa Mulungu, wokonzedwera mwamuna wace. Ndipo ndinamva mau akuru ocokera ku mpando wacifumu ndi kunena Taonani, cihema ca Mulungu ciri mwa anthu; ndipo adzakhalitsa nao, ndi iwo adzakhalala anthu ace, ndi Mulungu yekha adzakhalala nao, Mulungu wao.” (Cibvumbulutso 21:2-3)

Iye analenga dziko lapansi ndi mphamvu yace, nakhazikitsa dziko lapansi ndi nzeru yace, nayala thambo ndi kuzindikira kwace. (Yeremiya 10:12)

Pakuti mwa Iye tikhala ndi moyo ndi kuyendayenda, ndi kupeza mkhalidwe wathu. (Macitidwe 17:28)

Thambo, dziko lapansi, ndi zolengedwa zonse za moyo zomwe ziri padziko lapansi sizikhalapo popanda Mulungu. Mlengi wathu sanapange dziko lapansi, naliwayinda ngati koloko, kenako ndikulisiya kuti lizigwira ntchito palokha popanda kuwonjezera chirichonse. Mulungu mosalekeza “anyamula zonse ndi mau a mphamvu yace” pakuti “mwa Iye zinthu zonse zigwirizana” (Abebri 1:3; Akolose 1:17).

Ngati mwanyamula galasi la madzi m’dzanja lanu lamanja ndikuganiza kuti muligwetse, kodi mungafunike kugwiritsa dzanja lanu lamanzere kukakamiza dzanja lanu lamanja kuti muligwetse? Mulungu akutiuza kuti, “Inde dzanja langa linakhazika maziko a

dziko lapansi, ndi dzanja langa lamanja linafunyulula m'mwamba; pakuziitana Ine ziimirira pamodzi” (Yesaya 48:13).

Kuganiza kuti Mulungu ndi wowononga kumachepetsa udindo wake monga Wosamalira chilengedwe. Mulungu sayenera kuwononga mwachangu kuti chiwonongeko chichitike. Mwachitsanzo, kuwonongedwe kwa Sodomu ndi Gomora, kutanthauza wamba kumawona Mulungu akupanga moto ndi miyala ya moto kuti awononge zomwe Iye “akugwirizitsa” kapena kusamalira. Chithunzichi cha Mulungu ngati wowononga chimamuyika Iye kuzitsutsa Iye mwini monga momwe inu mungazitsutse ngati mutagwiritsa ntchito dzanja lanu lamanzere kukakamiza dzanja lanu lamanja kugwetsa galasi la madzi.

Kuti Mulungu awononge kumangofuka kuti asiye. Komabe, ndikofunika kumvetsetsa kuti samachita ngakale izi ndi cikhumbo cha imfa kapena chiwonongeko kuti chichitike. Mulungu amalola kusiya kokha chifukwa Iye ndiye chikondi, ndipo chikondi chimafuna ufulu weniweni. Mulungu amapereka munthu kapena mtundu monyinyirika komanso mwachisoni chachikulu: “Ndidzakusiya bwanji, Efraimu? Ndidzakupereka bwanji, Israyeli? Ndidzakuyesa bwanji ngati Adima? Ndidzakuika bwanji ngati Zeboimu? Mtima wanga watembenuka m’kati mwanga, zacifundo zanga zilira zonse pamodzi” (Hoseya 11:8).

Yesu ananena mawu awa polirira Yerusalemu: “Ha, Yerusalemu, Yerusalemu, amene umapha aneneri, ndi kuwaponya miyala iwo otumidwa kwa iwe! Ine ndinafunana kangati kusonkhanitsa pamodzi ana ako, inde monga thadzi lisonkhanitsa anapiye ace m’mapiko ace, koma inu simunafuna ai! Onani, nyumba yanu yasiyidwa kwa inu yabwinja” (Mateyo 23:37-38).

Pakuti Mwana wa munthu sanadza kudzawononga miyoyo ya anthu, koma kuwapulumutsa iwo. (Luka 9:56)

Zakumwamba zimalalikira ulemerero wa Mulungu; Ndipo thambo lionetsa nchito ya manja ace. Usana ndi

usana ucurukitsa mau, Ndipo usiku ndi usiku uonetsa nzeru. Palibe cilankhulidwe, palibe mau; Liu lao silimveka. (Masalmo 19:1-3)

Mulungu amalankhula ndi anthu onse kudzera mu chilengedwe chake. Palibe amene sanaitanidwe kuti aphunzire za Iye chifukwa cha zovuta zazinenero kapena kusowa kwa mawu wosindikizidwa.

Kwezani maso anu kumwamba, muone amene analenga izo, amene aturutsa khamu lao ndi kuziwerenga; azicha zonse maina ao, ndi mphamvu zace zazikuru, ndi popeza ali wolimba mphamvu, palibe imodzi isoweka.

— Yesaya 40:26

Titha Bwanji Kukhala Ndi Moyo Wamuyaya?

Koyambirira kwa bukuli tidawerenga za kugwa kwa anthu zolembedwa mu Genesis, mutu wachitatu. Njoka, wonyenga wodzibisa, idapangitsa Adamu ndi Hava kukhulupirira kuti Mulungu amadzikonda ndipo sangakhulupirike. Atakhulupirira bodza lija, adafuna kudzipatula okha kwa Wopatsa Moyo wawo, ndipo kufa kwa iwo kunayamba.

Imfa zonse kuyambira tsiku limenero ndi zotsatira zakukhulupirira bodza lonena za Mulungu. Anthu adasiyana ndi Mulungu mu munda wa Edeni chifukwa Adamu ndi Hava adasintha malingaliro awo okhudza Mulungu. Pamene kale ankakhulupirira Iye, tsopano samamukhulupirira Iye. Ili ndilo vuto lathu lenileni. Zomwe tikusowa ndikusintha malingaliro athu okhudza Mulungu. Tikachita izi kudalira kumachotsa kusadalira, ndipo chikondi chidzachotsa mantha pa Iye. Tidzayanjananso ndi Mlengi wathu, ndipo tidzakhala ndi moyo wosatha.

Adamu ndi Hava atakhulupirira bodza la njoka ponena za Mulungu ndikufunafuna kubisala kuchoka kwa Iye, Mulungu mwini sanasinthike ndi zomwe zidachitika. Chikondi chake kwa ana ake omwe tsopano ali otalikirana ndi Iye sichinachepe konse. Dongosolo lililonse la chipulumutso lomwe limadalira kuyetsetsa kwathu kuti tisinthe malingaliro a Mulungu za ife lofuna njira yothetsera vuto lomwe kulibe. Mulungu ali kale ndi malingaliro abwino kwa ife ndipo safuna kukakamizidwa kulikonse kuti atiganizire bwino. Iye amatikonda kale ndipo amawerengera aliyense wa ife.

Mulungu atatulutsa Aisrayeli ku Aigupto, iwo anachenjezedwa za kuopsa kwa kupembedza mafano. Milungu yonyengayi inali yofala munthawi za mu Baibulo ndipo yinali yopangidwa ndi malingaliro olakwika. Nthawi zambiri imadziwika kuti inali yokwiya ndipo imafuna kusangalatsidwa. Nsembe ndi zopereka zimaperekedwa kuti athetse mkwiyo yawo. Titha kufunsa mozama

kuti: Kodi njira yathu yokhudzana ndi Mulungu imabwerekera chirichonse kuchokera ku kupembedza mafano kwakale?

Koma moyo wosatha ndi uwu, kuti akadziwe Inu Mulungu woona yekha, ndi Yesu Kristu amene munamtuma. Ine ndalemekeza Inu pa dziko lapansi, m'mene ndinatsiriza nchito imene munandipatsa ndicite. (Yohane 17:3-4)

Mu pemphero ili la Yesu kwa Atate wake, akufotokoza momveka bwino moyo wosatha. Ndicho chokumana nacho chodziwa Mulungu. Kudziwa izi kumatijanitsa ife ndi Wotipatsa Moyo wathu. Timayamba kuwona cholinga chenicheni cha utumiki wa Yesu ku dziko lathu – kuwulula molondola Mulungu kuti ndi wosadzikonda, wokoma mtima, wofatsa, wachifundo, komanso wokhululuka. Anthu akamamvera mawu a Yesu, anali kumva mawu a Mulungu. Pamene anthu adamuwona Yesu akuchiritsa odwala, kudyetsa anjala, kupereka chirimbitso, atanyamula ana pamiyendo pake, ndikudzilola kuti asamvetsedwe ndi kunyozedwa, anali kuwona Mulungu – Mulungu mu ulemerero wake.

Pofuna kupewa chisokonekero, ndikofunikira kumvetsetsa kuti pali njira zambiri zopereka chipulumutso, koma zonsezi zimapereka chithunzi chotsutsana ndi cha Mulungu. Kafukufukuyu aganizira njira imodzi yodziwika ya chipulumutso yomwe pafupifupi aliyense mchigawo Chakumadzulo adakumana nayo. Anthu ambiri oona mtima amatsatira njirayi. Awa ndi malingaliro akuti chipulumutso ndi nkhani ya lamulo.

Makhalidwe ena mwa malingaliro awa akuphatikizapo:

- Kogogomezwa za ulamuliro wa Mulungu m'malo mwa mphatso ya ufulu wa Mulungu kwa ana ake.
- Kulimbikitsa pa mphamvu ya Mulungu yopulumutsa m'malo mwa khumbo la Mulungu kutijanitsa ife kwa Iye.
- Chikhulupiriro choti Mulungu ndi woyera komanso wopatulika koteru kuti amakwiysidwa ndi machimo athu m'malo mokhulupirira kuti Mulungu amatikonda ndipo

amafuna kutiyandikira monga momwe ife tilili. Mulungu amamva chisoni ndi tchimo chifukwa cha zomwe limachita kwa omwe amawakonda, osati chifukwa Iye pa yekha wakwiyitsidwa ndi tchimolo.

- Chikhupiriro chakuti Mulungu amafuna magazi kuti athetse mkwiyo wake m'malo momvetsetsa kuti Mulungu akufuna kutichiritsa ku matenda a mantha athu za Iye. Amafuna kuti timvetsetse kuti ndi uchimo womwe ndi wakupha – osati Iye.
- Chikhulupiriro chakuti Mulungu akusunga mbiri ya machimo athu kuti adzagwiritse ntchito pa ife pa chiweruzo chomwe chikubwera m'malo momvetsetsa kuti cholembedwa chirichonse chidzasungidwe chidzawonetse kuti Mulungu adachita zonse zomwe akadatha kupulumutsa munthu aliyense.
- Lingaliro loti Mulungu amapereka zilango chifukwa chophwanya malamulo ake m'malo momvetsetsa kuti ndi kudzikonda kwathu, posagwirizana ndi lamulo la chikondi, lomwe limatilanga. Monga momwe sitingaphwanye malamulo a chilengedwe popanda kulangidwa, sitingaphwanye lamulo la chikondi popanda chilango.
- Kutanthauzira uthenga wabwino ngati uthenga wabwino womwe Mulungu amapereka chifukwa chophwanya lamulo lake m'malo modziwa kuti uthenga wabwino umanena za Mulungu mwini. Mulungu akadakhala munthu amene angapereke chilango cha imfa chifukwa chophwanya malamulo ake, ikadakhala nkhani yoyipa.
- Malingaliro opulumutsa m'malo momuwona Mulungu ngati wodalirika. Kunena zowona, tikamaika chidwi chathu chonse pa zowona za Mulungu wathu wofatsa, sitidzakhanso ndi nkhwana za chipulumutso chathu, ndi pamene tidzakonda kwambiri kuwerengera ena: “Pakuti yense wakufuna kupulumutsa moyo wace adzautaya; ndipo yense wakataya moyo wace cifukwa ca Ine, ndi cifukwa ca Uthenga Wabwino, adzaupulumutsa” (Marko 8:35).

Uthenga wa lamulo nthawi zonse umalimbikitsa chidwi chosafunikira pakukhala ndi chitsimikizo cha chipulumutso. Mulungu sanatipatsenso mtolo wofuna kudziwa za chipulumutso cha wina aliyense – kuphatikizapo chathu. M'malo mongoyang'ana momwe moyo wathu wa uzimu ulili, tiyenera kuyang'ana pa Iye amene nthawi zonse amationa aliyense wa ife osati momwe tilili kokha koma momwe ife tingakhalire. Mulungu amakonda ndi kuwerengera aliyense wa ife koposa momwe tingadzikondere ndi kudziwerengera tokha. Mosakaika konse, Mulungu akufuna kuti aliyense wa ife tikhale naye kwamuyaya. Iye akufunanso kuti timvetsetse kuti Iye ndiwodalirika kotheratu ndipo ndiwoposa kuthekera kuchiritsa malingaliro athu a mantha: “Mulibe mantha m'cikondi; koma cikondi cangwiro citaya kunja mantha” (1 Yohane 4:18).

Tafanizira mwachidule mauthenga awiri osiyana: uthenga wa lamulo ndi uthenga wochiritsa. Uthenga wabwino wochiritsa ukugwirizana kwathunthu ndi ziphunzitso ndi chitsanzo cha Yesu, pomwe uthenga wa lamulo umafanana kwambiri ndi makhoti a dziko lapansi omwe adagwiritsa ntchito kuweruza Yesu (Mchiritsi wathu wofatsa) ku imfa.

Pakuti ndidziwa malingaliro amene ndilingirira inu, ati Yehova, malingaliriro a mtendere, si a coipa, akupatsani inu adzukulu ndi ciyembekezero. (Yeremiya 29:11)

Nthawi yayikulu, khama, ndi ndalama zomwe timagwiritsidwa ntchito potengera za chipembedzo, ndi cholinga chofuna kukopa Mulungu kuti Mulungu atiganizire, zakhala zopanda pake.

Tayani, ndi kudzicotsera zolakwa zanu zonse zimene munalakwa nazo, ndi kudzifunira mtima watsopano; pakuti mudzaferanji inu, nyumba ya Israyeli? Pakuti sindikondwera nayo imfa ya wakufayo, ati Ambuye Yehova; cifukwa cace bwererani, nimukhale ndi moyo. (Ezekieli 18:31-32)

Pempho la Mulungu kwa aliynse wa ife ndi kutembenuka kuchokera ku kudzikonda kunka ku njira ya moyo.

Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira Iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha. Pakuti Mulungu sanatuma Mwana wace ku dziko lapansi, kuti akaweruze dziko lapansi, koma kuti dziko lapansi likapulumutsidwe ndi Iye. (Yohane 3:16-17)

Kukhulupirira Yesu ndiko kukhulupirira zomwe adaulula za Iye (Mwana wa Mulungu) ndi Mulungu Atate.

Ndipo kunena kuti Mulungu anali mwa Kristu, alinkuyanjanitsa dziko lapansi kwa Iye yekha, osawawerengera zolakwa zao; ndipo anaikiza kwa ife mau a cayanjanitso. (2 Akorinto 5:19)

Ngati kuyetsetsa konse kwa Mulungu kutipulumutsa ku imfa yosatha kukhoza kufotokozedwa mwachidule ndi mawu amodzi, mawuwo akhoza kukhala kuyanjanitsidwa.

Ndipo inu, okhala alendo kale ndi adani m'cifukwa canu m'nchito zoipazo, koma tsopano anakuyanjanitsani. (Akolose 1:21)

Chiyambireni kugwa kwa anthu, chidwi chodzipatula chakhala chokhazikika m'malingaliro athu okha – osati mwa Mulungu.

Pakuti Mulungu amene anati, Kuunika kudzawala kuturuka mundima, ndiye amene anawala m'mitima yathu kutipatsa ciwalitsiro ca cidziwitso ca ulemerero wa Mulungu pankhope pa Yesu Kristu. (2 Akorinto 4:6)

Mdima womwe vesiri likunena ndiko kusamvetsetsa kwathu za Mulungu. Ulemerero wa Mulungu ndi khalidwe lake, lomwe limawonekera m'khope ya Yesu.

Koma ife tonse ndi nkhope yosaphimbika popenyerera monga mwa kalirole ulemerero wa Ambuye, tisandulika m'cithunzithunzi comweci kucokera kuulemerero kumka kuulemerero, monga ngati kucokera kwa Mzimu wa Ambuye. (2 Akorinto 3:18)

Timasinthika pakuwona. Mfundo imeneyi imagwira ntchito njira zonse ziwiri. Ngati tikhulupirira kuti Mulungu amadzikonda, zimalimbitsa kudzikonda kwathu. Ngati timuwona ngati wosadzikonda, zithandizira kuthetsa kudzikonda kwathu. Kulingalira za chikondi, chifundo, ndi kukhululukira kwa Mulungu kumatithandizira kukhala ndi makhalidwe omwewo mwa ife.

Ndinena kwa inu, kotero kudzakhala cimwemwe Kumwamba cifukwa ca wocimwa mmodzi wotembenuka mtima, koposa anthu olungama makumi asanu ndi anai mphambu asanu ndi anai, amene alibe kusowa kutembenuka mtima. (Luka 15:7)

Kulapa sikutanthauza kuti “Pepani” kwa Mulungu. Kulapa kumatanthauza kutembenuka, kapena kusintha malingaliro. Kulapa kowona, potengera zomwe Yesu anaphunzitsa, kumatanthauza kusintha malingaliro za Mulungu. Tidzamuwona Iye monga momwe Yesu adamuyimilila Iye molondola.

Idzani kuno kwa Ine nonsenu akulema ndi akuthodwa, ndipo Ine ndidzakupumulitsani inu. Senzani gori langa, ndipo phunzirani kwa Ine; cifukwa ndiri wofatsa ndi wodzicepetsa mtima: ndipo mudzapeza mpumulo wa miyoyo yanu. Pakuti gori langa liri lofewa, ndi katundu wanga ali wo pepuka. (Mateyu 11:28-30)

Sizifunika kugwira nthito kuti tikhale abwino pakuyesera kopanda pake podzikulitsa mwauzimu. Kuyesetsa kwathu kuti tichite izi kumatipangitsa kuti tizingodziyang'ana tokha ndipo zingadzitse kunyada kapena kukhumudwitsidwa. Yesu ali ndi yankho ku vuto lathu. Iye amangoti, “Phunzirani za Ine.”

Ndipo anapereka kwa Iye buku la Yesaya mneneri. Ndipo m'mene Iye adafunyulula bukulo, anapeza pomwe panalembedwa, Mzimu wa Ambuye uli pa Ine, Cifukwa cace Iye anandidzoza Ine ndiuze anthu osauka Uthenga Wabwino; Anandituma Ine kulalikira am'nsinga mamasulidwe, Ndi akhungu kuti apenyenso, Kumasula iwo amene adatunduzidwa. (Luka 4:17-18)

Tonsefe timafuna zomwe Yesu anabwera kudzakwaniritsa kwa ife, palibe kuchotserapo.

Tiyenera Kuopa Chiweruzo?

Poganizira za chiweruzo, zingakhale zothandiza kudziwa kaye yemwe akuweruzidwa komanso amene akuweruza. Kubwereranso ku kukambirana pakati pa Hava ndi njoka mu munda wa Edeni, kumbukirani kuti njoka inayika m'maganizo a Hava funso lokhudza chilungamo, kukoma mtima, ndi kukhulupirika kwa Mulungu. Poganizira mozama, zidzawonekeratu kuti sanali anthu omwe amayesedwa pamene – anali Mulungu.

Zingakhale zovuta kwa ife kumvetsetsa lingaliro loti Mulungu adalola kuti ayasedwe. Komabe, lingaliroli ndi lokhalo lomwe lingathe kufikiridwa potengera kuphuzira Baiulo mozama. Takhala tikuweruza Mulungu mosadziwa kuyambira pokambirana koyamba ndi mdierekezi. Kodi tamuweruza Iye mwachilungamo?

Pamene ife tasoheretsedwa mu makhaliidwe athu poziyika tokha pakatikati pa chiweruzo, ife ndife osamasulidwa pamene ikubwera nkhani yokhuzidwa ndi chiweruzo. Mulungu sanatiyike ife pa kuyesedwa; komabe, tiri ndi luso loziweruza ndi kuzitsutsa tokha. Yesu ananena kuti mawu amene ananena ndi a moyo. Tiri ndi mwayi mwina kumvomereza kapena kukana mawu ake. Ngati mawu ake alidi ndi moyo, ndipo tawakana, si ndiye kuti tazipanga chiweruzo ndi zotsatira zoipa pa ife tokha?

Mulungu samapereka chiweruzo monga zimachitikira ku khoti. Pamene tatsimikiza mtima kuyenda pa njira ya kudzitsutsa ndi imfa, Mulungu sangachitenso china chirichose kupatula kutsimikizira chisankho chathu monyinyirika.

Palonso mbali yina ya chiweruzo yoyenera kuilingalira. Pamene tikuweruza ena, zimatikhuza ife molakwika. Pamene tikutsutsa ena, ife timangodzitsutsa tokha potero. Kutu tiwone yemwe tiyenera kumuwopa pa chiweruzo, tiyenera kuyang'ana pa galasi.

Nkhani ya bwino ya mzimayi amene anagwidwa akuchita chigololo ikutipatsa fanizo la momwe chiweruziro chimagwirira ntchito:

Koma Yesu anamuka ku phiri la Azitona. Koma mamawa anadzanso ku Kacisi, ndipo anthu ose anadza kwa Iye; ndipo m'mene anakhala pansi anawaphunzitsa. Koma alembi ndi Afarisi anabwera naye kwa Iye mkazi wogwidwa m'cigololo, ndipo pamene anamuimika iye pakati. Ananena kwa Iye, Mphunzitsi, mkazi uyu wagwidwa alimkucita cigololo. Koma m'cilamulo Mose anatilamulira, tiwapoye miyala otere. Cifukwa cace Inu munena ciani za iye? Koma ici ananena kuti amuyese Iye, kuti akhale naco comneneza Iye. Koma Yesu, m'mene adawerama pansi analemba pansi ndi cala cace. Koma pamene anakhalakhala alikumfunsabe Iye, anaweramuka, nati kwa iwo, Amene mwa inu ali wopanda cimo, ayambe kumponya mwala. Ndipo pamene anaweramanso analemba ndi cala cace pansi. Koma iwo, m'mene adamva, anaturukamo amodzi amodzi, kuyambira akulu, kufikira otsiriza; ndipo Yesu anatsala yekha, ndi mkazi, alikuima pakati. Koma Yesu pamene adaweramuka, anati kwa iye, Mkazi iwe, ali kuti ajawa? Palibe munthu anakutsutsa kodi? Koma iye anati, Palibe, Ambuye. Ndipo Yesu anati, Inenso sindikutsutsa iwe; pita; kuyambira tsopano usacimwenso. (Yohane 8:1-11)

Mkazi adambweretsa pamaso pa Yesu ndikuwonetsedwa ngati woswa lamulo anali wozunzidwa wogwiritsidwa ntchito ndi atsogoleri achipembedzo pofuna iwo kuyesa kuwononga Yesu yemwe amamuwona ngati wowopseza chipembedzo chawo. Otsutsa mkaziyo adagwiritsa ntchito chilamulo cha Mose. Pakukumana kwina ndi Afarisi, pokhudzana ndi chisudzulo, Yesu adawauza kuti chilamulo cha Mose chinali ndi zolola za m'mitima yawo yowuma:

“Koma Yesu anati kwa iwo, Cifukwa ca kuuma kwa mitima yanu anakulemberani lamulo ili” (Marko 10:5).

Kukula kwa zomwe zidachitika mu bwaloli kudzawonekera poyera ife tikadziwa kuti Yesu anali Mulungu pa dziko lapansi ndi mphamvu zonse za umulungu, kuphatikizapo ufulu wopereka chiweruzo. Yesu sanapereke chiweruzo nthawi yomweyo pa mlandu womwe anabweretsa kwa Iye, koma m’ malo mwake anawerama ndi kulemba ndi chala chake pansi. Atamakamiza kuti ayankhe funso lawo, adati kwa iwo, “Amene alibe tchimo pakati panu, ayambe kumponya mwala.” Kenako adapitiriza kulemba pansi.

Yesu anali ndi cholinga mu zimene ananena ndi kuchita. Polemba pansi, sikunali kuthawa funso la atsogoleri a chipembedzo. Ankadziwa zomwe iwo adambweretsera mkaziyo kwa Iye. Yesu ankadziwanso mbiri ya aliyense womuneneza iye ndipo adawerenga malingaliro ndi zolinga zawo. Akadatha kudzudzula wonyengawo pamaso pa mbonizo. M’ malo mwake, mwachifundo adapangitsa atsogoleri a chipembedzo kuzindikira machimo awo powalemba mu fumbi – mbiri yapadera yolembedwa yosakhazikika ya machimo awo.

Yesu anakonda ndi kuwerengera kwambiri munthu aliyense amene anasonkhana momuzungulira posaganizira zinthu zomwe zinawabweretsa pamodzi. Ntchito yake inali yopulumutsa dziko lapansi, ndipo Iye adafunafuna kuyanjanitsa mkaziyo ndi omwe anamutsutsa iye, omwe Iye analibe khumbo lowataya kutali.

Yesu anati kwa atsogoleri achipembedzo, “Iye alibe tchimo pakati panu, ayambe kumponya mwala.” Apa amapereka udindo woweruza kwa iwo. Yesu sanabwere ku dziko lino kuti adzaweruze ndi kutsutsa, ndipo Iye sakanamkakhizira pa udindo woweruza. Kodi amlembi ndi Afarisi adatenga mawu a Yesu ngati kuwayitanira kuti amuponye miyala mkaziyo? Mwachiwonekere ayi, popeza onse adaturuka pa malopo “m’modzi m’modzi.”

Yesu, monga Mulungu, sanamutsutse mayiyu, koma m’ mawu ake akuti “pita, usakachimwense,” anamutsegulira iye khoma la

njira ya moyo. Sanali kumulamula kuti angosiya zomwe zinamupangitsa kuti abwere pamaso pake; Iye anali kumupatsa ufulu wochoka ku uchimo wakupha – chikhulupiriro chakuti Mulungu siwofunika kumukhulupirira.

Yesu adamupatsa mayiyu njira yopewera kutsutsika kwa mtsogolo. Anaulula chikondi cha Mulungu kwa iye monga munthu. Mkazi uyu anali pamaso pa Wopatsa Moyo, ndipo adadziwa kuti akhoza kumukonda ndi kumudalira. Maganizo ake wokhuza Mulungu komanso ubale wake ndi Iye zidasinthidwa kwambiri pambuyo pa kukumanaku. Kwa iye, chiweruzo chomwe chinachitika kunali kosintha moyo ndiponso kopereka moyo.

Yesu sanatsutse alembi ndi Afarisi ouma mtima omwe anali ofulumira kutsutsa mayiyu, koma anakweza galasi la uzimu patsogolo pawo lomwe linawonetsa makhaliidwe awo woipa. Zotsatira zake “adatsutsidwa ndi chikumbumtima chawo,” ndipo adamva kukakamizidwa kuchoka pamaso pa chikondi choyera chosadzikonda cha Wopatsa Moyo. Iwo adabwera kudzatsutsa wina, koma adadzitsutsa okha m’ malo mwake.

Cifukwa cace uli wopanda mau owiringula, munthu iwe, amene uli yense wakuweruza; pakuti m’mene uweruza wina, momwemo udzitsutsa iwe wekha, pakuti iwe wakuweruza, umacita zomwezo. Ndipo tidziwa kuti kuweruza kwa Mulungu kuli koonpa pa iwo akucita zotere. Ndipo uganiza kodi, munthu iwe, amene umaweruza iwo akucita zotere, ndipo uzicitanso iwe mwini, kuti udzapulumuka pa mlandu wa Mulungu? (Aroma 2:1-3)

Mulungu amapatsa kwa aliyense wa ife ufulu weniweni. Chiweruzo cha Mulungu pano ndikutsimikizira kwake monyinyirika kudzitsutsa tokha uku tikasankha kukhala kunja kwa mkombero wobwezera wa chikondi ndi moyo. Palibe kothawira ku chiweruzo ichi popeza Mulungu sangatikakamize, motsutsana ndi chifuniro chathu, kuyenda mu njira yopita ku moyo.

Pakuti Atate saweruza munthu ali yense, koma anapereka kuweruza konse kwa Mwana. (Yohane 5:22)

Mulungu, Atate, satiweruza ife.

Wopatsa moyo ndi mzimu; thupi silithandiza konse. Mau amene ndalankkula ndi inu ndiwo mzimu, ndi moyo. (Yohane 6:63)

Mawu a Yesu ndi moyo. Mu liwu liri lonse limene Yesu adanena adaulula chikondi choyanjanitsa cha Mulungu.

Koma Yesu anapfuula nati, Iye wokhulupirira Ine, sakhulupirira Ine, koma Iye wondituma Ine. Ndipo wondiona Ine aona amene anandituma Ine. Ndadza Ine kuunika ku dziko lapansi, kuti yense wokhulupirira Ine asakhale mumdima. Ndipo ngati wina akumva mau anga, ndi kusawasunga, Ine sindimweruza; pakuti sindinadza kudzaweruza dziko lapansi, koma kuti ndipulumutse dziko lapansi. Iye amene akaniza Ine, ndi kusalandira mau anga, ali naye woweruza iye; mau amene ndalankhula , iwowa adzamweruza tsiku lomariza. (Yohane 12:44-48)

Yesu satiweruza ife. Mulungu amatipatsa Mawu a Moyo, koma Iye sadzaticakamiza ife kuti tiwalandire.

Musaweruze, kuti mungaweruzidwe. Pakuti ndi kuweruza kumene muweruza nako, inunso mudzaweruzidwa; ndipo ndi muyeso umene muyesa nao, kudzayesedwa kwa inunso. Ndipo upenya bwanji kacitsotso kali m'diso la mbale wako, koma mtanda uli m'diso la iwe mwini suuganizira? Kapena udziti bwanji kwa mbale wako, Tandilola ndicotse kacitsotso m'diso lako; ndipo ona, mtandawo ulimo m'diso lakoli. Wonyenga iwe! Tayamba kucotsa m'diso lako mtandawo, ndipo pomwepo udzapenyetsa kucotsa kacitsotso m'diso la mbale wako. (Mateyu 7:1-5)

Ngati Mulungu satiweruza ife ndipo Yesu satiweruza ife, bwanji ife tingaganize kuti ndife oyenera kuweruza ena pamene tikhala ndi mzimu woweruza (mtanda m'diso lathu)?

Indetu, indetu, ndinena kwa inu, kuti iye wakumva mau anga, ndi kukhulupirira Iye amene anandituma Ine, ali nao moyo wosatha, ndipo salowa m'kuweruza, koma wacokera kuimfa, nalowa m'moyo. (Yohane 5:24)

Kumvetsetsa chowonadi chonena za Mulungu ndi kuphunzira kumukhulupirira Iye kumatsogolera ku moyo. Yesu anati, “Wokhulupirira Iye saweruzidwa; wosakhulupirira waweruzidwa ngakhale tsopano, cifukwa sanakhulupirira dzina la Mwana wobadwa yekha wa Mulungu” (Yohane 3:18).

Ndipo Paulo ndi Barnaba analimbika mtima ponena, nati, Kunafunika kuti mau a Mulungu ayambe alankhulidwe kwa inu. Popeza muwakankha, nimudziyesera nokha osayera moyo wosatha, taonani, titembenukira kwa amitundu. (Macitidwe 13:46)

Ichi ndi chitsanzo chowunikira chodzitsutsa.

Musaweruze, ndipo simudzaweruzidwa: ndipo musawatsutsa, ndipo simudzatsutsidwa: khululukirani, ndipo mudzakhulukidwa. (Luka 6:37)

Mu uthenga wabwino wa Luka, fanizo la mwana wolowerera limaphunzitsa kuti Mulungu watikhulukira kale ife tisanapemphe. Ife ngati tiweruzidwa, kutsutsidwa, kapena kusakhulukidwa, ndife tokha amene tiri ndi vuto “pakuti cimene munthu acifesa, cimenenso adzaciduta” (Agalatiya 6:7).

Ndipo Yesu anati, Kudzaweruza ndadza Ine ku dziko lino lapansi, kuti iwo osapenya apenye; ndi kuti iwo akupenya akhale osaona. Ndipo Afarisi ena akukhala ndi Iye anamva izi, nati kwa Iye, Kodi ifenso ndife osaona?

Yesu anti kwa iwo, Mukadakhala osaona simukadakhala nalo cimo; koma tsopano munena, kuti, Tipenya: cimo lanu likhala. (Yohane 9:39-41)

Kodi “chiweruziro” chomwe Yesu adabwerera mu dziko lapansi ndi chiyani? Iye adabwera mu dziko lapansi kudzaulula za chikondi cha Mulungu pa anthu ndi phindu lopanda malire lomwe amapereka kwa aliyense wa ife. Iye amafuna ife kuti tiziwonana monga momwe amatiwonera Iye, ndikutu tiziwerengerana momwe Iye amatiwerengera ife. Yesu amatiphunzitsa ife kuti tikhale akhungu ku machimo a ena komanso kuzopanga zosiyanyitsa zomwe zimatigawa: magawano, kukonda dziko lako, kusankhana mitundu, ndale zirizonse, kapena chida chirichonse chomwe chimatirimbikitsa kuthana mu maganizo.

Afarisi sanamvetse phunziro ili lomwe Yesu amaphunzitsa. Iwo anali gulu lowopsa ndipo amayang’ana Amitundu, omwe sanali Achiyuda, ngati agalu. Iwo analinso akatswiri wodzipangira okha ndi kuyang’ana machimo a ena ndi kuwaweruza molingana nawo.

Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira Iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha. Pakuti Mulungu sanatuma Mwana wace ku dziko lapansi, kuti akaweruze dziko lapansi, koma kuti dziko lapansi likapulumsidwe ndi Iye. Wokhulupirira Iye saweruzidwa; wosakhulupira waweruzidwa ngakhale tsopano, cifukwa sanakhulupirira dzina la Mwana wobadwa yekha wa Mulungu. Koma ciweruziro ndi ici, kutikuunika kunadza ku dziko lapansi, ndipo anthu anakonda mdima koposa kuunika; pakuti nchito zao zinali zoipa. (Yohane 3:16-19)

M’ndimeyi, dzina likutanthauza chikhalidwe. Kukana vumbulutso la chikhalidwe cha Mulungu chomwe Yesu adawunikira ndiko kukana Mulungu. Mwa Yesu, Mulungu akuti – ichi ndi chomwe Ine ndilili.

Ndipo pakudza mamawa, ansembe akuru ndi akuru a anthu onse anakhala upo wakumcitira Yesu, kuti amuphe; ndipo anammanga Iye, namuka naye, nampereka Iye kwa Pilato kazembeyo. (Mteyu 27:1-2)

Ndi chithunzi bwanji ichi! Opembedza odzazidwa ndi uchimo omwe akufuna imfa ya Wopatsa Moyo wawo, ndipo Iye sakuwakaniza iwo, kapena ngakhale kupereka chiweruziro pa iwo. Kodi ndi ndani kapena ndi chiyani chomwe chiri chowopsa – Mulungu kapena tchimo?

Timawerenga ndi kumva za nthawi maola omaliza a Yesu asanamwalire popanda kuzindikira tanthauzo lakuya kumbuyo kwa kuzengedwa kwake ndi kupachikidwa. Yesu ndi Mulungu wathunthu komanso munthu wathunthu. Pamene Yesu ankazengedwa pamaso pa Pilato, Iye anali Mulungu wathunthu. Pamene Iye anaweruzidwa ndi kutsutsidwa, Iye anali Mulungu wathunthu. Pamene Iye adakwapulidwa, kunyozedwa, ndi kupachikidwa pa mtanda kuti afe Iye anali, panthawiyi, Mulungu wathunthu.

Mulungu adalola kuti azengedwe ndi kutsutsidwa ndi omwe amawakonda ndipo analakalaka kuti ayanjanitsidwe ndi Iye. Chifukwa chiyani? Chifukwa tili ndi nthawi yovuta kwambiri kuwona zomwe tchimo lathu lachita kwa Iye.

Yesu, Mwana wa Mulungu, anazunzidwa kwambiri m’maola omaliza a moyo wake pa dziko lapansi – kuposa momwe ife tingaganizire. Koma kuzunzika kwa Yesu sikunayambire m’munda wa Getsemane, ndipo sikunathe ndi mawu ake akumwalira ali pa mtanda. Mulungu wazunzika ndi ife ndi chifukwa cha ife chiyambire pamene uchimo utalowa koyamba mdziko lathu, ndipo apitirira kuzunzika nafe limodzi ndi chifukwa cha ife mpaka tsiku lomwe tchimo lachita kuwononga kwake ndipo kuzunzidwa konse ndi imfa zidzatha kwa muyaya.

Kuzengedwa ndi kuzunzika kwa Yesu m’manja mwa omwe adawalenga kuti agawane nawo chikondi chake chopanda malire

kuyenera kutipatsa chithunzuthunzi cha mazunzo omwe tapatsa Mulungu kwa zaka zikwi zambiri. Tikupitirizabe kuyitanira Mulungu ku bwalo la milandu lathu kuti ayankhe milandu ya kuchita zolakwa, kulephera, kusachita kanthu, kudzikweza, ndipo ngakhale kuwononga koopsa. Nthawi zambiri chigamulo chathu chimakhala ndi mlandu ngati momwe taweruzira! Ndi chiyani china chomwe Mulungu angachite kuti ayanjanitse ana ake omwe athawa koposa momwe wachitira? Mtanda ndi chida cha umulungu cha chiyanjanitso. Mtanda umathetsa mkangano wa Satana woti Mulungu ndi wodzikonda, wosasamala, komanso wosadalilika.

Ngakhale momwe tinadetsera chikhalidwe cha Mulungu, pali nkhani yabwino – Mulungu amadziwa chifukwa chake sitimamumvetsetsa Iye, ndipo Iye satitsutsa ife chifukwa cha ichi. Iye adzapitirizabe kutikonda ife ngakhale tili osayamika pazomwe anatichitira ndipo akupitirizabe kutichitira tsiku ndi tsiku. Koma sizingakhale zabwino kwa Mulungu ngati tingadzindikire kuti sizokhudza ife tokha; Mlengi wathu zimamukhudzanso kwambiri pa vuto lathuli. Kodi tingaganizire za Iye? Kodi ife tingalole kumuwona Iye momwe alili – chikondi chosasunthika, chokonda ena, ndikubwezera chikondi chomuyenera Iye? Kodi ndikufunsa kochulukana uku? “Timamukonda, chifukwa anayamba Iye kutikonda” (1 Yohane 4:19).

M'mazunzo ao onse Iye anazunzidwa, ndipo mthenga wakuimirira pamaso pace anawapulumsa; m'kukonda kwace ndi m'cisoni cace Iye anawaombola, nawabereka nawanyamula masiku onse akale.

— Yesaya 63:9

Kodi Chiweruziro cha Mulungu Chimawoneka Motani?

Phunzirani kuchita zabwino; funani chiweruzo; thandizani osautsidwa, weruzirani ana amasiye, munenere akazi amasiye.

— Yesaya 1:17

Chiweruzo cha Mulungu sichotipatsa ife chiganizo chotiweruza ndi kutipatsa chilango. Chikutanthauza pano ngati kuthetsa mavuto ndi kulimbikitsa chilungamo m'dziko lopanda chilungamo.

Taona mnyamata wanga, amene ndinamsankha, Wokondedwa wanga, amene moyo wanga ukondwera naye; Pa Iye adzaika Mzimu wanga, Ndipo Iye adzalalikira ciweruzo kwa akunja. Sadzalimbana, sadzapfuula, Ngakhale mmodzi sadzamva mau ace m'makwalala; Bango lophwayika sadzalityola, Ndi nyali yofuka sadzaizima, Kufikira Iye adzatumiza ciweruzo cikagonjetse. Ndipo akunja adzakhulupirira dzina lace. (Mateyu 12:18-21)

Kuweruza mwachilungamo ndiponso mofatsa kwa Mulungu kumapangitsa anthu kukhulupirirana.

Pakukolola dzinthu za m'dziko mwanu, usamakololetsa m'mpheapete mwa munda wako, nusamakunkha khunkha. Usamakunkha khunkha la m'munda wako wamphesa, usamazitola zidagwazi za m'munda wako wamphesa; uzisiyire wosauka ndi mlendo; Ine ndine Yehova Mulungu wanu. (Levitiko 19:9-10)

Mulungu amafuna athandize osowa pa gulu la anthu akale.

Ndipo mlendo akagonera m'dziko mwanu, musamamsautsa. Mlendo wakugona kwa inu mumuyese pakati pa inu monga wa m'dziko momwemo; popeza munali alendo m'dziko la Aigupto; Ine ndine Yehova Mulungu wanu. Musamacita cisalungamo poweruza mlandu, poyesa utali wace, kulemera kwace, kapena kucuruka kwace. Mukhale naco coyeseera coona, muyeso yoona, efa woona, hini woona; Ine ndine Yehova Mulungu wanu, amene ndinakuturutsani m'dziko la Aigupto. (Levitiko 19:33-36)

Tsoka kwa iwo amene alamulira osalungama, ndi kwa alembi olemba mphulupulu; kuwapatulira osowa kuciweruziro, ndi kucotsera anthu anga aumphawi zoyera zao, kuti alandire za akazi amasiye, nafunkhire ana amasiye! (Yesaya 10:1-2)

Mulungu ndi wophatikiza – ndi Iye palibe akunja. Mulungu amadziwa malamulo a anthu, zochitika za bizinesi, ndi mabungwe omwe amapindulitsa anthu olemera pozunza osauka. Iye amakutcha uku ndi kuba. Mtundu uliwonse oyimirira molakwi pamalonda kumakhala kutanthauza kwa Baibulo ndi kwakuba.

Amati, Bwanji ife tasala kudyā, ndipo Inu simuona? Ndi bwanji ife tabvutitsa moyo wathu, ndipo Inu simusamalira? Taonani, tsiku la kusala kudyā kwanu inu mupeza kukondwerera kwanu, ndi kutsendereza anchito anu onse. Taonani, inu musala kudyā kuti mukangane ndi kutsutsana ndi kukantha ndi nk'honya yoipa; inu simusala kudyā tsiku lalero kuti mumveketse mau anu kumwamba. Kodi kusala kudyā koteroko ndiko ndinakusankha? Tsiku lakubvutitsa munthu moyo wace? Kodi ndikokuweramitsa mutu wace monga bango, ndi kuyala ciguduli ndi phulusa pansu pace? Kodi uyesa kumeneko kusala kudyā, ndi tsiku lobvomerezeka kwa Yehova? Kodi kumeneku si kusala kudyā kumene ndimakusankha: kumasula nsinga za zoipa, ndi

kumasula zomanga gori, ndi kuleka otsenderezedwa amuke mfulu, ndi kuti mutyole magori onse? Kodi si ndiko kupatsa cakudya cako kwa anjala, ndi kuti ubwere nao kunyumba kwako aumphawi otayika? Pakuona wamalisece kuti umbveke, ndi kuti usadzibisire wekha a cibale cako? (Yesaya 58:3-7)

Kungochita za chipembedzo chabe kumakhala kopanda phindu ngati tinalanyaza kuthandiza osowa. Yesu anati, “Koma tsoka inu, Afarisi! Cifukwa mupereka limodzi la magawo khumi la timbeu tonukhira, ndi timbeu tokometsa cakudya ndi ndiwo zonse, ndipo mumaleka ciweruziro ndi cikondi ca Mulungu” (Luka 11:42).

Watero Yehova wa makamu, kuti, Weruzani ciweruzo coona, nimucitire yense mnzace cifundo ndi ukoma mtima; musazunza mkazi wamasiye, kapena ana amasiye, mlendo kapena waumphawi; ndipo nanena mmodzi wa inu alingalire m’mtima mwace kumcitira coipa munthu mnzace. (Zekariya 7:9-10)

Mulungu savomemereza kupondereza kwa mtundu wuliwonse, kapena machenjerero aliwonse wodzipindulira yekha popondereza wina.

Abale anga, musakhale naco cikhulupiriro ca Ambuye wathu Yesu Kristu, Ambuye wa ulemerero, ndi kusamala maonekedwe. Pakuti akalowa m’sunagoge mwanu munthu wobvala mphete yagolidi, ndi cobvala cokometsetsa, ndipo akalowanso munthu wosauka ndi cobvala codetsa; ndipo mukapenyenera iye wobvala cokometsetsa, nimukati naye, Inu mukhale apa pabwino; ndipo mukati kwa wosaukayo, Iwe, ima uko, kapena, khala panso pa mpando wa mapazi anga; kodi simunasiyanitsa mwa inu nokha, ndi kukhala oweruza oganizira zoipa? Mverani, abale anga okondedwa; kodi Mulungu sanasankha osauka a dziko lapansi akhale olemera ndi cikhulupiriro, ndi olowa nyumba a ufumu

umene adaulonjeza kwa iwo akumkonda Iye? Koma inu mumanyoza munthu wosauka. Kodi sakusautsani inu acuma, nakukokerani iwowa ku mabwalo a mirandu? Kodi sacitira mwano iwowa dzina lokomali muitanidwa nalo? Koma ngati mucita cikwanirire lamulolo lacifumu, monga mwa malembo, Uzikonda mnzako monga udzikonda wekha, mucita bwino. (Yakobo 2:1-8)

Mulungu alibe sankho; tonse ndife ofanana pamaso pake: “Mulungu alibe sankho” (Macitidwe 10:34)

Mapembedzedwe oyera ndi osadetsa pamaso pa Mulungu ndi Atate ndiwo: kuceza ndi ana amasiye ndi akazi amasiye m’cisautso cao, ndi kudzisungira mwini wosacitidwa mawanga ndi dziko lapansi. (Yakobo 1:27)

Chipembedzo choyera si zachipembedzo, mwamwambo, chiphunzitso, malingaliro, kapena kutsatira ulaliki.

Pomwepo Mfumuyo idzanena kwa iwo a ku dzanja lace lamanja, Idzani kuno inu odalitsika a Atate wanga, lowani mu Ufumu wokonzedwera kwa inu pa cikhazikiro cace ca dziko lapansi: pakuti ndinali ndi njala, ndipo munandipatsa Ine kudya; ndinali ndi ludzu, ndipo munandimwetsa Ine; ndinali mlendo, ndipo munacereza Ine; wamarisece Ine, ndipo munandibveka; ndinadwala, ndipo munadza kuceza ndi Ine; ndinali m’nyumba yandende, ndipo munadza kwa Ine. Pomwepo olungama adzayankha Iye kuti, Ambuye, tinakuonani liti wanjala, ndi kukudyetsani? Kapena aludzu, ndi kukumwetsani? Ndipo tinaona Inu liti mlendo, ndi kukucerezani? Kapena wamalitsece, ndi kukubvekani? Ndipo tinakuonani Inu liti wodwala, kapena m’nyumba yandende, ndipo tinadza kwa Inu? Ndipo Mfumuyo idzayankha nidzati kwa iwo, Indetu ndinena kwa inu, Cifukwa munacitira ici mmodzi wa

abale anga, ngakhale ang'onong'ono awa, munandicitira
ici Ine. (Mateyu 25:34-40)

Kodi ndi ziyeneretso zotani zokhala m'bale kapena mlongo wa
Yesu ndi ziti? Pali chimodzi chokha: chiwalo cha mtundu wa anthu.
Ife tonse ndife abanja la Yesu.

Ndipo ndinena ndi inu, kuti ambiri a kum'mawa ndi a
kumadzulo adzafika, nadzakhala pamodzi ndi
Abrahamu, ndi Isake, ndi Yakobo, mu Ufumu wa
Kumwamba.

— Mateyu 8:11

Mulungu Ndi Wodzichepetsa

Ngakhale Mulungu ndiye wamphamvu kwambiri m'chilengedwe chonse; alinso, nthawi yomweyo, wodzichepetsa kwambiri.

Ndipo mngelo anati kwa iwo, Musaope; pakuti onani, ndikuuzani inu uthenga wabwino wa cikondwero cacikuru, cimene cidzakhala kwa anthu onse; pakuti wakubadwirani inu lero, m'mudzi wa Davide, Mpulumutsi, amene ali Kristu Ambuye. Ndipo ici ndi cizindikilo kwa inu: Mudzapeza mwana wakhanda wokuta ndi nsaru atagona modyera. (Luka 2:10-12)

Mulungu adasankha cholowera chodzichepetsa kwambiri mdziko lathu lapansi – ngati khanda lopanda vuto lililonse likugona modyera.

Idzani kuno kwa Ine nonsenu akulema ndi akuthodwa, ndipo Ine ndidzakupumulitsani inu. Senzani gori langa, ndipo phunzirani kwa Ine; cifukwa ndiri wofatsa ndi wodzichepetsa mtima: ndipo mudzapeza mpululo wa miyoyo yanu. Pakuti gori langa liri lofewa, ndi katundu wanga ali wo pepuka. (Mateyu 11:28-29)

Kodi zingatheke bwanji kuti Yesu, Mwana wa Mulungu, amveke bwino? Iye amati, “Ndine wofatsa ndi wodzichepetsa mtima.”

Ndipo Yesu ananena kwa iye, Ankhandwe ali nazo nkhwimba zao, ndi mbalame za m'mlengalenga zisa zao, koma Mwana wa munthu alibe potsamira mutu wace. (Mateyu 8:20)

Apa Yesu akudziwika ndi anthu osauka kwambiri: osowa pokhala.

Ndipo anambveka Iye cibakuwa, naluka korona waminga, nambveka pa Iye; ndipo anayamba kumlankhula Iye, kuti, Tikuoneni, Mfumu ya Ayuda! Ndipo anampanda Iye pamutu pace ndi bango, namthira malobvu, nampindira maondo, namlambira. Ndipo atatha kumnyoza anambvula cibakuwaco nambveka Iye zobvala zace. Ndipo anaturuka naye kuti akampacike Iye pamtanda. Ndipo anampacika Iye, nagawana zobvula zace mwa iwo okha, ndi kucita maere pa izo, kuti adziwe yense adzatenga ciani. Ndipo anapacika pamodzi ndi Iye acifwamba awiri; mmodzi ku dzanja lace lamanja ndi wina kulamazere. Ndipo lemba lidakwaniritsidwa, lomwe limati, Ndipo adawerengedwa pamodzi ndi olakwa. (Marko 15:17-20, 24, 27-28)

Kuyambira kubadwa kwake modzichepetsa mpaka kupachikidwa kwake pakati pa mbala ziwiri Yesu, Mwana wa Mulungu, nthawi zonse adawonetsa kufatsa ndi kudzachepetsa.

Iye anakuuza, munthuwe, comwe ciri cokoma; ndipo Yehova afunanji nawe koma kuti ucite colungama, ndi kukonda cifundo ndi kuyenda modzichepetsa ndi Mulungu wako? (Mika 6:8)

Kodi awiri adzayenda pamodzi asanapanganiranetu? (Amosi 3:3)

Ife tidzayenda mogwirizana ndi Mulungu tikakhala odzichepetsa monga Iye.

Pamene ife tamvetsetsa kudzichepetsa komwe Mulungu wathu wofatsa adawonetsa, ife tingalole bwanji kukhala ndi chikayiko pang'ono za kudalirika kwake?

Tonse tasocera ngati nkhusa; tonse tayenda yense m'njira ya mwini yekha; ndipo Yehova anaika pa lye mphulupulu ya ife tonse. lye anatsenderezedwa koma anadzicepetsa yekha osatsegula pakamwa pace; ngati nkhusa yotsogoleredwa kukaphedwa, ndi ngati mwana wa nkhusa amene ali du pamaso pa omsenga, motero sanatsegula pakamwa pace. Anacotsedwa ku cipsinjo ndi ciweruziro; ndipo ndani adzafotokoza nthawi ya moyo wace? Pakuti walikhidwa kunja kuno; cifukwa ca kulakwa kwa anthu anga lye anakhomedwa. Ndipo anaika manda ace pamodzi ndi oipa, ndi pamodzi ndi olemera mu imfa yace, ngakhale lye sanacita ciwawa, ndipo m'kamwa mwace munalibe cinyengo.

— Yesaya 53:6-9

Mulungu Ndi Wantchito, Osati Mbuye Wa Kapolo

Sindichanso inu akapolo; cifukwa kapolo sadziwa cimene mbuye wace acita; koma ndacha inu abwenzi; cifukwa zonse zimene ndazimva kwa Atate wanga ndakudziwitsani.

— Yesu (Yohane 15:15)

Mulungu safuna kuti tigonjere chikhulupiriro chathu mwakhungu. Iye amafuna ubwenzi wathu. Tikamayankhulana ndi mnzathu, sitigwiritsa ntchito zongopeka kapena zinsinsi. Mulungu amafuna ife kuti tizilankhulana naye moona mtima monga timayakhulirana ndi mnzathu wapamtima – ili ndiye tanthauzo lenileni la pemphero. Mulungu adatilenga ndi luntha la kulingalira, ndipo akutiiza tizichita izi, “Tiyeni, tsono, tiweruzane, ati Yehova” (Yesaya 1:18).

Koma Yesu anawaitana, nati, Mudziwa kuti mafumu a anthu amadziyesa okha ambuye ao, ndipo akuru ao amacita ufumu pa iwo. Sikudzakhala comweco kwa inu ai; koma amene ali yense akafuna kukhala wamkuru mwa inu, adzakhala mtumiki wanu; ndipo amene ali yense akufuna kukhala woyamba mwa inu, adzakhala kapolo wanu; monga Mwana wa munthu sanadza kutumikiridwa koma kutumikira, ndi kupereka moyo wace dipo la anthu ambiri. (Mateyu 20:25-28)

Yesu adawonetsa lamulo la moyo – adadziperereka yekha kuti atumikire ena.

Ndipo Yesu anayendayenda m’Galileya monse, analikuphunzitsa m’masunagoge mwao, nalalikira uthenga wabwino wa Ufumu, naciritsa nthenda zonse ndi kudwala konse mwa anthu. Ndipo mbiri yace

inabuka ku Suriya konse; ndipo anatengera kwa Iye onse akudwala, ogwidwa ndi nthenda ndi mazunzo a mitundu mitundu, ndi ogwidwa ndi mizimu yoipa, ndi akhunyu, ndi amanjenje; ndipo Iye anawaciritsa. Ndipo inamtsata mipingo mipingo ya anthu ocokera ku Galileya, ndi ku Dekapole ndi ku Yerusalemu, ndi ku Yudeya, ndi ku tsidya lija la Yordano. (Mateyu 4:23-25).

Ndipo anadza kwa Iye wodwala khate, nampempha Iye, namgwadira, ndi kunena ndi Iye, Ngati mufuna mukhoza kundikonza. Ndipo Yesu anagwidwa cifundo, natansa dzanja namkhudza iye, nanena naye, Ndifuna; khala wokonzedwa. Ndipo pomwepo khate linamcokera, ndipo anakonzedwa. (Marko 1:40-42).

Yesu anagwira ntchito osatopa ndiponso mwachifundo kuti athetse mavuto onse. Panalibe amene Iye anampitirira ndikumusamalira mwa chikondi: “Koma palinso zina zambiri zimene Yesu anazicita, zoti zikadalembedwa zonse phe, ndilingalira kuti dziko lapansi silikadakhala nao malo a mabuku amene akadalembedwa. Amen” (Yohane 21:25).

Yesu, podziwa kuti Atate adampatsa Iye zonse m’manja mwace, ndi kuti anacokera kwa Mulungu, namuka kwa Mulungu. Ananyamuka pamgonero, nabvala Malaya ace; ndipo m’mene adatenga copukutira, anadzimanga m’cuuno. Pomwepo anathira madzi m’msambidwe, nayamba kusambitsa mapazi a akuphunzira ace, ndi kuwapukuta ndi copukutira, cimene anadzimanga naco. (Yohane 13:3-5)

“Chochita cha Mulungu” chowululira ichi chinachitika pa Mgonero Womaliza wa Khristu kutatsala maola ochepa kuti Iye aweruzidwe ndi kupachikidwa. Uthenga wabwino wa Luka umafotokoza mwatsatanetsatane za ophunzira a Yesu pa nthawiyi: “Ndipo kunakhala kutsutsana mwa iwo, ndani wa iwo ayesedwe wamkuru” (Luka 22:24).

Izi ndi zomwe zinachitika: Yesu amadziwa kuti adachokera kwa Mulungu. Zinthu zonse zinali m’manja mwake. Mwa mawu ena, Yesu ankadziwa bwino lomwe kuti Iye ndi Mulungu, ndi mphamvu zonse za Mulungu. Ankadziwanso kuti ophunzira ake anali pakati pa mkangano wonena za amene adzakhala wamkulu mu ufumu wa Mulungu. Kodi Yesu anatani? Iye “adatenga chopukutira, nadzimanga m’chiuno mwake” ndikusambitsa mapazi a ophunzira ake omwe adaziyesa okha-ofunikira (ntchito ya kapolo wolembedwa pa nyumba pa chikhalidwe chimenecho).

Mukhale nao mtima m’kati mwanu umene unalinso mwa Kristu Yesu, ameneyo, pokhala nao maonekedwe a Mulungu, sanaciyesa colanda kukhala wofana ndi Mulungu, koma anadzikhuthula yekha, natenga maonekedwe a kapolo, nakhala m’mafanzidwe a anthu.

— Afilipi 2:5-7

Mulungu Amakukondani Mosasamala

Kodi mkazi angaiwale mwana wace wa pabere, kuti iye sangacitire cifundo mwana wombala iye? Inde awa angaiwale, koma Ine sindingaiwale iwe. Taona ndakulembera iwe pa zikhato za manja Anga.

— Yesaya 49:15-16

Ife titha kukhala ndi nthawi zina zomwe timamva kuti Mulungu watiwala ife, koma malingaliro sikuti nthawi zonse amakhala mulungo wa zenizeni. Mulungu akuti Iye sadzaiwala: “Kodi mpheta zisanu sizigulidwa timakobiri tiwiri? Ndipo palibe imodzi ya izo iiwalika pamaso pa Mulungu; komatu ngakhale matsitsi onse a pamutu panu awerengedwa. Musaopa, muposa mtengo wace wampheta zambiri” (Luka 12:6-7).

Pakuti ndakopeka mtima kuti ngakhale imfa, ngakhale moyo, ngakhale angelo, ngakhale maufumu, ngakhale zinthu ziripo, ngakhale zinthu zirinkudza, ngakhale zimphamvu, ngakhale utali, ngakhale kuya, ngakhale colengedwa cina ciri conse, sicingadzakhoze kutisiyanitsa ife ndi cikondi ca Mulungu, cimene ciri mwa Kristu Yesu Ambuye wathu. (Aroma 8:38-39)

Sizingatheke kufotokoza mwakuya chikondi cha Mulungu kwa ife. Khama lathu lonse lofotokozera za chikondi chake silimakwanira.

Taonani, cikondico Atate watipatsa, kuti tichedwe ana a Mulungu; ndipo tiri ife otere. Mwa ici dziko lapansi silizindikira ife, popeza silimzindikira Iye. (1 Yohane 3:1)

Chiyembekezo cha Mulungu kwa aliyense wa ife ndi kuti tidzamuzindikira ngati Atate wathu Wakumwamba. Kenako ife tidzazindikira cholowa chathu ngati ana amuna ndi akazi a Mulungu.

Yang'anirani kuti musanyoze mmodzi wa ang'ono awa; pakuti ndinena kwa inu, kuti angelo ao apenya cipenyere nkhope ya Atate wanga wa Kumwamba. Nanga muyesa bwanji? Ngati munthu ali nazo nkhosa makumi khumi, ndipo ikasokera imodzi ya izo, kodi saleka zija makumi asanu ndi anai mphambu zisanu ndi zinai, napita kumapiri, kukafuna yosokerayo? Ndimu akaipeza, indedi ndinena kwa inu, akondwera nayo koposa ndi makumi asanu ndi anai mphambu asanu ndi zinai zosasokera. Comweco siciri cifuniro ca Atate wanu wa Kumwamba kuti mmodzi wa ang'ono awa atayike. (Mateyu 18:10-14)

Munthu aliyense, kuchokera mfumu yodzikweza kwambiri pampando wachifumu mpaka wopemphapempha wosauka kwambiri pamsewu, ndiwofunika kwa Mulungu. Wofunika motani? Mulungu akadachoka kumwamba; akadavutika ndikufera m'modzi wa m'banja lake la munthu – ngati munthu m'modzi yekha ndi amene amafunikira kuyanjanitsidwa.

*Yehova anaonekera kwa ine kale, ndi kuti, Inde,
ndakukonda iwe ndi cikondi cosatha; cifukwa cace
ndakukoka iwe ndi kukukomera mtima.*

— Yereimiya 31:3

Ufumu wa Mulungu

Ufumu wa Mulungu sukudza ndi maonekedwe; ndipo sadzanena, Taonani uwu, kapena uwo! Pakuti, taonani, Ufumu wa Mulungu uli m’kati mwa inu.

— Yesu (Luka 17:20-21)

Maufumu ndi mabungwe adziko lapansi onse amawoneka, okhala ndi mpando wowonekera waboma kapena likulu. Ngati tikufuna chiwonetsero chowonekera cha ufumu wa Mulungu, sitidzachipeza. Ufumu wa Mulungu umangowonekera m’mitima mwathu monga kukonda Mulungu ndi wina ndi mnzake m’ malo mwa kudzikonda tokha.

Ndipo ananena, Tidzafanizirani Ufumu wa Mulungu? Kapena tidzaulinganiza ndi fanizo lotani? (Marko 4:30)

Ndizovuta bwanji kupeza mawu mchinenero cha anthu omwe amapereka chithunzi cholongosoka cha ufumu wa Mulungu kwa iwo omwe amangodziwa maufumu adziko lino!

Yesu anayankha nati kwa iye, Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona Ufumu wa Mulungu. (Yohane 3:3)

Ndi ntchito ya Mzimu Woyera kupangitsa zinthu za uzimu kumveka. Pamene ife tavomereza kutengeka mofatsa ndi Mzimu Woyera, zenizeni zauzimu zimabwera ndikuunika zomwe zimapangitsa kuti tione kapena kumvetsetsa za Ufumu wa Mulungu. Kusintha pakuwona kwatsopano kumene kumayanjanitsa ndikupatsa moyo, monga ngati “kubadwanso.”

Mzimu Woyera sikuti angogwira ntchito m’malire achipembedzo, monga momwe ife timaganizira nthawi zina. Iye amalankhula ndi aliyense mosatengera komwe akuchokera, kapena

komwe amakhala padziko lapansi, kapenanso malingaliro awo. Ngakhale okhulupirira kuti kulibe Mulungu sali otetezeka pantima ku ntchito ya Mzimu Woyera. Mulungu alibe tsankho lathu loyang'ana pafupi kapena samakukhumudwa pamene munthu sakhulupirira kuti Iye aliko.

Zinthu zauzimu zomwe Mzimu Woyera amazipanga zimveke bwino sizongodziwa m'mutu chabe, koma kusintha kwa mtima. Mwachitsanzo, osakhulupirira wachifundo wokoma mtima komanso wowolowa manja kapena okhulupirira kuti kulibe Mulungu ali omvera ku chikoka cha Mzimu Woyera ndipo amakhala pafupi ndi Ufumu wa Mulungu kuposa wachipembedzo wodziyeretsa yekha ndiponso wouma mtima. Kodi chingakhale chovuta kwambiri kwa Mulungu ndi chiyani – kusintha malingaliro a munthu za kukhalako kwa Mulungu kapena kusintha wamakani ndi wouma mtima?

Ndipo analinkudza nato kwa Iye tiana, kuti akatikhudze; ndipo ophunzirawo anawadzudzula. Koma pamene Yesu anaona anakwiya, ndipo anati kwa iwo, Lolani tiana tidze kwa Ine; mutsatiletse: pakuti Ufumu wa Mulungu uli wa totere. Ndithu ndinena ndi inu, munthu ali yense wosalandira Ufumu wa Mulungu ngati kamwana, sadzalowamo konse. (Marko 10:13-15)

Pankhani yophunzira zoonza zenizeni za Mulungu ndi Ufumu wake, chovuta kwambiri sikuphunzira koma kusaphunzira komwe kuyenera kuchitidwa. Ambiri a ife tayika chuma chochuluka kwambiri kukulitsa chithunzi chathu cha Mulungu. Ngati chithunzi chathu nchopotoka, kumakhala kovuta kwambiri kuchisiya. Popeza chithunzi chopotoka cha Mulungu chakhazikitsidwa mchipembedzo chofala kwa nthawi yayitali, chimakhala cholepheretsa chachikulu kumvetsetsa chowonadi chokhudza Mulungu ndi Ufumu wake. Ana amakhala ndi mwayi wochepera wodziwa chithunzi chopotokachi cha Mulungu, zomwe zimapangitsa kuti zikhale zotsavuta kuti avomereze zenizeni za Mulungu wathu wofatsa.

Nthawi yomweyo ophunzira anadza kwa Yesu, nanena, Ndani kodi ali wopambana mu Ufumu wa Kumwamba? Ndipo pamene Yesu anaitana kamwana, anakaimitsa pakati pao, nati, Indetu ndinena kwa inu, Ngati simutembenuka, nimukhala monga tianato, simudzalowa konse mu Ufumu wa Kumwamba. Cifukwa cace yense amene adzicepetsa yekha monga kamwana aka, yemweyo ali wopambana mu Ufumu wa Kumwamba. (Mateyu 18:1-4)

Ufumu wa Kumwamba ndi wosiyana ndi maufumu apadziko lapansi. Pali malo odzikuza, owongolera, okakamiza, kapena onyadira udindo. Ife tifunikira chidaliro chonga cha ana mwa Atate wathu Wakumwamba ndi kulolera kuphunzitsidwa.

Ufumu wa Kumwamba uli wofanana ndi Cuma cobisika m'munda; cimene munthu anacipeza, nacibisa; ndipo m'kucikonda kwace acoka, nagulitsa zonse ali nazo, nagula munda umenewu. Ndiponso Ufumu wa Kumwamba uli wofanana ndi munthu wa malonda, wakufuna ngale zabwino: ndipo m'mene anaipeza ngale imodzi ya mtengo wapatari, anapita, nagulitsa zonse anali nazo, naigula imeneyo. (Mateyu 13:44-46)

Pamene ife tamvetsetsa zowona za Mulungu – kuti Iye ali ndi chikondi chopanda malire choganizira ena ndiponso Iye ali wokhulupirika kwathunthu, wachifundo, ndi wowolowa manja – nthawi yomweyo tidzamvetsetsa bwino za ufumu wake m'mene ulili. Ife tidzawona chithunzi chathu chopotoka cha Mulungu ngati chopanda pake ndipo mosangalala tidzachigulitsa kuti tigule chithunzi chowona cha Mulungu ndi ufumu wake.

Ndipo anadza mmodzi wa alembi, namva iwo alikufunsana pamodzi, ndipo pakudziwa kuti anawayankha bwino, anamfunsa Iye, Lamulo la m'tsogolo la onse ndi liti? Yesu anayankha, kuti, La m'tsogolo ndi ili, Mvera, Israyeli; Ambuye Mulungu

wathu, Ambuye ndiye mmodzi; ndipo uzimkonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse, ndi mphamvu yako yonse. Laciwiri ndi ili, Uzikonda mnzako monga udzikonda mwini. Palibe lamulo lina lakuposa awa. Ndipo mlembiyo anati kwa Iye, Cabwino, Mphunzitsi, mwanena zoonza kuti ndiye mmodzi; ndipo palibe wina, koma Iye: ndipo, kumkonda Iye ndi mtima wonse, ndi nzeru yonse, ndi mphamvu yonse, ndi kukonda mnzace monga adzikonda mwini, ndiko kuposa nsembe zopsereza zamphumphu zonse, ndi nsembe zophedwa. Ndipo pakumuona kuti anayankha ndi nzeru, Yesu anati kwa iye, Suli kutali ndi Ufumu wa Mulungu. Ndipo palibe munthu analimbanso mtima kunfunsa Iye kanthu. (Marko 12:28-34)

Yesu adalimbikitsa mlembi yemwe anamuyankha kuti: “Iwe suli kutali ndi Ufumu wa Mulungu.” Mlembiyo adafotokoza momveka bwino za zenizeni za uzimu kuposa ambiri. Iye anapitirira kuwerenga kwa malemba kwa pamwamba ndi kumvetsetsa masomphenya a lamulo la chikondi chomwe Yesu adawonetsa.

Kodi dziko lapansi lokonzedwanso mwatsopano lidzakhala lotani pamene lamulo la chikondi lidzakhala lokhalo lamulo mdziko? Chikondi chokonda ena cha Mulungu chidzawonekera mwa anthu onse. Munthu aliyense adzakonda ndi kuwerengera munthu wina aliyense ngati “woposa iwo eni” (Afilipi 2:3). Kudzakhala mkhalidwe wa chimwemwe ndi chisungiko kopanda malire kuposa momwe ife tingaganizire.

Koma monga kulembedwa, Zimene diso silinazona, ndi khutu silinazimva, Nisizinalowa mu mtima wa munthu, Zimene ziri zonse Mulungu anakonzeratu iwo akumkonda lye.

— Akorinto 2:9

Mulungu Amatipatsa Ufulu Weniweni

Ndipo anati Mulungu, Tipange munthu m’cifanizo cathu, monga mwa cikhalidwe cathu: alamulire pa nsomba za m’nyanja, ndi pa mbalame za m’mlengalenga, ndi pa ng’ombe, ndi pa dziko lonse lapansi, ndi pa zokwawa zonse zakukwawa pa dziko lapansi.

— Genesis 1:26

Ulamuliro wa padziko lapansi womwe Mulungu adapatsa anthu sunavomereze kuzunza kapena kudyera masuku pamutu. Adamu ndi Hava ndi mbadwa zawo anayenera kukhala osamalira mwa chikondi dziko lapansi ndi cholengedwa chirichonse m’menemo. Lemba likunena kuti, “Dziko lapansi analipereka kwa ana a anthu” (Masalmo 115:16). Pamene makolo athu oyamba adakhulupirira bodza loti Mulungu ndi wodzikonda komanso wopondereza, adagonjetsedwa ndi wonyengayo ndipo malingaliro awo adakhala akapolo wake, “Pakuti iye amene munthu agonjedwa naye, ameneyonso adzakhala kapolo wace” (2 Petro 2:19). Kumene Adamu ndi Hava nthawi ina anali ndi ufulu iwo ndi ana awo tsopano anali mu ukapolo wa mdierekezi. Kwa nthawi yowopsa pambuyo pa kugwa, zinawoneka kuti anthu sangachitire mwina koma kuwonongedwa mopanda thandizo ku chiwonongeko chofananacho chomwe sichinapeweke monga Satana ndi angelo ena akugwawo.

Komabe pali uthenga wabwino; Mulungu adapereka njira yotuluka mu ukapolo kwa iwo ndi mbadwa zawo. Kuti athane ndi zadzidzidzi izi, Mulungu adalankhula ndi Satana mawu awa: “Ndipo ndidzaika udani pakati pa iwe ndi mkaziyo, ndi pakati pa mbeu yako ndi mbeu yace” (Genesis 3:15). Kodi udani umenewu nchiyani?

Satana ndi omutsatira adapandukira Mulungu kumwamba, iwo adachita izi kuchokera pa udindo wa nthawi yayitali ya ubale wawo ndi Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera. Iwo anali ndi zochitika

zokwanira zodziwira chikondi cha Mulungu ndipo analibe chifukwa chokayikira za ubwino wake. Pamene adadzipatura okha kwa Mulungu monga iwo adachitira, iwo adazipereka okha kusakwanitsa kuyankha Mzimu Woyera. Chifukwa cha kunyada kwawo kwamakani, iwo adadziwononga okha ku mdima ndipo pamapeto pawo anayiwalika osatha kulapa ndikubwerera kwa Mlengi wawo.

Pamene Adamu ndi Hava adachimwa, adachita izi kuchokera ku malo osadziwa zambiri za Mulungu komanso zokumana nazo zochepa za Iye. Iwo ananyengedwa ndi Satana; iwo sanapange chisankho chokana Mlengi wawo. Kutalikirana kwa anthu ndi Mulungu sikuti kunalibe thandizo. Lonjezo la Mulungu loti “adzaika udani” pakati pa Satana ndi mkaziyo linali uthenga wabwino woyamba wa padziko lapansi.

Mulungu mwachifundo adapereka chiyebekezo kwa Adamu ndi Hava komanso kwa mbadwa zawo kuti mitima ndi malingaliro awo athe kumvera Mzimu Woyera – iwo akadakhala osatetezeka ku chikondi cha Mulungu. Ukapolo wa anthu kwa Satana sukanakhala kwathunthu. Ufulu wakudzisankhira wa munthu aliyense ungakhalebe wopanda malire pakulepheretsa chikoka cha Satana pa ife ndikuwonetsetsa kuti tili ndi ufulu wosankha kuyanjananso ndi Mlengi wathu.

Ndi ciyebekezo kuti colengedwa comwe cidzamasulidwa ku ukapolo wa cibvundi, ndi kulowa ufulu wa ulemerero wa ana a Mulungu. (Aroma 8:21)

Kristu anatisandutsa mfulu, kuti tikhale mfulu; cifukwa cace cirimikani, musakodwenso ndi gori la ukapolo. (Agalatiya 5:1)

Cifukwa cace ngati Mwana adzakuyesani inu afulu, mudzakhala mfulu ndithu. (Yohane 8:36)

Mwa amene mulungu wa nthawi yino ya pansu pano unacititsa khungu maganizo ao a osakhulupirira, kuti

ciwalitsiro ca Uthenga Wabwino wa ulemerero wa Kristu, amene ali cithunzithunzi ca Mulungu, cisawalire. Pakuti Mulungu amene anati, Kuunika kudzawala kuturuka mumdima, ndiye amene anawala m'mitima yathu kutipatsa ciwalitsiro ca cidziwitso ca ulemerero wa Mulungu pankhope pa Yesu Kristu. (2 Akorinto 4:4, 6)

Kodi ino si nthawi yoti tichotse chophimba chachilamulo ndi zosagwirizana zomwe Satana wabisa Uthenga Wabwino wa Kristu ndi kusankha kusakhala nawo mu kusamvetsetsa kopambana za Mulungu wathu wofatsa?

Ngati mukhala inu m'mau anga, muli akuphunzira anga ndithu; ndipo mudzazindikira coonadi, ndipo coonadi cidzakumasulani.

— Yesu (Yohane 8:31-32)

Chowonadi ndi uthenga wabwino wokhudza Mulungu wathu wofatsa!

Atero Yehova, wanzeru asadzitamandire m'nzeru zace, wamphamvu asadzitamandire m'mphamvu yace, wacuma asadzitamandire m'cuma cace; koma wakudzitamandira adzitamandire adzikweze umo, kuti ali wakuzindikira, ndi kundidziwa Ine, kuti ndine Yehova wakucita zokoma mtima, ciweruziro, ndi cilungamo m'dziko lapansi, pakuti m'menemo ndikondwerera, ati Yehova.

— Yeremiya 9:23-24

Kuphatikizira

1. Kumvetsedwa molondola, Bible ndi lomveka. Baibulo limadzifotokozero ndi kudzitaunthauzira lokha. (Yesaya 1:18; 1 Akorinto 2:13)
2. Njira zathu ndi malingaliro athu siziwonetsera njira ndi malingaliro a Mulungu. (Yesaya 55:8-9; Masalmo 50:21)
3. Ulemerero wa Mulungu ndi khalidwe lake. (Ekiyosodo 34:6-7; 2 Akorinto 4:4, 6)
4. Mulungu ndiye chikondi. (1 Yohane 4:8, 16)
5. Chikondi cha Mulungu nchopanda dyera kwathunthu. (Yohane 3:16-17; Aroma 5:8)
6. Chikondi chimafuna ufulu. (Deuteronomo 30:19-20; Yohane 8:32, 36)
7. Yesu ndi Mulungu. (Yohane 1:1-3, 14; Akolose 1:13-17)
8. Yesu ndiye vumbulutso lomveka bwino la Mulungu. (Ahebri 1:3)
9. Mulungu sasintha. (Malaki 3:6; Ahebri 13:8; Yakobo 1:17)
10. Mulungu ndiye Mlengi ndi Wosamalira – osati wowononga. (Genesis 1:1; Masalmo 33:6, 9; Ahebri 1:3; Luka 9:56; Yohane 10:10)
11. Funso lomwe lili pa mkangano ndilokhudza mfundo za Mulungu zaulamuliro – sizokhudza mphamvu zake. (Genesis 3:1-5)
12. Ufumu wa Mulungu umalamulidwa ndi lamulo la chikondi – osati kulamalira ndi lamulo. (Mateyu 22:37-40; Agalatiya 5:14, 22-23; 1 Akorinto 13)
13. Mulungu sagwiritsa mphamvu. Amagonjetsa choyipa ndi chabwino. (Mateyu 5:43-48; Aroma 12:20-21; Luka 23:34)
14. Satana ndiye mdani wa Mulungu komanso ndi mbuye wachinyengo. (Yohane 8:44; 2 Akorinto 11:14; Cibvumbulutso 12:7-9; 1 Petro 5:8)
15. Tchimo ndikuwona Mulungu ngati wodzikonda komanso wosadalirika. (Genesis 3:1-5; Akolose 1:21)
16. Tchimo limapha – osati Mulungu. (Aroma 6:23; Yakobo 1:13-15)
17. Mulungu samatiweruza – timadziweruza tokha. (Yohane 3:17-21; 5:22; 12:44-48; Mateyu 7:1-5; Luka 6:37; Aroma 2:1-3)
18. Uthenga Wabwino ndi nkhani yabwino yonena za Mulungu. (2 Akorinto 4:3-6; Cibvumbulutso 14:6-7; Luka 15:11-32; Yohane 3:16-17; Aroma 5:8)
19. Chipulumutso ndi kuchiritisa chiyanjanitso – si nkhani yalamulo. (Marko 2:16-17; Luka 4:18-19; Macitidwe 28:27; 2 Akorinto 5:18)
20. Kudziwa Mulungu ndiye moyo wosatha. (Yohane 17:3)



Machitidwe a Mulungu Wathu Wofatsa akupereka umboni wotsimikizira kuchokera m'Baibulo woneneza Mulungu kuti Iye ndi wosasamala, woweluzza, wolamulira, wokondera, wokwiya, kapena wachiwawa. Bukuli likuwonetsa kuti Baibulo lonse, momveka bwino, limagwirizana ndi mawu womveka bwino akuti: "Mulungu ndiye chikondi" (1 Yohane 4:8).



Ulendo wa wolemba mwini ku chithunzi chowala cha Mulungu wathu wofatsa watenga zaka zopitirira makumi asanu. Iye amakhala ndi mkazi wake, Julie, m'nyumba yake yolimbikitsidwa ndi Walden kumpoto kwa Minnesota. Amakonda kucheza ndi abwenzi ake a miyendo inayi ndi a nthenga.